

***MFUNDO***

***ZA***

***KUSANTHULA ZINTHU ZOTIZUNGULIRA***

**HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	5

## MFUNDO ZA KUSANTHULA ZINTHU ZOTIZUNGULIRA

1. Zinthu Zotizungulira .....	6
2. Kusanthula Zinthu Zotizungulira.....	17
3. Maziko a Mbaibulo: Chipangano Chakale.....	27
4. Maziko a Mbaibulo: Chipangano Chatsopano.....	35
5. Kudzisanthula kwa Munthu.....	44
6. Kusanthula Gulu la Anthu.....	61
7. Kusanthula Dera.....	77
8. Kusanthula Mtundu.....	87
9. Kusanthula Chigawo.....	97
10. Kusanthula Bungwe la Chikhristu.....	107
11. Ndondomeko za Dongosolo.....	114
12. Mayankho a Mafunso.....	121

## **KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adziperezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

## **MAWU OYAMBA**

Phunziroli likutibweretsera Mfundo za Kawuniwuni wa Zinthu Zotizungulira limene ndi lofunika pa dongosolo ndi kayendetsedwe ka zipangizo za utumiki wa uzimu.

Phunziroli likukhazikika pa kufunika kwa kawuniwuni wa malo pa njira za kukonzekera kufikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. “Kawuniwuni wa malo watanthauzilidwa ndi Chipangano Chakale ndi Chatsopano chomwe. Malangizo aperekedwa pakuchita kawuniwuni wa munthu, magulu a anthu, madera osiyanasiyana, zigawo za dziko komanso mabungwe a Chikhristu.

Phunziroli ndi lachiwiri mu mndandanda wa maphunziro a mabuku atatu monga; “Buku la Dongosolo” la maphunziro operekedwa ndi Harvestime International Network. “Mfundo za Machitidwe a Mbaibulo” limabwera pa ili ndipo limatsatira ndi la “Dongosolo la Zolinga.”

Choncho ndi koyenera kuti maphunziro atatu amenewa aphunziridwe molingana ndi ndondomeko zawo kuti muwamvetse bwino pa za utsogoleri, malingaliro, ndi dongosolo zofukika pa utumiki wa mphamvu.

## **ZOLINGA ZA PHUNZIRO**

Pakutha pa phunziroli muyenera:

- Kupereka tanthauzo la mawu oti “kawuniwuni wa zinthu zotizungulira.”
- Kudziwa zolinga za kawuniwuni wa zinthu zotizungulira.
- Kudziwa zitsanzo za Chipangano chakale za kawuniwuni wa zinthu zotizungulira.
- Kudziwa zitsanzo za Chipangano Chatsopano za kawuniwuni wa zinthu zotizungulira.
- Kupanga kawuniwuni wa malo a munthu.
- Kusanthula za dera.
- Kusanthula za mtundu wa anthu.
- Kusanthula za chigawo cha dziko.
- Kulongosola dongosolo la “REAP” la Harvestime International Network.
- Kugwiritsa ntchito kawuniwuni wa zinthu zotizungulira popanga dongosolo la kayendetsedwe ka utumiki.

# CHAPUTALA CHA 1

## ZINTHU ZOTIZUNGULIRA

### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kepereka tanthauzo la mawu oti “zinthu zotizungulira.”
- Kulongosola zoyamba zomuzungulira munthu.
- Kulongosola zomwe zazungulira dziko.
- Kufotokoza zimene zinasintha zotizungulira zatsopano kuchokera ku zoyamba.
- Kudziwa njira zitatu za zotizungulira zimene zimakhudza moyo wa uzimu wa munthu.
- Kulemba chidule cha dongosolo la Mulungu lopulumutsa munthu ku uchimo.
- Kulongosola za mmene zinthu zotizungulira zimakhudzira utumwi wa Mpingo.

### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha (Genesis 6:5).**

### MAWU OYAMBA

Wokhulupirira aliyense amene ndi wobadwa mwatsopano anaitanidwa ndi Mulungu kuti akhale gawo la thupi la uzimu litchedwa Mpingo. Ntchito yaikulu imene inaperekedwa ku Mpingo ndi kulalikira Uthenga Wabwino kwa anthu a mitundu yonse.

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:**

**Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano (Mateyu 28:19-20).**

**Ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu,**

**Ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu (Luka 24:46-47).**

Ntchito yokwaniritsa kutumaku imakhudzidwa kwambiri ndi “zinthu zimene zatizungulira.” Choncho phunziroli likubweretsa mutu umenewu wa zinthu zomwe zatizungulira, tanthauzo lake, ndi mmene zotizungulirazi zimagwirizana ndi ntchito ya umishoni wa Mpingo.

## **ZINTHU ZOMWE ZATIZUNGULIRA**

Zinthu zomwe zatizungulira ndi monga zogwirika, anthu, zikhalidwe ndi zinthu za uzimu zimene zamuzungulira munthu. Zimakhudza magawo onse a dera limene munthu amakhalamo, kugwira ntchito ndi kutumikiramo.

**Zinthu zotizungulirazi** ndi monga zooneka zimene zimazungulira munthu. Kaya dziko, mzinda kapena mudzi umene munthu amakhala. Zimakhuzanso zinthu zimene zikhoza kuoneka ndi maso athu monga zomanga, nthaka, nyama, mitengo, mapiri ndi katundu ndi zina.

Komanso zinthu zoonekazi ndi monga chipululu chouma, madera ozizira a mapiri, nkhalango kapena chilumba. Akhoza kukhala malo abwino amene ali ndi nyengo yabwino ya zomera. Akhoza kukhala malo a ovuta a nyengo yosakhala bwino amene chakudya chimasowako. Malowa akhoza kukhala mzinda wa anthu ambiri kapene ochepa amene anthu ake amakhala kutali.

**Malo a nthu amene atizungulira** ndi anthu amene amakhala mmalo ena aliwonse. Malo a anthu amenewa ndi a anthu amene mumakhala nawo, kugwira nawo ntchito ndi kutumikira.

Munthu mudera lililonse amakhala chiwalo cha banja. Mabanjawa amakhala mmagulu a mitundu yawo. Mmagulu a anthu amenewa mulinso magulu ena monga osauka, olemera, ophunzira ndi osaphunzira. Dziko limakhala ndi anthu a magulu osiyana amene muwaphunzira patsogolo muphunziroli. Mmene anthu amakhala mmalo amatchedwa “makhalidwe a anthu.”

**Malo a zikhalidwe za anthu** awa ndi malo amene anthu amakhala ndi makhalidwe a moyo wawo molingana ndi mtundu wa anthu awo. Makhalidwewa ndi monga zilankhulo, machitidwe, miyambo, zinthu zawo ndi miyeso ya moyo.

Chikhalidwe chimakhudzanso zinthu monga nyimbo, luso, zasayansi, zolemba, ndondomeko ya maphunziro ndi za ndale. Chikhalidwe chimakula chifukwa cha nkhanzi za chipembedzo ndi za ndale ndi pobwerezedwa kwa makhalidwe ena kwa nthawi yaitali.

Chikhalidwe chimasiyana potengera mtundu ndi magulu a anthu mdziko. Mwachitsanzo, mu nthawi ya Mbaibulo chikhalidwe cha Ayuda chimasiyana ndi cha Amitundu. Ayuda samadya nyama zina ndipo amachita mdulidwe. Pamene amitundu amadya nyama zonse ndipo sachita mdulidwe. Magulu awiriwa akusiyana mu chipembedzo, miyambo ndi makhalidwe awo a mmudzi.

Zotizungulira za uzimu ndi zinthu zimene zimakhudza uzimu wa munthu. Mulungu ali utatu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana Yesu Khristu ndi Mulungu Mzimu. Munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu ngati wamagawo atatu. Munthu sli ndi thupi, moyo ndi mzimu.

Malo a zochitika za uzimu ndi amene amakhudza moyo ndi mzimu wa munthu. Pali mphamvu za zoipa za uzimu za Satana. Palinso mphamvu zabwino za Mulungu. Mphamvu za uzimu zimenezi zimalimbana ndi moyo ndi mzimu wa munthu.

(Harvestime International Institute limapereka phunziro limene mutu wake ndi *“Ndongomeko za Uzimu: Buku la Nkhondo za Uzimu”* limene limakhudza mutu wa malo a zochitika za uzimu mwatsatanetsatane).

Pofuna kumvetsa zinthu zooneka, anthu, zikhalidwe, ndi malo a uzimu a munthu, tikuyenera kuonanso zimene Mulungu analemba mmawu ake, Baibulo. Tikuyenera kubwerera ku mbiri imene nthawi isanayambe, monga tikudziwa inayamba pano padziko.

### **CHIYAMBI CHA ZINTHU ZONSE**

Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu alipo. Alibe chiyambi ndi mathero. Ndipo amakhala Kumwamba. Analenga malo ake ndiko Kumwamba. Ndipo analenganso malo a munthu amene ndi dziko lapansi. Chilichonse chopezeka chinalengedwa ndi Mulungu.

**Pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye.**

**Ndipo iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa iye (Akolose 1:16-17).**

Chilichonse chimene Mulungu analemba kuchokera pachiyambi chinali chabwino:

**Ndipo anazona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu (Genesis 1:31).**

### **CHIYAMBI CHA CHOIPA**

Mwa zolengedwa zamoyo zonse zimene Mulungu anazilenga panalinso angelo. Panli mngelo amene analengedwa mwapaderadera ndi Mulungu ameneyi amatchedwa Lusifala. Baibulo limatiuza kuti Lusifala pachiyambi anali wangwiro, okongola, ndipo anali ndi udindo waukulu Kumwamba.



Keneko Lusifala anayamba kunyada pa kukongola ndi udindo wake. Amamemeza ena mwa angelo mkuyamba kuukira Mulungu. Mu kudzikweza kwake, Lusifala amafuna kukhala wamkulu kuposa Mulungu. Anayesera kuchotsa Ufumu wa Mulungu Kumwamba.

Chifukwa cha uchimo, Lusifala ndi angelo amene amaukira nawo anachotsedwa kumwamba kupita ku dziko lapansi. Lusifala anayamba kudziwika ngati Satana kapena Mdierekezi. Angelo ake anayamba kudziwika ngati ziwanda. Mukhoza kuwerenga mbiri ya izi mbuku la Yesaya 14:12-15 ndi Ezekieli 28:14-16. Satana ndiye mphamvu ya uzimu ya machimo onse, zosalungama zonse ndi choipa chonse cha mdziko lapansi.

## **MALO OYAMBA**

Pamene Mulungu analenga dziko lathuli, linali dziko langwiro. Mulungu anaona ntchito yonse ya manja ake ndipo anati, “kunali bwino” (Genesis 1). Pamene Mulungu analenga munthu mchifanizo chake, munthunso anali wangwiro. Anali opanga tchimo ndi wachiyanjano chabwino ndi Mulungu (Genesis 1:26 ndi chaputala cha 2).

Pamene Mulungu analenga mkazi, anawauza banjali kuti achulukane ndi kubereka ana. Adamu ndi Hava amayenera kulidzadza dziko ndi ena opanda uchimo, anthu a umulungu ngati iwo eni (Genesis 2:18-25; 1:28).

Malo oyamba amene Adamu ndi Hava amakhala kunali mmunda wa Edeni. Mundawu unali wabwino ndi wodzadza ndi chilengedwe chodabwitsa cha Mulungu:

**Ndipo Yehova Mulungu anabzala m'munda ku Edene cakum'mawa; momwemo ndipo adaika munthu adamuumbayo.**

**Ndipo Yehova Mulungu anameretsa m'nthaka mitengo yonse yokoma m'maso ndi yabwino kudya; ndiponso mtengo wa moyo pakati pa mundapo, ndi mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa.**

**Ndipo unaturuka m'Edene mtsinje wakuthirira m'mundamo (Genesis 2:8-18).**

Mulungu analenga malo angwiro. Koma kumbukirani kuti, Satana anali atachotsedwa Kumwamba mkupita kudziko. Satana anabweretsa kusintha kowawa mu dziko langwiro la munthu limene Mulungu anampatsa.

## **TCHIMO LIPEZEKA PA MALO**

Atalengedwa mchifanizo cha Mulungu, munthu anali ndi maganizo a nzeru amene akanamapanga ziganizo. Munthu akanamasankha kumvera ndi kusamvera Mulungu. Kumbukirani kuti Satana ndiye mwini choipa. Chifukwa cha kupezeka kwa choipa, munthu anali ndi ufulu wosankha chabwino ndo choipa, munthu anasankha choipa. Kusamvera koyamba kwa

munthu kumatchedwa “kugwa kwa munthu,” kutanthauza kuti munthu anagwa pa chilungamo ku uchimo. Mukhoza kuwerenga nkhani yonseyi mu Genesis chaputala cha 2 mpaka 3.

Mmunda wa Edeni, munali mitengo yambiri imene Adamu ndi Hava akanamadya. Koma panali mtengo umodzi umene anauzidwa kuti asadye:

**Ndipo Yehova Mulungu anamuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m'munda udyeko;**

**Koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu (Genesis 2:16-17)**

Munthu anali ndi mphamvu yotha kusankha kumvera ndi kusamvera Mulungu. Satana anatsogolera Adamu ndi Hava kusamvera Mulungu. Chifukwa cha kusamvera kwawo, uchimo unalowa pakati pawo.

### **MALO ASINTHA**

Tchimo linabweretsa kusintha kowawa kwa munthu ndi malo omuzungulira. Mulungu anawachenjeza kuti mphoto ya uchimo inali imfa. Imeneyi inali imfa ya kuthupi ndi ku uzimu. Imfa ya kuthupi kunali kutayika kwa chiyanjano chawo ndi Mulungu. Imfa ya kuthupi inali kufa kwa matupi awo.

Chifukwa choti Adamu ndi Hava anachimwa, tchimo ndi imfa inafikira kwa anthu onse:

**Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anachimwa (Aroma 5:12)**

Chifukwa cha kugwa kwa Adamu ndi Hava, tchimo linafikira anthu onse. Kuthanthauza kuti aliyense wobadwa amakhala ndi tchimo. Monganso makhalidwe a kuthupi amapatsirana, makhalidwe a chibadwidwe cha uchimonso amapatsirana.

Munthu aiyense amachimwa payekha pamene akokedwa ndi chilakolako cha thupi poukira Mulungu.

**Koma munthu ali yense ayosedwa pamene cilakolako cace ca iye mwini cimkokera, nicimnyenga.**

**Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa (Yakobo 1:14-15)**

Chifukwa cha chikhalidwe cha uchimo ndi machitidwe a uchimo a munthu, anthu onse amalawa nawo imfa ya kuthupi ndi ku uzimu:

**Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu (Aroma 3:23)**

Malo amene munthu amakhala anatembereredwanso. Mulungu ananena kuti dziko lidzakubalira minga ndi mitulo. Ntchito yolemetsa (yathukuta) ndi chizindikiro wake wa munthu ndi malo amene akhalamo:

**Kwa Adamu ndipo anati, Cifukwa kuti wamvera mau a mkazi wako, nudya za mtengo umene ndinakuuza iwe kuti, Usadyeko; nthaka ikhale yotembereredwa cifukwa ca iwe; m'kusauka udzadyako masiku onse a moyo wako:**

**minga ndi mitula idzakubalira iwe; ndipo udzadya therere la m'thengo:**

**m'thukuta la nkhope yako udzadya cakudya, kufikira kuti udzabwerera kunthaka: cifukwa kuti m'menemo unatengedwa: cifukwa kuti ndiwe pfumbi, ndi kupfumbiko udzabwerera (Genesis 3:17-19)**

Dziko lomwe lija linaipitsidwa ndi machimo a munthu:

**Kwezera maso ako ku mapiri oti se, nuone: sanagona ndi iwe kuti? Panjira wakhalira iwo, monga M-arabu m'cipululu; ndipo waipitsa dziko ndi zigololo zako, ndi zoipa zako.**

**Ndipo mvula yakanidwa, ndipo panalibe mvula ya masika; ndipo unali ndi nkhope ya mkazi wadama, unakana manyazi (Yeremiya 3:2-3)**

Sipanapite nthawi yaitali kufikira Mulungu analiyang'ana dziko lapansi limene analilenga:

**Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha (Genesis 6:5)**

Ichi ndi chidule cha mmene malo omuzungulira munthu anasinthira chifukwa cha tchimo:

- 1. Munthu anasinthira ku uzimu:** Sanalinso pa ubale ndi Mulungu. “Imfa yak u uzimu” imatanthauza kuti kusiyantsidwa ndi Mulungu kwamuyaya chifukwa cha uchimo. Aliyense wa ku mibadwo ya kutsogolo anatenga chikhalidwe cha uchimochi ndipo onse anachimwa.
- 2. Munthu anasinthira kuthupi:** Thupi lake linayamba kukalamba, ngakhale kufa ndipo amabwerera ku dothi kumene anachokera pomulenga Mulungu.
- 3. Dziko nalonso linatembereredwa:** “Minga ndi mitulo” zimaimira themberero limene linakhudza zinthu zonse zozungulira. Munthu amakumana ndi zowawa payekha ndi uchimo wa zinthu zimene zamuzungulira mmalo amene amakhala.

## MMENE ZINTHU ZILILI NTHAWI INO

Mdziko limene munthu akukhala pakali pano likadali loipa. Kufikira Mulungu ataononga dziko lochimwa ndi kulenganso dziko latsopano la Kumwamba ndi pansu, pakuti chilengedwe chose chibuula kufuna maomboledwe awo chifukwa cha uchimo:

**Pakuti tidziwa kuti colengedwa conse cibuuula, ndi kugwidwa m'zowawa pamodzi kufikira tsopano (Aroma 8:22)**

## MMENE MUNTHU AKUKHUDZIDWIRA

Uchimo umene ulili mu dzikoli umakhudza uzimu wa munthu chifukwa cha adani atatu amene amagwira ntchito: Dziko, thupi ndi Mdierekezi:

1. **Dziko:** Satana amagwira ntchito kudzera mu zochitika za dziko, zimene ndi za uchimo, kukhazikika pa za chuma ndi nzeru zimene si za umulungu.
2. **Thupi:** Anthu onse anabadwa ochimwa. Satana amgwira ntchito kudzera mu chikhalidwe cha uchimo cha anthu powatsogolera ku machitachita a uchimo. Makhalidwe a uchimowa molingana ndi Baibulo amabweretsa zowawa, machitidwe a uchimo osalungama.
3. **Mdierekezi:** Satana akadali pa nchito mdzikoli yofuna kukwaniritsa zolinga zake. Amagwira ntchito kudzera mu ziwanda komanso mwa anthu amene amagonjera ku zofuna zake.

## NJIRA YOPULUMUKIRA

Mulungu anapereka njira yopulumuka ku makhalidwe a uchimo. Munthu atha kupulumutsidwa ku zowawa zodza Kamba ka imfa ya uzimu (kusiyanitsidwa ndi Mulungu).

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha (Yohane 3:16)**

Kudzera mwa Yesu, munthu athanso kupulumutsidwa ku zotsaira za muyaya za imfa ya uzimu. Okhulupirira onse owona mtima amene anafa kuthupi adzaukitsidwa tsiku lina kuchoka ku imfa ya kuthupi kupita kumoyo wosatha:

**Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka;**

**Pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse (I Atesalonika 4:16-17)**

Dziko lochimwa limene tikukhalali lidzaonongedwa tsiku lina, ndipo Mulungu adzalenga Kumwamba ndi dziko zatsopano:

**Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyamba idzapita ndi cibumo cacikuru, ndi zam'mwamba zidzakanganuka ndi kurenta kwakukuru, ndipo dziko ndi nchito ziri momwemo zidzarenthedwa**

**Koma monga mwa lonjezano lace tiyembekezera miyamba yatsopano, ndi ziko latsopano m'menemo mukhalitsa cilungamo (II Petro 3:10,13)**

Ngakhale dziko likadali pansu pa themberero la uchimo, okhulupirira akhoza kumasulidwa ku themberero ndi kuyamba kukhala ndi moyo wochuluka mwa Khristu. Yesu anati:

**...Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka (Yohane 10:10)**

Makhalidwe anu a uchimo akhoza kusinthika ndi mphamvu ya Mulungu pobala chipatso cha cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupirtro (Agalatiya 5:22-23). Ngakhale mukadalibe mdziko, simuli nawo gawo limodzi la zoipa zake.

**Sindipempha kuti muwacotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo.**

**Siali adziko lapansi monga Ine sindiri wa dziko lapansi (Yohane 17:15-16)**

Tili mdziko ndi cholinga chofalitsa uthenga wabwino ku dziko loipali:

**Monga momwe munandituma Ine ku dziko lapansi, Inenso ndinatuma iwo ku dziko lapansi (Yohane 17:18)**

Tikhoza kukondwera chifukwa Yesu...

**...Amene anadzipereka yekha cifukwa ca macimo athu, kuti akatilanditse ife m'nyengo ya pansu pano yino yoipa, monga mwa cifuniro ca Mulungu ndi Atate wathu (Agalatiya 1:4)**

### **MALO AMENE TILI NDI UMISHONI WA MPINGO**

Malo amene tili ndi ofunika kwambiri pa nkhani ya umishoni wa Mpingo wofikira anthu amitundu yonse ndi uthenga wabwino:

**Koyamba:** Mautumiki onse amachitika mmalo osiyanasiyana a dziko amene mwaphunzira kuti ndi oyipa. Mukamvetsa izi simuzadabwa pamene mdani akulimbana nanu pochita utumiki.

**Kachiwiri:** Pali malo osiyanasiyana mdzikoli amene ndi osiyana ndi ena. Monganso anthu onse amakhudzidwa ndi zoipa za malo amene akukhala, amakhudzidwanso ndi zinthu zina kumene akukhala. Mukamvetsa zinthu zimene zili kumalo amene muli, mukhoza kutumikira bwino uthenga wabwino.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “zinthu zotizungulira.”

---

3. Longosolani malo oyamba a munthu.

---

4. Longosolani mmene zinthu zilili pano mdziko.

---

5. Kodi ndi chiyani chimene chinabweretsa kusintha kwa mmene zinthu zinalili poyamba mkukhala mmene zilili pano?

---

---

---

6. Lembani njira zitatu zimene zikuonetsera mmene uzimu wa munthu ulili panopo.

---

---

---

7. Kodi dongosolo la Mulungu lopulumutsa munthu ku uchimo ndi lotani?

---

8. Kodi zinthu zomwe zatizungulira zimakhudza bwanji umishoni wa mpingo?

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani Genesis chaputala cha 3 ndi kuona mmene Satana anagwiritsira ntchito zinthu zimene zinalipo mu yesero loyamba. Munda udalengedwa ndi Mulungu wangwiro. Koma panali mtengo umodzi woletsedwa. Munthu anapatsidwa ufulu: Kumvera Mulungu ndi kusadya zipatso za mtengowo ndi kupitilira kukhala mmunda kapena kusamvera Mulungu ndi kulola tchimo kupezeka pakati pawo. Mu Genesis 3, Hava anali pamalo oyandikana ndi mtengo woletsedwa. Baibulo limachenjeza za choipa...

### **Pewapo, osapitamo; Patukapo, nupitirire. (Miyambo 4:15)**

**Hava anamva:** Mawu a Satana kuchokera ku mtengo woletsedwa.

**Anaona:** Chinachake chokopa ku mtengowo. Unali mtengo woletsedwa.

**Anatenga:** Chinthu cha uchimo ku mundawo.

**Anadya:** Chipatso choletsedwa. Koma asanadye choipacho chinali cha kunja. Sizinamukhudze ku uzimu wake, koma atangodya, anakhala ochimwa.

**Anampatsa:** Hava amakhala limodzi ndi Adamu chifukwa anali mkazi wake. Anamukopa Adamu ku uchimo pomupatsa chipatso choletsedwa. Anthu nthawi zambiri amakopedwa ku uchimo chifukwa cha anzawo amene amakhala nawo.

**Adamu anadya:** Nayenso anatenga mkudya chipatso choletsedwa. Kuzungulira kwa tchimo kunayamba ndipo kumapitilira mu mbiri kwa nthawi yaitali. Anthu onse anakhala ochimwa ndipo malo awo anakhalanso ochimwa.

2. Longosolani nyengo imene anasankha Loti mu Genesis 13:8-11.
3. Ndi uzimu wamtundu wanji umene unali mu mzinda wa Sodomo umene Loti anasankha? Onani Genesis 13:13 ndi machaputala 18-19.
4. Fananitsani nyengo ya uzimu umene ukupezeka mu Genesis 6:5 ndi umene uli mu Chibvumbulutso 21:10-27.



## CHAPUTALA CHA 2

### KUSANTHULA ZINTHU ZOTIZUNGULIRA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la “kusanthula zotizungulira.”
- Kudziwa mitundu isanu ndi umodzi wa zinthu zotizungulira mu phunziroli.
- Kulemba zifukwa zisanu ndi ziwiri za kufunika kwa kusanthula zinthu zotizungulira pofalitsa uthenga wabwino kwa amitundu.
- Kulemba chidule cha zovuta zisanu ndi chimodzi posanthula zinthu zotizungulira.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu (I Yohane 5:3)**

#### MAWU OYAMBA

Chaputala ichi chikutibweretsa za “kusanthula zinthu zomwe zatizungulira” limene ndi luso lobweretsa kumvetsetsa kwa zinthu zotizungulira zimene anthu amakhalamo ndi mmene zimakhudzira pofalitsa uthenga wabwino. Motero “kusanthula zinthu zimene zatizungulira” ndi mtundu wa kusanthula umene ukudziwika. Zotsatira posanthula komanso kufunika kosanthula zalongosoledwanso.

#### KUSIYANA KWA ZINTHU ZOMWE ZATIZUNGULIRA

Mu chaputala chathachi mwaphunzira kuti zinthu zimene zatizungulira ndi monga zogwirika, anthu, zikhalidwe ndi zokhudza uzimu wa munthu. Mwaphunziranso kuti dzikoli ndi lochimwa ndipo anthu amene amakhalamo ndi ochimwa amene akuyenera mpulumutsi.

Mautumiki onse amachitika mdzikoli. Koma pali zinthu zosiyanasiyana mdziko lochimwali ndipo zinthuzonso zimasiyana. Mwachitsanzo, zinthu zopezeka ku mtundu waung’ono wa ku chipululu cha Sahala ndi chosiyana ndi cha anthu a ku Ulaya.

Monganso mmene anthu amakhudzidwira ndi zinthu zimene zawazungulira, komanso amakhudzidwa ndi zinthu za kumene iwo akukhala. Pamene mwamvetsa za zinthu zawo, mukhoza kutumikira bwino uthenga wabwino.

#### KUSANTHULA ZINTHU ZIMENE ZATIZUNGULIRA

“Kusanthula zinthu zotizungulira” kuzakuthandizani kumvetsa malo a zinthu zina. Kusanthula chinthu kumatanthauza kuchiphunzira mwachindunji, kuchizukuta magawo onse amene amapanga chinthucho. Kusanthula zinthu zotizungulira zimatanthauza kuti kuphunzira gawo lililonse la chinthu monga maonekedwe ake, anthu ake, chikhalidwe, ndi zochitika za uzimu. Musanthula zinthu zokuzungulirani zenizeni mwatsatanetsatane.

## **MITUNDU YA KUSANTHULA ZINTHU YA ZOTIZUNGULIRA**

Pali mitundu isanu ndi umodzi ya kusanthula zinthu zotizungulira imene ikupezeka mu phunziroli, imene ndi yofunika potumikira uthenga wabwino ku dziko lapansi. Chilichonse chifotokozeredwa pachokha:

**KUSANTHULA MUNTHU:** Uku kumakhala kusanthula zinthu zimene zakuzungulira komanso iwe mwini ngati wokhulupirira.

**KUSANTHULA ANTHU APAGULU:** Dziko lili ndi magulu a anthu osiyanasiyana. Anthuwa amalankhula zilankhulo zosiyana, ali ndi makhalidwe osiyana, ndipo amakhala ndi ndondomeko zawo. Malo aliwonse, mtundu, ndi zigawo za dziko lili ndi anthu amagulu osiyanasiyana.

**KUSANTHULA DERA:** Dera ndi malo apaderadera opezeka mkati mwa mtundu wa anthu. Akhoza kukhala dziko, mzinda, mudzi, chigawo, kapena malire.

**KUSANTHULA MTUNDU:** Mtundu ndi dziko komanso anthu amene alumikizana pamodzi mwa utsogoleri ndi boma limodzi.

**KUSANTHULA CHIGAWO:** Chigawo cha dziko chimakhala cha anthu a madera ambiri a dziko. Monga Malawi ali ndi zigawo zitatu mmene muli maboma ambiri.

**KUSANTHULA MABUNGWE A CHIKHRISTU OMWE ALIPO:** Iyi ndi mipingo, magulu a chipembedzo ndi mabungwe amene anakhazikitsidwa ndi cholinga chofuna kuchita utumiki wa Chikhristu.

## **KUFUNIKA KWA KUSANTHULA ZINTHU ZIMENE ZATIZUNGULIRA**

Kumvetsetsa zinthu zimene zatizungulira ndi kofunika pa kufalitsa uthenga wabwino chifukwa:

### **ZIMATHANDIZA OKHULUPIRIRA KUDZIWA MALO AWO MU UTUMIKI:**

Mu phunziro la “Kusanthula zinthu zimene zamuzungulira munthu,” mudzadziwa mphamvu zanu za uzimu, kufooka kwanu, maitanidwe ndi mphatso. Kusanthula uku ndi kofunikira chifukwa kumakuthandizani kudziwa malo anu mu utumiki. Zimadziwitsa zofooka zanu mu uzimu zimene mumatha kuzikonza ndi cholinga chakuti mukhala amphamvu mu uzimu zimene mungathe kutumikira nazo Mulungu.

### **ZIMAKHUDZA MUNTHU ALIYENSE:**

Pofalitsa uthenga wabwino, ndi zofunika kumvetsetsa kuti palibe amene amasemphana ndi zoipa za dziko. Anthu onse a zikhalidwe ndi mitundu yonse ndi ochimwa ndipo afunika mpulumutsi. Pali ziopa zimene zimapezeka ku zikhalidwe za anthu ndipo chikhalidwe cha uchimo chilipo kwa osakhulupirira. Satana amagwirabe ntchito ku malo onse amene mumatumikirako. Muzapitilira kulimbana ndi dziko, thupi komanso Mdierekezi.

### **ZIMAGWIRIZANA NDI UTHENGA WABWINO KU MALOKO:**

Kuthekera kwa anthu komvetsa uthenga wabwino kumakhudzidwa ndi nyengo zawo. Mwachitsanzo, mumayenera kufalitsa Mau a Mulungu mu zilankhulo zimene anthu amazimva.

Mukuyenera kufalitsa uthenga wabwino mu makhalidwe ndi ndondomeko zovomerezeka. Ku magulu ena a anthu, ndi zofunika kupempha chilolezo kwa atsogoleri musanayambe kufalitsa uthenga mu zilakhulo zanu. Njira imene mumagwiritsa ntchito kuperekerana uthenga kumakhuzidwa ndi mtundu wa anthu ndi maphunziro awo. Choncho mumayenera kusintha uthenga wanu moyenera.

Mumayenera kusinthano makhalidwe anu a moyo kuti agwirizane ndi chikhalidwe cha anthu. Mwachitsanzo mtumwi Paulo amadya nyama, koma kwa anthu a zikhalidwe zina samadya. Amazisintha yekha pa makhalidwe ake molingana ndi mtundu wa anthu pofalitsa uthenga wabwino.

**Cifukwa cace, ngati cakudya cikhumudwitsa mbale wanga, sindidzadya ayama ku nthawi yonse, kuti ndiogakhumudwitse mbale wanga (I Akorinto 8:13)**

Choncho SIMUKUYENERA kusintha makhalidwe anu posemphana ndi Mau a Mulungu, koma pamene pali kusintha kwa makhalidwe anu mukhoza kutero pofuna kufalitsa uthenga wabwino.

Kumadera ambiri mukhoza kugwiritsa ntchito chikhalidwe popititsa uthenga wabwino patsogolo. Koma pochita zimenezi, muyenera kumvetsa bwino chikhalidwe cha anthuwo. Chikhalidwe chikhoza kugwira ntchito ngati cholulumikizira mu ufumu wa Mulungu kapene chotchinga cholepheretsa anthu.

### **ZIMAPANGITSA KUGWIRITSA NTCHITO ZINTHUZO KUPHUNZITSA UTHENGA:**

Yesu anagwiritsa ntchito zinthu zomwe zinamuzungulira pofuna kuphunzitsa uthenga wabwino. Amakamba nkhani zogwirizana ndi chikhalidwe cha anthu pogwiritsa ntchito tirigu, nsomba, maluwa, nyali ndi zomangamanga pophunzitsa maphunziro a uzimu.

Yesu sanawapititse ophunzira ake ku zinthu zonama. Komanso sanawasekere mmalo obisika. Anaphunzitsa anthu bwino za mmene angakhalire, angagwirire ntchito ndi kutumikira.

Amatengera uthenga wabwino ku nyengo zawo. Zinthu zowazungulira zinali malo ophunzirirapo amene amaphunzitsa moyo wawo.

### **KUDZIWA MALO OYENERA A ZAUZIMU:**

Mu dziko lathuli, alimi amadziwiratu nthaka asanadzale mbewu zawo. Amachita izi pa zifukwa zitatu izi:

**Koyamba**, amafuna asankhe nthaka yabwino yoyenera mbewu zawo. Amadziwa kuti nthaka yabwino ndi yokhayo imene ingabweretse zokolola zochuluka.

**Kachiwiri**, amadziwanso nthaka yosakhala bwino ndi mmene angaikonzekere pa ulimi. Akakhala anthu ena, nthakayo amaithira fetereza ndi cholinga choikonza. Ena amadula mitengo, mkuiotcha mu dothi ndi kugwiritsa ntchito phulusa kupanga fetereza.

**Kachitatu**, amalisanthula dothi ndi kupeza mtundu wa mbewu umene zingachite bwino pa ulimi. Mwachtsanzo, kodi amagwiritsa ntchito mthirira kapena mvula imabwera yambiri? Nanga amadzala chiyani? Amakolola bwanji?

Kusanthula zinthu za uzimu ndi chimodzimodzi mmene alimi amachitira. Timasanthula anthu, madera, mitundu ndi zigawo za anthu pa zifukwa zofanana:

**Koyamba**, timafuna kudziwa malo abwino ochitapo za uzimu. Madera ena amakonzekera zokolola za uzimu. Baibulo limati ogwira ntchito ndi ochepa pa zokolola za Mulungu. Pakuti mphamvu ya zokolola za uzimu ndi ya malire, timayenera tike chidwi pa pa malo amene ndi okonzekera zokolola za uzimu.

**Kachiwiri**, timafuna tidziwe njira zimene tingagwiritse ntchito ku madera amene sanakonzekere ndi zokolola za uzimu. Anthu ena, madera, mitundu ndi zigawo sakhala ndi chidwi ndi uthenga wabwino. Timayenera tidziwe chifukwa ndi njira zimene tingagwiritse ntchito kusintha malowa.

**Kachitatu**, timadziwa njira zabwino zoti tigwiritse ntchito ndipo izi zimatitengera ku chifukwa china chachikulu cha kusanthula zinthu chimene ndi...

### **KUDZIWA ZINTHU ZIMENE ZIMAKHUDZA UMISHONI:**

Umishoni wa mpingo ndi kufalitsa uthenga wabwino. Zinthu zimene zawazungulira zimakhudza ndondomeko za ntchitoyi kuti ikwaniritsedwe. Ndongomeko ndi njira kapena dongosolo lokwaniritsa cholingachi. Ngati mukufuna kukwaniritsa cholinga cha kufalitsa uthenga wabwino, mukuyenera kukhala ndi ndondomeko kapene njira zochitira kuti mukwaniritse cholingachi.

Dongosolo lomweli silingagwire ntchito kwa munthu aliyense komanso kumalo aliwonse. Izi ndi chifukwa chakuti anthu awiri kapena malo awiri sakhala ofanana ngatinso mbewu kapena minda iwiri sizikhala zofanana.

Pamene mukusanthula magulu a anthu, malo, mitundu komanso magawo, mumakhala ndi chidziwitso chimene chimakuthandizani kupanga njira zoti mufikire anthu mosiyanasinyana ndi uthenga potengera nyengo zawo. Zinthu zimene zimatizungulira zimatidziwitsa za njira zimene titatenge pogawira anthu osiyana utsogoleri uthenga wabwino.

Mwachitsanzo, maiko ena amaletsa misonkhano ya mapemphero a pamtetete. Madera ena sumaloledwa kugula malo mkumangapo mpingo. Mmadera ena sumaloledwa kukhala ndi chikalata cha umishoni wa uthenga wabwino.

Malamulo ena samatanthauza kuti musiyere kutumikira ayi. Mukungoyenera kusintha njira zanu za kafalitsidwe ka uthenga wabwino ku malo amenewo. Mwachitsanzo mmalo mochita umishoni, mukhoza kupempha kalata yolowera dziko lina kukagwira ntchito. Mkatikati mogwira ntchito mkumawagawira anthu uthenga wabwino. Mmalo mwa misonkhano mukhoza kumachita utumiki wa munthu ndi munthu. Mmalo momanga mpingo, mukhoza kukhala ndi gulu la anthu kumasonkhana mnyumba ya okhulupirira.

Kusanthula malo kapena zinthu zimene zakuzungulirani, kumathandiza kupanga dongosolo monga lopeza malo a mpingo ndi kochitira mapemphero kumene anthu akhoza kubwerako. Komanso ngakhala nthawi imene anthu akhoza kukwanitsa kupezekako. Kusanthula malo kumathandiza kudziwa njira za kaperekere ka uthenga wabwino kamene kakhoza kupangisa uthenga ulandilidwe kwa anthu osiyana.

#### **KUONA MMENE MULUNGU AMACHITIRA NDI MUNTHU:**

Mulungu anatomiza chigumula chachikulu cha madzi pa dziko chifukwa cha nyenyo yowawa ya imene inadza chifukwa cha uchimo:

**Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha.**

**Ndipo Yehova anamva cisoni cifukwa anapanga munthu pa dziko lapansi, ndipo anabvutika m'mtima mwace.**

**Ndipo anati Yehova, Ndidzafafaniza anthu amene ndawalenga pa dziko lapansi; anthu, ndi nyama, ndi zokwawa, ndi mbalame za m'mlengalenga: pakuti ndimva cisoni cifukwa ndapanga izo (Genesis 6:5-7)**

Werengani nkhani ya Sodomu ndi Gomora mu Genesis 18-19. Mulungu anatumiza chiwerezo pa mizindayi chifukwa cha uchimo umene amachita.

Werengani nkhani ya Ninevi mu buku la Yona. Mulungu anakonza chiweruzo pa mzindawu chifukwa cha uchimo. Pamene mzinda wonse unalapa, Mulungu anachita nawo mosiyana chifukwa zinthu komanso miyoyo ya anthu inasintha.

Pali zitsanzo zambiri za Mbaibulo za mmene zinthu komanso machitidwe a Mulungu kwa munthu. Ngati mumvetsa machitidwe a Mulungu ndi munthu, mukuyenera kumvetsanso mmene zinthu zilili.

### **ZOIPA ZOYENERA KUPEWA**

Kusanthula zinthu zotizungulira ndi nkhani yochokera Mbaibulo. Muphunzira mwatsatanetsatane mu chipangano chakale ndi chatsopano mu maphunziro awiri akubwerawa. Koma musanatero, pali zoipa zina zimene muyenera kuzidziwa.

Kudzidziwa izi, pafunika kutenga nkhani ya kusanthula zinthu ya anthu khumi ndi awiri imene ikupezeka mbuku la Numeri 13-14.

Pali zoipa zina zapadera zochitika pa kusanthula zinthu mu nkhani imeneyi. izi ndi zina zimene muyenera kupewa:

### **MUSASANTHULE POWIRITSA NTCHITO MAGANIZO A UMUNTHU WOKHA:**

Chidziwitso chanu chambiri chimene muchipedza posanthula zinthu chimachokera pa kuwerenga ndi kuonetsetsa zinthu mdzikoli. Koma muyenera kuona mopitilira maonedwe a dziko pofuna kufikira dziko la uzimu.

Azondi amene anapita ku Kanani anaona ziphona mmaso awo a dziko. Pamene analakwitsa ndi poti amawasanthula pogwiritsa ntchito nzeru za dziko zokha. Maonedwe a dziko amaziona ziphona ngati zazikulu kwambiri.

Musapange ziganizo za uzimu pogwiritsa ntchito maganizo a umunthu okha. Zochitika za dziko ziphunzilidwe ngati zotsogolera njira zanu, koma mudzisanthulenso ku uzimu.

### **MUSAOPSEDWE NDI NTCHITO:**

Khumi mwa azondi a ku Kanani aja anaopsedwa ndi kukula kwa ntchito. Amaziona ziphona kuhka zammphamvu zoti sangazigonjetse. Amayang'ana mphamvu ya mdani ndi kuthekerera kwawo. Amakhazikika pa zotchinga osati kuthekerera kwawo.

Kusanthula zinthu zimene zatizungulira kumaulula zotchinga zambiri. Koma kusakhazikike pa kukula kwa ntchito. Khazikikani pa ukulu wa Mulungu. Musayang'ane kulephera kwanu koma

onani kuthekera kwa Mulungu. Musaopsedwe ndi mphamvu ya mdani chifukwa wamkulu ndi amene ali mwa inu kusiyana ndi wa dziko lapansi (I Yohane 4:4 ndi 5:4).

### **MUSAKHUDZIKE NDI MBIRI YOSAKHALA BWINO:**

Mbiri yosakhala bwino imene inabwera ndi azondi khumi mu Numeri 13 inakhudza chisankho cha anthu a Mulungu. Pamene mwakonzeka kuchita ntchito ya Mulungu, muzakumana ndi anthu amene adzakuuzani kuti sizingatheke. Adakuuzani maganizo olakwika ndi za mbiri yoipa.

Musalole kuti akukopeni, mukalolera, mudzakhala osowa kolowera ku uzimu monganso mmene analili Israyeli. Muzasemphana ndi mwayi olova kapena kuitanitsa malo atsopano a Mulungu.

### **MUSAKHALE AMANTHA NDI OSAKHULUPIRIRA:**

Israyeli sanalowe mdziko la malonjezano chifukwa chifukwa cha mantha ndi kusakhulupirira zochokera mu kusanthula kwawo:

**Koma anakwiya ndi ayani zaka makumi anai? Kodi si ndi awo adacimwawo, amene matupi ao adagwa m'cipululu?**

**Ndipo adawalumbirira ayani kuti asalowe mpumulo wace?**

**Si awo kodiosamverawo? Ndipo tiona kuti sanakhoza kulowa cifukwa ca kusakhulupirira (Ahebri 3:17-19)**

Musakhala kunja kwa malo chifukwa cha mantha ndi kusakhulupirira kuchokera pa zimene mwazimva.

### **MUSAPEZE ZOONA OPANDA CHIFUKWA:**

Kusanthula zinthu kwanu kuli ndi cholinga, osati kungopeza zinthu zimene mukufuna kudziwa ayi.

Azondi amapita ku dziko la Kanani anakapeza zoona zake zenizeni za malowo, anthu ake ndi zopezekako. Koma sanachite molingana ndi zimene anadziwa. Sanakhudzike ndi kutenga malo amene Mulungu anawapatsa.

Mukhoza kupereka nthawi yanu yonse kufufuza zinthu, kupanga dongosolo, komatu ndi pokhapokha muli mmunda wa zokolola ndi kugwiritsa ntchito njira zanu, anthu sangafikilidwe ndi uthenga wabwino.

### **MUSAKHAZIKIKE PA “NGATI,” KOMA KHAZIKIKANI PA “MUCHITA BWANJI”:**

Mu buku la Numeri 13, azondi amene anapita kukazonda dziko la Kanani, anatumidwa kuti akaone kuti dziko alitenga motani, osati akapange chiganizo kuti ngati atakalitenge. Patatha zaka 40 pamene Israyeli anabweranso pa malire a Kanani, azondi aja anatumidwanso kukozonda dzikolo. Koma anthuwa anadziwa ntchito yawo bwino kusiyana ndi azondi oyamba aja. Anatsimikizika za mmene angachitire osati ngati angatenge dzikolo lopatsidwa ndi Mulungu (Yoswa 2).

Monga okhulupirira, tatumidwa ndi Mulungu kupita kwa anthu a mitundu yonse ndi uthenga wabwino. Pamene tikusanthula, tikuchita ndi cholinga cha mmene tingachitire bwino kuti tifikire anthu ndi uthenga wabwino.



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “kusanthula zinthu zotizungulira.”

---

3. Lembani mitundu isanu ndi iwiri ya ya kusanthula zinthu zotizungulira mu phunziroli.

---

---

4. Lembani zifukwa zisanu ndi ziwiri za kufunika kwa kusanthula zinthu mogwirizana ndi umishoni wa mpingo wolalikira uthenga wabwino kudziko lapansi.

---

---

---

5. Membani zoipa zisanu ndi ziwiri zimene mungapewe posanthula zinthu zimene zakuzungulirani.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Paulo anagwiritsa ntchito nyengo imene analimo ngati khwerero mmalo mwa chotchinga ku uthenga wabwino. Werengani zitsanzo zili mmusimu ndi kuona mmene nyengo za anthu zinakhudzira njira zolalikira uthenga wabwino:

-Analalikira kwa iwo amene anali “a pansi” pakuwafikira mu muyeso wawo Aroma 12:16

-Anagwiritsa ntchito chilankhulo chogwirizana ndi zikhalidwe za anthu: Machitidwe 22:1-2

-Anasinthia makhalidwe ake kuti asalakwitse zikhulupiriro ndi zikhalidwe za anthu: I Akorinto 8:10-13, Aroma 14:15

-Sanawakakamize obadwa mwatsopano aja ndi makhalidwe a Chiyuda: Machitidwe 15:1-32

2. Chitsanzo cha zimene zimachitika pamene mukusanthula pogwiritsa ntchito nzeru za umunthu chikupezeka mu Machitidwe 27. Anthu amene anali mu ngalawa amasanthula zinthu pogwiritsa ntchito nzeru zawo. Choncho zimaoneka kuti ayenera kupitilira. Koma Paulo analandira chidziwitso cha uzimu. Mulungu anamuululira kuti sinali nthawi yake kupitilira ndi ulendo.
3. Chitsanzo cha kukhala owopsedwa ndi nyengo chikupezeka mu kusanthula kumene kuli mu II Mafumu 6:14-17. Gehazi anakhazikika pa ntchito yaikulu osati pa ukulu wa Mulungu.

## CHAPUTALA CHA 3

### MAZIKO A M'BAIBULO: CHIPANGANO CHAKALE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachimuyenera:

- Kudziwa zitsanzo za mu Chipangano Chakale za kusanthula zinthu zotizungulira.

#### MAWU OYAMBA

Baibulo lili ndi zitsanzo zambiri za kusanthula zinthu zotizungulira. Iyi ndi mbiri ya munthu padziko lapansi ndi mmene amachitira ku zofuna za zomwe zamuzungulira. Mwachitsanzo Baibulo limasanthula zakale, zatsopano ndi za kutsogolo kwa munthu. Komanso limasanthula mmene uzimu wa munthu ulili popanda Mulungu ndi kuufanizira ndi okhulupirira enieni. Komanso limasanthula adani athu a ku uzimu.

Muphunziro ili, muphunzira zitsanzo za Mbaibulo za kusanthula zinthu. Mkosatheka kusanthula chilichonse mogwirizana ndi mutu chifukwa ndi zochuluka. Pachifukwa ichi ndime zazikulu zokha ndi zimene zasankhidwa ngati zitsanzo.

#### GENESIS

Machaputala cha 1-2: Mulungu analenga dziko langwiro.

Chaputala cha 3: Tchimo linalowa mdziko. Kodi linakhudzidwa bwanji? Kodi Mulungu anasanthula bwanji uzimu wa Adamu ndi Hava tchimo litangolowa?

6:5-6: Onani mmene zochitika zinasinthira kuchokera pa zimene zikunenedwa mu Genesis 1-2.

Machaputala 6-7: Mulungu anasanthula ndi kuthana ndi nyengo yoipa ya padziko.

Chaputala cha 11: Werengani nkhani ya nsanja ya Babele. Fanizirani kusanthula kumene kunzchitika ndi anthu a Mulungu.

13:6-13: Zisankho molingana ndi tsogolo. Loti anapanga chiganizo cholakwikwa chogwirizana maonedwe ake a nyengo pogwiritsa ntchito umunthu osati nzeru za uzimu.

Isaki: analibe malire ndi zovuta za munyengo yake. (onani 24:34-35; 25:32; 26:12-14.)

Chaputala cha 22: Abrahamu anasanthula kusatheka kwa nyengo mu dziko nayamba kutenga zinthu mwa iye yekha osati kudikira pa dongosolo la Mulungu.

Machaputala 37-38: Mwa vumbulutso la uzimu, Yosefe anazindikira nyengo imene analimo ndi ya kutsogolo ndipo anapulumutsa mbadwo onse ku njala.

## **EKSODO**

Chaputala cha 2: Mayi wake wa Mose anasanthula nyengo yoopsa napulumutsa moyo wa mwana wake.

Chaputala cha 2-3: Mose anazindikira nyengo yake, nachita mosayenera, mkuthawira ku chipululu.

6:9: Onani mmene nyengo inakhudzira zimene Israyeli anachita pa Mau a Mulungu.

Machaputala 7-13: Akanakha kuti Farao anasanthula bwino nyengo, akanazindikira machitidwe a Mulungu pa iye mkuyamba kuchita bwino.

Chaputala cha 14: Kusanthula nyengo pogwiritsa ntchito nzeru za umunthu, zinapangitsa Israyeli kukhala kakasi. Mulungu analowerera pamene amawapulumutsa. Sitingathe kudziwa nyengo zathu pogwiritsa ntchito nzeru za umunthu zokha.

15:22-27: Israyeli pa madzi a Mara. Kodi anachita bwanji pa nthawi imene ija? Kodi Mulungu anagwiritsa bwanji ntchito nyengo ija?

Chaputala cha 32: Aroni awada anthu (amene anamuzungulira) chifukwa cha machimo ake.

18:1-27: Yetero anasanthula nyengo imene inabweretsa bungwe latsopano.

## **LEVITIKO**

Buku la Levitiko limakamba za malamulo a Mulungu kwa anthu ake. Malamulo ambiriwa amakhudzana ndi zinthu zimene zatizungulira monga kusala zakudya zina, za umoyo ndi za ukhondo. Zina zimakhudza za utsogoleri, za mmene angathetsere mikangano ndi mavuto ena. Malamulo ena amakamba za nyengo ya uzimu monga dongosolo la Mulungu pothana ndi machimo.

## **NUMERI**

Chaputala cha 13-14: kusiyana pakati pa kusanthula kwa uzimu ndi kwa kuthupi. Azondi khumi amaliona dziko mmaganizo awo a thupi. Koma awiri okha amaona mwa uzimu.

Chaputala cha 22-25: Werengani nkhani ya Balaki ndi Balamu. Maonedwe a Balaki amatsaira pemphe lake kwa Balamu.

*Dziwani: Mabuku a Eksodo, Numeri ndi Deuteronomo amakamba za zochitika za ana a Israyeli mu chipululu atatha kukana kulowa mdziko la malonjezano chifukwa cha mantha ndi kusakhulupirira. Zambiri zikhodza kuphunziridwa ndi mmene anthu a Mulungu amasanthulira zinthu ndi kuthana ndi nyengo pa ulendo wa zaka zokwana 40.*

## DEUTERENOMO

Chaputala cha 1-4: Machaputalawa amakamba za mbiri ya Israyeli mu ulendo wawo wa mu chipululu. Onani mmene nyengo zawo ndi mmene anachitira zinakhudzira ubale wawo ndi Mulungu.

Chaputala cha 6: Kodi zingatheke bwanji nyengo ndi malo abwino komanso olemera kukhudza ubale wanu ndi Mulungu.

## YOSWA

Chaputala cha 2: Kusanthula kwa nyengo ya azondi awiri. Onani kusanthula kwawo mmene kunasiyanira ndi azondi ena mu Numeri 13-14. Chikhulupiriro sichichepetsa zovuta utatha kusanthula. Chikhulupiriro chimangoziona zazing'ono kuyerekeza ndi mphamvu ya Mulungu.

Chaputala cha 7: Yoswa sanakhale tcheru ku nyengo ya uzimu ndipo anagonja.

Chaputala cha 9: Zotsatira za kusanthula mwa nzeru zathu popandapo uphungu wa Mulungu. Onani vesi la 4.

*Dziwani: Kusanthula zinthu kunali kofunika mu buku la Yoswa pokonzekera nkhondo zimene zimabwera mu dziko limene iwo amakhala. Dongosolo la nkhondo linakhazikika pa zimene anasanthula. Izi ndi zoonza zake za nkhondo za muchipangano chakale. Kodi zingathe kugwira ntchito ku uzimu?*

## OWERUZA

Buku la oweruza ndi mbiri ya mafumu amene analamulira anthu a Mulungu. Mafumu ena anali abwino pomwe ena anali oyipa. Bukuli limakambansi za nkhani ya oweruza a umulungu amene Mulungu anawadzutsa kuti apulumutse anthu ku ukapolo. Utsogoleri wa umulungu komanso wopanda umulungu ukutsindikizidwa mu bukuli. Za mmenenso athu a Mulungu anachitira ku mautsogoleri amenewa zimaonetsranso mmene Mulungu anachitira.

## RUTE

Werengani buku lonseli la nkhani yaifupi ndi kuona mmene Naomi anazindikirira nyengo yake pofooketsa chikhulupiriro cha Rute mu chaputala cha 1. Onaniso mmene Naomi anasanthulira

ndi kuchitira ndi Boazi poyanga'ana nyengo ya Rute. Boazi amagwira ntchito mu chikhalidwe chake poombola Rute (chaputala cha 4).

## **I SAMUELI**

2:113:21: Eli sanasanthule bwibobwino nyengo yake ya uzimu ya mnyumba mwake.

15:1-35: Sauli anazindikira pogwiritsa ntchito nzeru za umunthu osati lamulo la Mulungu. Anasemphana ndi ufumu chifukwa chimenechi.

## **II SAMUELI**

Chaputala cha 12: Kusanthula kwa za uzimu kwamphamvu kwa Natanieli. Zotsatira zake Davide analapa tchimo.

Machaputala 13-19: Nkhani ya kugalukira kwa Abisalomu. Kodi nyengo inamukhudza bwanji? Kodi Davide adakana kuona nyengo mmene inalili?

## **I MAFUMU**

9:1-10:29: Kodi nyengo ya Solomoni idali yotani?

11:1-43: Kodi nyengo inakhudza bwanji Solomoni ku uzimu?

## **II MAFUMU**

Bukuli ndi mbiri ya mafumu amene amalamulira anthu a Mulungu. Onani mmene nyengo inakhudzidwira ndi atsogoleri a umulungu ndi opanda umulungu. Kodi anthuwa anakhudzidwa bwanji?

## **I NDI II MBIRI**

Mbiri ya chipembedzo cha anthu a Mulungu inalembedwa mmabukuwa. Pamene mukuwerenga mabukuwa, onani mmene nyengo inakhudzidwira ndi atsogoleri a uzimu ndi opanda uzimu.

## **EZARA**

Ezara anasanthula nyengo ya Yerusalemu ndi kudziwa chosowa chomanganso Kachisi. Pa nthawi imene amamanga, anakumana ndi omutsutsa amene amakhala nawo chifupi. Ndi khama lake la ku uzimu, anadziwa mmene akanachitira ku nyengo iliyonse moyenera. Onani makamaka mmene anachitira pa uchimo wa anthu a Mulungu mu chaputala cha 9-10.

## **NEHEMIYA**

Kusanthula nyengo kukukhazikika mu bukuli, pamene akukamba za kumangidwanso kwa chipata cha Yerusalemu ndi Nehemiya. Makamaka onani mu 2:11-20 nyengo yake yak u Yerusalemu. Mu buku lonse, Nehamiya akupitilira kusanthula nyengo ndi kuchita mwa chikhulupiriro pa zinthu zosakhala bwino zimene zimasokoneza ntchito ya Ambuye.

### **ESTERE**

Chaputala cha 2: Kusanthula zinthu ka Modekaye kunapangitsa Estere kupezeka pamalo abwino amene Mulungu anamugwiritsa ntchito.

Chaputala cha 3-9: Estere anasanthula nyengo ndi kupanga dongosolo lopulumutsa mtundu wonse.

### **YOBU**

Bukuli ndi nkhani ya munthu wolungama wotchedwa Yobu amene anakanthidwa ndi Satana ku thupi, mmaganizo, ku chuma, ku maubale ndi ku uzimu. Yobu anadziwa mmene nyengo zake zinalili, ndipo abwenzi ake anachita mosayenera potengera maganizo awo a umunthu, ndipo bukuli likutsindika pa kusanthula kwa Mulungu.

### **MASALMO**

1:1-3: Nyengo ya munthu wa Mulungu ikusanthulidwa.

3:6: Musaope mphamvu za nyengo zimene zakuzungulirani.

11:4-5; 14:2-3; 17:3: Mulungu amasanthula chilengedwe chonse.

19:12,14; Machaputala 26, 51, 69; 40:2-3; 119:59: Davide anatenga nthawi yaitali kuzisanthula yekha. Izi ndi zitsanzo zochepa chabe mu buku la Masalmo.

Machaputala 78, 105-107: Kusanthula mtundu wa Israyeli.

115:4-8; 135:15-18: Kusanthula kwa mafano onama.

### **MIYAMBO**

Ndime zambiri mu bukuli zimasanthula ndi kuchenjeza pa nyengo yoipa. (Onani 1:10-19; 2:10-22; 4:14-19; 7:6-27; 9:13-18.)

Chaputala 5; 14:7: Tikuyenera kuthawa nyengo zina. Onani 5:8

6:6-11: Werengani nthawi ya nyerere ndi kuona chimene mungaphunzire.

6:27-28; 22:24-25: Nyengo ya kuthupi kaya ku uzimu imakukhudzani.

20:4: Musalole nyengo yanu kuti ikulepheretseni kugwira ntchito yanu.

21:2: Mulungu amasanthula mitima yanu.

21:29; 4:26: Tinauzidwa kuti tiyang'anitsitse mayendedwe athu, ndi malo opitano mapazi athu. Uku ndi kuzisanthula kwa munthu.

24:30-34: Munda wosabala umasanthulidwa.

27:23: Onani mmene nkhosa zanu zilili, kuthandauza kuti tikuyenera kusamala iwo amene timawayang'anira.

### **MLALIKI**

Bukuli ndi kawuiwuni wa moyo wa pansu pano padziko kupatula kwa Mulungu. Wolemba akusanthula chilichonse chopezeka mdziko ndi chachabe. Kumaliza kwake ndi kusanthula kopezeka pa 12:13-14.

### **NYIMBO YA SOLOMONI**

Bukuli limaonetsa ubale wa pakati pa Yesu ndi Mpingo monganso zimakhallira mu ubale wa mbanja. Onani kusanthula kwa munthu ngati mkwatibwi ndi mkwati.

### **YESAYA-DANIELI**

Mabuku a Yesaya mpakana Danieli amatchedwa aneneri a akulu. Mauneneli awo ndi a atali opita kwa a mitundu kuchokera kwa aneneri amene amauzilidwa ndi Mulungu. Onaninso mabukuwa ndipo onani mmene nyengo ya uchimo analingololera imene anthu amakhalamo. Onani uneneri wa mmene Mulungu anapangira dongosolo lothana nawo chifukwa cha uchimo wawo. Kodi zilipo zinthu mdziko lero zimene ndi umboni?

Onaninso nkhani ya Danieli ndi abwenzi ake atatu mu chaputala cha 1-3 ndi 6. Sanalole nyengo ya uchimo ikhudze uzimu ndi ubale wawo ndi Mulungu.

### **HOSEYA-MALAKI**

Buku ka Hoseya mpaka Malaki amatchedwa aneneri ang'ono chifukwa cha mauneneri awo ochepa, osati chifukwa uthenga wawo unali osafunika ayi.

Aneneriwa, mouzilidwa ndi Mulungu, anazindikira nyengo ya maiko osaiyana. Onaninso mabukuwa, ndi kuyang'ana mmene nyengo yawo ya uchimo mmene inalili ndi mmene Mulungu anathanirana nawo chifukwa cha uchimo, kodi zinthu zimene amachitazo zikupedzeka mdziko lathu lero? Onani Amosi 4:6-13 akulongosola mmene Mulungu anagwiritsira ntchito nyengo



pothana ndi anthu ake. Akanazindikira nyengo yawo ndi kulapa, Mulungu akanawakhululukira ndi kuwachiritsa.

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Chidule ichi chikuonanso za chipangano chakale pa za kufumika kwa kumvetsa ndi kuchitapo kanthu pa nyengoyo. Anthu a Mulungu...

...Anagonjetsedwa pamene anasanthula nyengo ndi maganizo awo a mantha ndi kusakhulupirira kapena pamene analephera kusanthula kumene.

...Anapambana pa chigonjetso chachikulu pamene anasanthula nyengo zawo ndi maso a uzimu.

...Analora nyengo zawo ziwalamulire ku uzimu, kumanso ku ubwino ndi kukuipa.

...Anakhudza nyengo yawo imene amakhala, kugwira ntchito ndi kutumikira.

...Anagwira ntchito pakati pa chikhalidwe chawo pokwaniritsa dongosolo la Mulungu.

Pali zitsanzo zambiri za kusanthula nyengo mu chipangano chakale. Pitilizani phunziroli ndi kutambasula maphunzirowa mu zolemba zanu pa mutuwu.

## CHAPUTALA CHA 4

### MAZIKO A M'BAIBULO: CHIPANGANO CHATSOPANO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kudziwa zitsanzo za mu Chipangano Chatsopano za kusanthula zinthu.

#### MAWU OYAMBA

Muphunziro loyamba mwaphunzira za mfundo za mbaibulo za kusanthula zinthu mu Chipangano Chakale. Muphunziro ili tionanso mu Chipangano Chatsopano.

Izi ndi zina mwa zitsanzo mu Chipangano Chatsopano za kusanthula nyengo kapena zinthu zotizungulira.

#### MAUTHENGA ABWINO

##### **Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane**

Mauthenga amapereka mfundo zofanana za nyengo ndi nthawi ya utumiki wa Yesu ndi mmene anasanthulira nyengo. Chifukwa cha ichi, mabukuwa akuonedwa pamodzi. Kutsindika pa utumiki wa Yesu mu mauthenga abwino. Onani mmene Yesu....

...Anasanthulira nyengo ndi kudziwa mmene anatumikilira zosowa za anthu.

...Anazindikira mafunso a amene amasusana nawo kuti asakodwe.

...Anadziwira maganizo ndi ntchito za anthu. Mwachitsanzo, munthu mwini chuma amene sanavomere ku maitanidwe ake a Yesu chifukwa cha chuma, zolinga ndi dongosolo la Yudas, chikondi chenicheni cha Petro ndi zina.

...Anadziwa nyengo yache ya mu mzinda imene amatumikira. Mwachitsanzo onani Mateyu 23:37-39; Luka 13:34-35 ndi Mateyu 11:21-24.

Mauthenga abwino amaunikira za nthawi ya chipembedzo mmene chinalili mu nthawi ya Yesu. Kodi ndi zinthu zimene zimakhudza atsogoleri achipembedzo potengera za iwo otchedwa Alembi, Afalisi ndi Asaduki?

Izi ndi zina mwa zitsanzo zokhuzana nyengo zawo:

Mateyu 7:15-20: Mmene mungadziwire mautumiki oona ndi onama.

Mateyu 13: Kuzindikira dera lolandira mawu.

Mateyu 10:5-15; Marko 6:10-11: Kuzindikira nyengo pamene mukutumikira ndi kuchita bwino.

Marko 13:5-35: Kuzindikira tsogolo la dziko mmene lingadzakhalire.

Luka 14:7-14, 28-32: Zitsanzo zimene zimatsindika pa kufunika kwa kusanthula nyengo.

### **MACHITIDWE**

2:41-47; 5:42: Mavesiwa amasanthula nyengo ya uzimu ya mpingo woyamba ku Yerusalemu.

6:1-6: Kusanthula kwa nyengo imene inabweretsa kusankha atumiki woyamba.

6:7: Kusanthula nyengo ya ku Yerusalemu.

8:17-24: Petro asanthula munthu wotchedwa Simon.

10:34-11:18: Petro asanthula mmene Mulungu anagwirira ntchito pa amitundu.

11:27-30: Kusanthula nyengo yak u Yudeya

Chaputala cha 13-38: Paulo anayendera mizinda yambiri ndi kutumikira kwa anthu ambiri. Onani mmene Paulo anazindikirira ndi kusintha uthenga wabwino molingana ndi nyengo imene analimo.

Chaputala cha 27: Kusanthula kuwiri kotsutsana ndi zotsatira.

### **AROMA**

1:7-8: Paulo anawazindikira okhulupirira a ku Aroma. Kodi ndi zinthu ziti zitatu zimene anakamba za iwo?

1:21-32: Kusanthula nyengo yoipa ya anthu amene anaperewera pa ulemerero wa Mulungu.

3:9-19,23; 5:12: Kusanthula dziko lopanda Mulungu.

10:1-3,21: Kusanthula mtundu wa Israyeli.

11:2-4: Kusanthula kwa kuitanidwa kwa mneneri Eliya.

16:17-18: kusanthula kwa iwo amene amayambitsa magawano mu Mpingo.

### **I AKORINTO**

Chaputala cha 8: Paulo adziwa milungu yabodza (mafano)

9:19-22: Kusanthula kwa Paulo mwani.

10:27-33: Santhula nyengo yanu mosamala. Musakhumudwitse ena ndi ntchito zanu.

16:8-9: kusanthula mzinda wa Aefeso.

## **II AKORINTO**

1:8-9: Kusanthula m'Asiya.

2:12-13; 7:5; 8:1-5; 11:9: Kusanthula Makedoniya.

4:7; 5:17: Kusanthula okhulupirira mwa Yesu.

9:1-4: Kusanthula Akaya.

Paulo anasanthula mpingo wa ku Akorinto mu buku la I ndi II Akorinto. Kodi mwaphunzira chiyani zokhudza mpingo kuchokera kukusanthulaku?

## **AGALATIYA**

1:6-7; 3:1-5; 4:9-20; 5:1,7-8; 6:15: Ndi ziti zimene zalankhulidwa zokhudza mpingo wa ku Agalatiya molingana ndi mavesi amene aperekedwa?

1:4: Kusanthula za mmene dziko lilili.

1:11-2:21: Kuzisanthula yekha kwa Paulo.

Chaputala cha 3: Kusanthula kwa Abrahamu.

5:16-21; 6:7-8: Kusanthula kwa moyo wokhala kuthupi.

5:22-26: Kusanthula kwa moyo wa Mzimu wa Mulungu.

6:3: Samalani za mmene mumazisanthulira!

## **AEFESO**

1:3: Kusanthula kwa Paulo kwa madalitso a uzimu mwa Yesu amene ali kwa okhulupirira. Anawadziwa ambiri mu buku la Aefeso. Lembani madalitsowa potengera kusanthula kwa Paulo mu machaputalawa.

2:1-3, 11-12: Kusanthula za mmene tinalili tisanamdziwe Ambuye.

2:4-10, 13-22: Mmene tilili pano titamdziwa Ambuye.

3:7-8; 4:1; 6:19-20: Kudzisanthula kwa Paulo.

4:3-6: Kusanthula thupi limodzi lowona la Khristu.

4:11-16: Kusanthula zolinga za mphatso za uzimu.

4:17-5:9: Phunzirani kusanthula kwa Paulo pa makhalidwe athu akale. Siyanitsani ndi malangizo a makhalidwe a okhulupirira.

6:11-18: Kodi kusanthula uku kukuphunzitsa chani zakhudza adani a ku uzimu.

### **AFILIPHI**

1:12-14,19: Paulo asanthula nyengo zake.

1:15-18: Kusanthula zolinga zosiyana za utumiki.

1:20-25: Kusanthula phindu la imfa ndi moyo.

2:5-8: Kusanthula maganizo a yesu.

2:25-30: Paulo asanthula bwenzi lake Epafrodito.

3:3-14: Paulo azisanthula yekha.

3:18-21: Kusanthula adani a mtanda.

4:11-13: Mmene Paulo anasanthulira ndi kuthana ndi nyengo zake.

4:14-18: Kodi ndi ziti zimene mungaphunzire zokhudza mpingowa ku Afilipi kutengera zimene Paulo anawauza?

### **AKOLOSE**

Ku mpingo wa ku Akolose kunali gulu la okhulupirira limene linabwera ndi ziphunzitso zonama. Kodi Paulo anasanthula bwanji za nyengo imeneyo? Kodi kusanthulako kunamuthandiza bwanji kuti athane ndi nyengoyo? Ndi lamulo liti limene Paulo anapereka pofuna kukonza nyengoyo ndi kulimbana ndi chiphunzitso chonama?

### **I NDI II ATESALONIKA**

Kodi mungaphunzire chiyani za mpingo wa ku Atesalonika molingana ndi uthenga umene ukupezeka mbukuli? Ndi zina mwa zinthu ziti zabwino zokhuza mpingowu zimene Paulo anazikambapo? Ndi magawo ati amene amafuna kukonza?

## I TIMOTEO

I ndi II Timoteo analembedwa ndi mtumiki wachpchipere wotchedwa Timoteo. Werengani mabuku onsewa ndi kuona zimene Paulo anasanthula zokhudza makhalidwe oyenera a mtumiki wa uthenga wabwino.

1:4-7: Kusanthula kwa zinthu zina zimene zinachotsa anthu ku uthenga wabwino.

1:8-10: Kusanthula cholinga cha lamulo.

1:11-16; 2:7: Kuzisanthula wa Paulo.

1:18-20: Kodi ndi ziti zimene mungaphunzire kwa Humenayo ndi Alesandro pa kusanthula kwa Paulo?

3:1-13: Kusanthu pa zowayenereza atsogoleri a mpingo.

4:1-5: Kusanthula kwa nyengo ya masiku otsiriza.

4:6-6:21: Phunzirani kusanthula kwa Paulo pa zinthu zimene zimamupanga Timoteo kukhala mtumiki wabwino wa Mulungu.

## II TIMOTEO

1:5-6, 13-14; 3:15: Kutengera ndi zimene zikupezeka mu mavesiwa, kodi mungaphunzire chiyani zokhudza nyengo ya Timoteo.

1:11-12; 2:9-10; 3:10-11; 4:6-8,18: Kuzisanthula kwa Paulo.

1:15-18: Kusanthula nyengo yak u m'Asiya ndi munthu wotchedwa Onesiforo.

3:1-9,13; 4:3-5: Kusanthula za masiku otsiriza.

3:16-17: Kusanthula za cholinga cha Mau Mulungu.

4:9-17: Kusanthula kwa anthu osiyana amene Paulo amakumana nawo.

## TITO

Buku la Tito linalembedwanso ndi Paulo kwa mtumiki wachichepere. Ndi ziti zimene Paulo anasanthula zoyenera kwa mtumiki wochita bwino wa uthenga wabwino? Kuonjezera, werenganinso ndimezi:

1:9-16; 3:10-11: Kusanthula anthu osapembedza.

3:3-7: Kusanthula pa chimene tinali kuyerekeza ndi chimene tili mwa Yesu.

### **FILEMONI**

Werengani buku lalifupili la ndime imodzi yokha. Santhulani nyengo imene Paulo amalimbana nawo molingana ndi mavesi omwe akupezekawo.

### **AHEBRI**

Chaputala cha 3-4: Kusanthula chifukwa chimene Israyeli sanalowe mu zinthu zabwino za Mulungu.

5:12-14: Kusanthula kwa okhulupirira amene alibe luso Mmau a Mulungu.

Chaputala cha 7: Kusanthula kwa kulimbana kwa moyo ndi thupi.

Chaputala cha 8: Kusanthula pa kusiyana kwa moyo wa uzimu.

Chaputala cha 11: Kusanthula chikhulupiriro ndi kufunika kwake mmoyo wa anthu a Mulungu.

Chaputala cha 12: Kusanthula cholinga cha chilango.

Buku la Ahebri limakamba za pangano lakale ndi latsopano la Mulungu ndi munthu, kusanthula kusiyana dongosolo la ubale wake ndi munthu.

### **YAKOBO**

1:6-8: Kusanthula kwa munthu wa mitima iwiri.

1:12-14: Kusanthula nyengo ya mayesero.

1:17: Kusanthula komwe kumachokera mphatso.

1:27: Kusanthula maziko a chipembedzo choyenera.

2:1-9: Magwiritsidwe ntchito osayenera a kusanthula.

2:20-24: Kusanthula umunthu wa Abrahamu.

2:25-26: Kusanthula Rahabe.

3:1-13: Kusanthula mwa manthu pa lilime lathu limene limakhudza nyengo zathu.

3:14-16: Kusanthula mao amene pamapedzeka mikangano.

4:1-3: Kusanthula nyengo imene imayambitsa nkondo ndi kumenyana.



5:1-6: Kusanthula anthu a chuma.

5:16-18: Kusanthula moyo wa Eliya.

## **I PETRO**

Petro akulimbana ndi nyengo ya masautso mu ndimezi. Kodi akunenapo chiyani pa kusanthula cholinga, zotsatira ndi malingaliro oyenera a okhulupirira mu nyengo imeneyi? Werenganinso ndi kuona malangizo amene aperekedwa kwa okhulupirira kuti akhale ndi nyengo yabwino ku mpingo pa makhalidwe a chipembedzo.

## **II PETRO**

Chaputala cha 2-3: Kusanthula kwa anthu amene anali onyenga. Fananitsani ndi kusanthula kwa Yuda.

## **I YOHANE**

Yohane analemba njira zambir za mmene mungazisanthule nokha pofuna kuona kuti mumamdziwa Mulungu. Werengani bukuli ndi kuona zimenezi.

1:6-10: Kufunika kwa kuzisanthula wekha.

2:15-17; 5:19: Kusanthula dziko.

2:18-19: Mmene mungasanthulire ndi kuzindikira mzimu wa okana Khristu.

4:1-6: Kusanthula mizimu pa malangizowa.

5:4: Mmene mungagonjetsere nyengo iliyonse.

## **II YOHANE**

Vesi la 4: Kusanthula okhulupirira amene amawalemba.

Mavesi 7-11: Kusanthula onyenga.

## **III YOHANE**

Mavesi 1,3-8: Kusanthula munthu wotchedwa Gayo.

Mavesi 9-12: kusanthula pa kusiyana kwa Diotrefe ndi Demetriyo.

## **YUDA**

Vesi 4: Kusanthu kwa anthu ena, kwa chaputala chonse. Kodi mungaphunzire chiyani za anthuwa mu chaputalachi?

Vesi 5: Kusanthula Aigupto.

Vesi 6: Kusanthula za angelo oyipa.

Vesi: Kusanthula za Sodomu ndi Gomora.

## **CHIBVUMBULUTSO**

Buku la Chibvumbulutso limasanthula za nyengo ya masiku a nthawi ino otsiriza a padziko lapansi. Werengani bukuli ndi kuona nthawizi.

Chaputala cha 2-3: Kusanthula kwa nyengo ya mipingo 7 ya Ku m'Asiya. Kodi makhalidwe amenewa mukuwaona mu mpingo wa lero?

Chaputala cha 21-22: Kusanthula nyengo ya Kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano limene Mulungu adzalenga.



## CHAPUTALA CHA 5

### KUZISANTHULA KWA MUNTHU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la kuzisanthula kwa munthu.
- Longosolani zimene zimakhudza kusanthula kwa munthu.
- Kudziwa zolinga za kuzisanthula kwa munthu.
- Kusanthula munthu payekha.
- Kugwiritsa ntchito zotsatira za kuzisanthula pokwaniritsa utumiki wanu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Dziyeseni nokha, ngati muli m'cikhulupiriro, dzitsimikizeni nokha... (II Akorinto 13:5)**

### MAWU OYAMBA

Mwaona mawu oyamba a kusanthula nyengo ndi maziko a Mbaibulo. Chaputala ichi muona maphunziro otsatana amene mulongosola za mmene mungasanthulire nyengo zambiri. Onetsetsani kuti mukumaliza maphunziro anu musanapite ku phunziro lina pamene maphunziro akuthandizana. Mu phunziro ili muphunzira za kusanthula munthu payekha.

### KUSANTHULA MUNTHU PAYEKHA

Kusanthula munthu payekha ndi kuphunzira nyengo zanu. Komanso kuphatikiza moyo wanu, maubale anu, zinthu zanu zooneka, maphunziro, chuma chanu ndi moyo wanu wa uzimu.

### CHOLINGA CHA KUZISANTHULA NOKHA

Izi ndi zolinga za kuzisanthula nokha:

#### KUTI MUONE MMENE MOYO WANU WA UZIMU ULILI:

Baibulo limanena kuti muyenera kuzisanthula nokha kuti muone mmene moyo wanu wa uzimu ulili:

**Dziyeseni nokha, ngati muli m'cikhulupiriro, dzitsimikizeni nokha... (II Akorinto 13:5)**

**Koma munthu adziyese yekha (I Akorinto 11:28)**

Mukuyenera kuzisanthula nokha molingana ndi “chikhulupiriro.” Izi zikutanthauza moyo wanu wa uzimu molingana ndi Mau a Mulungu. Kudzitsimikizira nokha ndi chimodzimodzinsu kuzisanthula. Baibulo limati:

**Yesani zonse; sungani cokomaco (I Atesalonika 5:21)**

Kuzisanthula nokha kumakhudza kuonanso moyo wanu wa uzimu, komanso kuona madera amene muli ochitachita. Awa ndi monga maonekedwe anu, chuma chanu, maphunziro anu ndi zina. Mukuyenera “kuziyesa” mu “zonse” mmoyo wanu.

Munthu ali ndi thupi, moyo ndi mzimu. Chimene chimachitikira thupi chimakhudza moyo wa uzimu. Mmene moyo ndi mzimu ulili zimakhuzza thupi. Ichi ndi chifukwa chake muyenera kusanthula zinthu zonse.

Ndi kofunikanso kusanthula mmoyo wanu chifukwa madera amene mumachitachita akhoza kuopseza dongosolo la Mulungu pa inu. Zinthu za dziko lapansi zikhoza kutchinga ntchito ya Mulungu mmoyo wanu:

**Ndipo malabadiro a dziko lapansi, ndi cinyengo ca cuma, ndi kulakalaka kwa zinthu zina, zilowamo, zitsamwitsa mau, ndipo akhala opanda cipatso (Marko 4:19)**

Zochitika zokhudza moyo zimalepheretsa kubala chipatso ku uzimu:

**Ndipo zija zinagwa ku mingazi, ndiwo amene adamva, ndipo m'kupita kwao atsamwitsidwa ndi nkhawa, ndi cuma, ndi zokondweretsa za moyo, ndipo sakhwimitsa zipatso zamphumphu (Luka 8:14)**

Kukangalika mu zochitika zonse kumatchinga nkhondo ya uzimu:

**Msilikari sakodwa nazo nchito wamba, kuti akakondweretse iye amene adamlemba usilikari (II Timoteo 2:4)**

Chidwi pa zochitika za moyo zimakugonjetsani kulephera kukonzekera kubweranso kwa Ambuye:

**Koma mudziyang'anire nokha, kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi madyaidya ndi kuledzera, ndi zosamalira za moyo uno, ndi kuti tsiku ilo lingafikire inu modzidzimutsa ngati msampha (Luka 21:34)**

**KUDZIWA ZOFOOKA ZANU ZA KU UZIMU:**

Simukhala amphamvu mu utumiki pokakamiza zofooka zanu. Mumakhala amphamvu pa kulimbikitsa mphamvu za uzimu zimene Mulungu akupatsani. Mu fanizo la matalente ku Mateyu 25:14-30, kapolo wina aliyense Anaika chidwi pa zimene anali nazo, osati pa zimene analibe.

Mumadziwa mphamvu zanu za uzimu chifukwa cha utumiki, osati chifukwa cha kuthekera kwanu. Mphamvu zanu zonse zimene muli nazo ndi zochokera kwa Ambuye, monganso mmene zinalili mu fanizo. Monganso kapolo mu fanizo, muli ndi udindo wogwiritsa ntchito mphamvu za uzimu, luso ndi kuthekera ku ulemerero wa Mulungu.

Kumbukiraninso kuti sizitengera kuti muli ndi mphamvu zotani zimene muziziwa, koma pali mwayi wochitanso bwino. Paulo anasanthula mphamvu zake koma anati...

**Si kunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndatha kukonzeka wamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinso ndikacigwire ici cimene anandigwirira Yesu Kristu.**

**Abale, ine sindiwerengera ndekha kuti ndatha kucigwira: koma cinthu cimodzi ndicicita; poiwaladi zam'mbuyo, ndi kutambalitsira zam'tsogolo,**

**ndilondetsa polekezerapo, kutsatira mfupo wa maitanidwe akumwamba a Mulungu a mwa Kristu Yesu.**

**Tonsefe amene tsono tidakonzeka amphumphu, tilingirire ici mumtima; ndipo ngati kuli kanthu mulingirira nako kwina mumtima, akanso Mulungu adzabvumbulutsira inu (Afilipi 3:12-15)**

Pamene mukuzindikira mphamvu zanu za ku uzimu, kumbukirani kuti chipambano sichiyesedwa ndi chimene muli. Koma chimayesedwa ndi chimene mufana nacho pa chimene mukhala mwa Mulungu. Uthenga wofunika wa buku la Yobu mbaibulo ndi oti munthu wolungama akhoza kupindula pa zimene akumana nazo ndi Mulungu.

#### **KUDZIWA MPHATSO ZANU ZA UZIMU:**

Mphatso za uzimu ndi kuthekera kwapadera kwa mzimu woyera kopangisa ntchito ya utumiki iyende. Mutuwu ndi wofunika kuti Hvestime International Institute ali ndi buku lake la izi.

Phunziro la “*Utumiki wa Mzimu Woyera*” limalongosola mphatso za Mzimu mwachindunji. Ngati simumvetsa mphatso za mzimu kapena simunadziwe mphatso zimene Mulungu anakupatsani, phunziroli likhoza kukuthandizani kudziwa.

Baibulo limaphunzitsa kuti wokhulupirira aliyense ali ndi mphatso imodzi (I Akorinto 12:4-11) imene mukuyenera kuidziwa ndi kuitukula ngati mphatso yanu (II Timoteo 1:6).

Uwu ndi mndandanda wa mphatso za uzimu:

**Mphatso zapadera:** Izi zimaperekedwa ndi cholinga chokonzekeretsa anthu a Mulungu ku ntchito ya utumiki.

Atumwi, Aneneri, Alaliki, Abusa ndi Aphunzitsi

**Mphatso zolankhula:** Mphatso izi zimalongosola choonadi cha Mulungu:

Uneneri, Chiphunzitso, Chilimbikitso, Mau a nzeru ndi Mau a chidziwitso.

**Mphatso zotumikira:** Mphatso izi zimachita ntchito ya Mulungu.

Kutumikira, Kuthandiza, Utsogoleri, Dongosolo, Kupereka, Kuonetsa chifundo, Kuzindikira Mizimu, Chikhulupiriro, ndi Kucheleza alendo.

**Mphatso za zizindikiro:** Mphatso izi zimakhazikitsa ulamuliro wa Mulungu.

Malilime, Kupembedzera, Zodabwitsa, Machiritso.

#### **KUDZIWA MALO ANU MU UTUMIKI:**

Kudziwa malo mphatso yanu ya uzimu ndi njira yokhayo yodziwira malo anu mu utumiki. Mutatha kudziwa mphatso yanu, mukuyenera kudziwa kumene Mulungu akufuna kuti kuti mukagwiritse ntchito mu thupi la Khristu.

Werengani I Akorinto 12 Mbaibulo lanu. Chaputalachi chimalongosola za mmene Mpingo ukufananira ndi thupi la munthu. Monga ngati gawo lililonse la thupi lili ndi ntchito yake, momwemonso chiwalo cha mu mpingo wa Khristu. Kuti mukhale wamphamvu, mukuyenera kudziwa malo anu mu thupi la Khristu. Kuti mudziwe chifuniro cha Mulungu, mukuyenera kudzipereka nokha ngati nsembe yoti ayigwiritse ntchito monga mmene afunira Iye.

**Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera.**

**Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansu pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifundo ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro (Aroma 12:1-2)**

Mukuyenera kudziwa mphatso yanu ya uzimu, kusanthula mphamvu zanu ndi zofooka zanu ndi kudziyesa nokha pa chifuniro cha Mulungu. Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “*Kudziwa Liwu la Mulungu*” limene likuthandizani pa maphunzirowa.

Tchimo lina la kuthupi mu buku la Agalaitiya 5:20 ndi “kutsanzira.” Uku ndi kuyesera kuchita zimene wina achita. Mulungu safuna inu kuti muzikopera utumiki wa ena. Amafuna inu mudziwe malo anu mu a utumiki ndi utumiki umene wakonzera moyo wanu:

**Koma yense ayesere nchito yace ya iye yekha, ndipo pamenepo adzakhala nako kudzitamandira cifukwa ca iye yekha, si cifukwa ca wina (Agalatiya 6:4)**

#### **KUKONZA DONGOSOLO LOKWANIRITSA UTUMIKI WANU:**

Kusanthula bwino moyo wanu wa uzimu, mphamvu zanu, zofooka zanu, mphatso zanu za uzimu kuzapangitsa kuti mudziwe malo anu mu thupi la Khristu. Kumavumbulutsa malo anu mu utumiki.

Pakudziwa malo anu kokha sikukwanira. Mukuyenera kupanga dongosolo lokwaniritsa utumiki umene Mulungu wakupatsani, keneko kwaniritsani dongosololo:

**Ndipo kapolo uyo, wodziwa cifuniro ca mbuye wace, ndipo sanakonzana, ndi kusacita zonga za cifuniro caceco, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri (Luka 12:47)**

Kuzisanthula kwa munthu sikokwanira pokhapokha mugwiritsa ntchito zimene mwaphunzira pokwaniritsa utumiki wanu.

#### **MMENE TINGADZIWIRE ZINTHU**

#### **PEMPHERANI:**

Mfuseni Mulungu akuululireni mene uzimu wanu ulili, mphamvu zake, zofooka zake, ndi malo anu mu dongosolo lake. Davide anati:

**Mundiyesere, Yehova, ndipo mundisunthe; Yeretsani imso zanga ndi mtima wanga (Masalmo 26:2)**

#### **PHUNZIRANI MAU A MULUNGU:**

Mau a Mulungu ndu muyeso osasintha umene muyenera kudziyesa nawo:

**Mau anu aikika kumwamba, Kosatha, Yehova (Masalmo 119:89)**

#### **GWIRITSANI NTCHITO MPHATSO ZA UZIMU:**

Mphatso za uzimu zikuthandizani pa kuzitsandthula kwanu. Mwachitsanzo, Ambuye atha kukupatsani chidziwitso chokhudzana kufooka kwanu ku moyo wa uzimu kapena kugwiritsa ntchito wina ndi mphatso ya chidziwitso kapena mau a nzeru kutumikira moyo wanu.



## **FUNANI UPHUNGU KWA ATSOGOLERI A UZIMU:**

Funsani atsogoleri anu a uzimu akuthandizeni kukusanthulani. Mulungu amakupatsani atsogoleri kuti akutsogolereni. Afunseni atsogoleri anu asanthule mphamvu kapena kufooka kwanu kwa uzimu. Afunseni akupempherereni mmadera a utumiki wanu.

## **PEMPHANI ZOLEMBEDWA:**

Mukhonza kugwiritsa ntchito zolembedwa zina pofufuza. Mwachitsanzo, dongosolo la kayendetdedwe ka ndalama, za ku banki, macheke zimene zitha kugwira ntchito posanthula chuma chanu.

## **KONZANI MAFUNSO:**

Pemphani munthu wa banja la pafupi kapena mbale zokhuza zofooka kapena zabwino zanu za moyo wa uzimu.

## **DZIYANG'ANIRENI NOKHA:**

Mudziyang'anire nokha mmagawo ambiri a utumiki wanu. Kodi mumachita bwanji mukakhumudwa kapena muli ndi nkhwana? Kodi chipatso cha mzimu chimaonekera mmoyo wanu?

## **KUZISANTHULA KWA INU NOKHA**

Gwiritsani ntchito mndandandawu pozisanthula mwa inu nokha:

### **SANTHULANI MAUBALE ANU**

Mau a Mulungu ndi moyo wa chikhristu zimakhazikika pa maubale. Chifukwa cha ichi, mkofunikira kusanthula maubale anu ndi Mulungu komanso ndi anthu ena:

**Ndipo Yesu anati kwa iye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse.**

**Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba.**

**Ndipo laciwiri lolingana nalo ndili, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini.**

**Pa malamulo awa awiri mpokolowekapo cilamulo conse ndi aneneri (Mateyu 22:37-40)**

Santhulani maubale anu ndi zinthu izi:

## **MULUNGU:**

-Kodi ndinu wokhulupirira wobadwa mwatsopano?

-Munabatizidwapo mmadzi?

-Kodi mukuyenda mu chiyanjano ndi Mulungu? Kapena pali tchimo linalake mmoyo wanu limene mukufuna kulisaiya?

-Munabatizidwapo ndi Mzimu Woyera?

-Kodi mumawerenga Baibulo pafupipafupi?

-Kodi mungachite bwino bwanji pa makhalidwe anu ophunzira Baibulo?

-Kodi mumapemphera pafupipafupi?

-Kodi mungachite bwino bwanji moyo wanu wa pemphero?

-Kodi ndi ochichita mu chiyanjano cha mpingo?

-Kodi moyo wanu umaonetsa chipatso cha Mzimu Woyera molingana ndi Agalatiya 5:22-23?

-Kodi ndi magawo ati a moyo wanu wa uzimu sanakule, ndipo akufunika kukula?

### **WACHIKONDI WANU:**

-Kodi muli pa ubale wabwino ndi wachikondi wanu? Mumakhala bwino, kulumikizana bwino, kukhala ndi nthawi limodzi ndi zina?

-Mumapemphera, kuwerengan Mau a Mulungu ndi kupita limodzi ku mpingo? Ngati sichoncho, muchita bwanji kuti muzipanga zimenezi mu ubale wanu?

-Kodi zimene amachita bwino wachikondi wanu ndi ziti?

-Kodi zimene sachita bwino wachikondi wanu ndi ziti?

-Kodi ubale wanu umalepheretsa utumiki wanu?

-Mungachite chiyani kuti ubale wanu ndi wachikondi wanu upindule koposa kukhala cholepheretsa ku ntchito ya Mulungu?

### **WOKULEMBANI NTCHITO:**

-Kodi muli pa ubale wabwino ndi omwe anakulembani ntchito?

-Ngati sichoncho, mungakonze bwanji?

-Kodi mumawapatsa ulemu ndi kuwalemekeza?

-Kodi mumachita zinthu zonse pa ntchito yanu ngati kwa Mulungu? Onani (I Akorinto 10:31)

### **ANA ANU:**

-Kodi muli ndi ubale wabwino ndi ana anu?

-Kodi mungakonze bwanji ubale wanu ndi ana anu?

-Kodi ana anu ali ndi mwambo?

-Kodi ndi madera ati amene alibe mwambo?

-Kodi mungachite chiyani kuti akhale amwambo?

-Kodi anawo analandira Yesu ngati mpulumutsi wawo?

-Kodi mungawathandize bwanji ana anu apange chisankhochi?

-Ngati muli mtsogoleri mu mpingo, kodi muli ndi anthu amene mumawayang'anira monga zilili ku Tito 1:6 ndi I Timoteo 3:4-5? Ngati sichoncho, mungachite chiyani kuti mufikire muyesewu?

### **ANTHU ENA A PABANJA:**

-Kodi muli ndi vuto lokhala pa ubale ndi ndi anthu ena a mbanja? Ngati ndi choncho, ndi ndani komanso chifukwa chiyani?

-Mungachite chiyani kuti mukonze izi?

### **ANTHU ENA MU THUPI LA KHRISTU:**

-Kodi mukukumana ndi vuto loyanjana ndi akhristu ena amene ali mthupi la Khristu? Ngati ndi choncho, ndi ndani amene muli naye vutoli?

-Kodi mungachite chiyani kuti mubwenzeretse ubale ndi mbale kapena mlongo ameneyi? Njira zobwezeretsa maubale ndi okhulupirira ena Mbaibulo zikupezeka ku Mateyu 18:15-17.

### **OSAKHULUPIRIRA:**

-Kodi mumalumikizana ndi osakhulupirira kapena mumakhala ndo akhristu okhaokha? Simungabweretsere anthu kwa Yesu ngati simulumikizana nawo.

-Kodi mumatani kuti muwabweretsere kwa Ambuye osakhulupirira amene mumakumana nawo?

-Kodi mumakhazikitsa maubale otani ndi osakhulupirira ndi cholinga chofalisa uthenga wabwino?

-Kodi muli ndi maubale ndi okhulupirira amene sawerenga Mau komanso amaononga ubale wanu ndi Mulungu? Ngati ndi choncho, mungatani kuti mukonze zimenezi?

### **SANTHULANI NYENGO ZANU ZA KUTHUPI**

-Baibulo limatiuza kuti thupi lanu ndilo kachisi wa Mzimu wa Mulungu. Pokhala kuti thupi lanu ndi malo okhalamo Mulungu, mukuyenera kulisamalira (I Akorinto 3:16-17)

-Zochita zanu za kuthupi zimakhudza ku uzimu chifukwa munthu ali kuthupi, moyo ndi mzimu. Pamene thupi lanu silikusamalidwa, mukhoza kukhumudwa ku uzimu. Mulibe mphamvu kapena kuthekera kochita ntchito ya Mulungu.

-Kodi thupi la limalekera kwambiri?

-Kodi kapene simumalembera kwambiri?

-Kodi mumagwiritsa zoononga monga mowa, fodya ndi mankhwala ena?

-Kodi mumadya molingana ndi dongosolo lanu la ndalama kapena mene nyengo yanu ilili?

-Kodi mumachita masewera olimbitsa thupi pafupipafupi?

-Kodi muli ndi vuto la kuthupi limene limalepheretsa kutumikira Mulungu? Ngati ndi choncho, kodi mumachita chiyani? Onani zina zimene mungachite bwino pokudya zoyenera ndi kupanga masewera olimbitsa thupi. Zina Mulungu akhoza kuchiritsa.

### **SANTHULANI MUYESO WA MAPHUNZIRO ANU**

-Kodi panopa muyeso wanu wa maphunziro ndi wotani?

-Kodi mungachite chiyani kuti kukonzetso maphunziro anu kuti mupindulire ntchito ndi utumiki? Kuphunzira maphunziro a Harvestime International Institute ndi njira imodzi! Musagwe mphwayi ngati mulibe mwayi okhala ndi maphunziro a pamwamba. Yesu anasankha anthu wamba ngati asodzi ndipo anawagwiritsa ntchito mwamphamvu mu utumiki. Ngati mulibe mwayi wopitiliza maphunziro anu ndipo mukuona kuti ndi chifuniro cha Mulungu, ife tikulimbikitsani kuti mutero.

### **SANTHULANI CHUMA CHANU**

-Kodi mumapereka chakhuma pafupipafupi? (Gawo la 10 la ndalama zonse zimene mumapeza muzimpatsa Mulungu. Iyi ndi mfundo ya Mbaibulo).

- Kodi mumapereka zopereka zina kupatula chakhumi?
- Kodi chaka chatha zopereka zanu ku mpingo zinali zingati?
- Kodi mumapereka zingati ku utumiki wa mishoni?
- Kodi ndi ziti zimene mungasinthe mmachitidwe anu kuti muzipereka zambiri ku ntchito ya Mulungu?
- Kodi muli mu ngongole? Ngati ndi choncho, muchita bwanji kuti muzithetse?
- Kodi muli ndi umboni wabwino wokhudzana ndi za chuma chanu, mmene mumathandizira banja lanu ndi kulipira zina ndi zina?
- Kodi mumakhala ndi chidwi chokhala ndi chuma kapena zinthu? Kodi zimenezi zimatenga nthawi komanso mphamvu zanu zambiri?

### **SANTHULANI KUTHEKKERA KWANU KWANU KWA UZIMU**

- Kodi mumagwiritsa ntchito nthawi yanu mwa nzeru pa za uzimu ndi ntchito ya utumiki?
- Ndi ntchito ziti zimene muyenera kuzithetsa ndi cholinga choti mukhale ndi thawi yambiri yotumikira?
- Kodi mukudziwa utumiki weniweni umene Ambuye akupatsani mu thupi la Yesu?
- Kodi mukukwaniritsa panopo? Ngati sichoncho, ndi chifukwa chiyani?
- Kodi mukudziwa mphatso za uzimu zimene mwaatsidwa? Ngati sichoncho, chitani izi:

### **GAWO LOYAMBA: Badwani mwatsopano**

Mukuyenera kubadwa mwatsopano. Mphatso za uzimu zimabwera kupyolera mkubadwa mwatsopano monganso luso la kuthupi limabwera pa kubadwa mwakuthupi. Ngati simunabadwe mu thupi simungakhale ndi luso la kuthupi. Choncho ngatinso simunabadwe ku uzimu, simungapatsidwe mphatso za ku uzimu.

**Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera (Machitidwe 2:38)**

### **GAWO LACHIWIRI: Landilani ubatizo wa Mzimu Woyera.**

Malangizo a za mmene mungalandilire Mzimu Woyera aperekedwa mu phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa, *“Utumiki wa Mzimu Woyera”*

### **GAWO LACHITATU: Dziwani mphatso za uzimu.**

Mukuyenera kudziwa kuti kodi mphatso za uzimu ndi chiyani. Ngati simudziwa, zidzakhala zovuta kudziwa mphatso ya uzimu imene Mulungu wakupatsani.

### **GAWO LACHITATU: Funani mphatso ya uzimu.**

**Koma funitsitsani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu (I Akorinto 12:31)**

Tonse tili ndi mphatso ya uzimu imodzi, koma timafuna mphatso zina. Vesili likutanthauza kuti mutha kulandira mphatso imene mulibe.

### **GAWO LACHISANU: Kusanjika manja**

Mulore atsogoleri anu a uzimu akusanjikeneni manja ndi kupemphera kuti Mulungu akululireni mphatso yanu ya uzimu.

**Usanyalapse mphatsoyo iri mwa iwe, yopatsidwa kwa iwe mwa cinenero, pamodzi ndi kuika kwa manja a akulu (I Timoteo 4:14).**

Zotsatira za gawo loyamba ndi lachisanu, Mulungu akhoza kuulura mphatso yanu, koma ngati izi sizingatheke, pitilizaninso ndi magawo ena awa:

### **GAWO LACHISANU MCHIMODZI: Dziwani zokonda zanu za uzimu.**

Kodi ndi mphatso iti imene mumaifuna kuti ikhale mmoyo wanu? Kodi ndi mphatso ili imene imakubweretserani chimwemwe mukamaiganizira kapena kuigwiritsa ntchito. Kodi mumakondwera ndi chiphunzitso? Kodi mumakondwera ndi kucheleza alendo kapena kukhala ndi anthu kunyumba kwanu? Kapena mumakhudgidwa ndi kupereka ndalama zochuluka ku ntchito ya Mulungu?

### **GAWO LACHISANU MCHIWIWI: Kusanthula kwa tsogoleri wa mpingo**

Lolani astogoleri a mpingo asanthule kuthekera kwanu kwa uzimu. Kodi ndi chiyani chimene awona chokhudzana ndi utumiki wanu? Kodi akamakuonani, ndinu wotsogolera bwino, mphunzitso ndi zina? Mmaganizo mwawo kodi ndi utumiki kapena mphatso iti imene mwakhala mukuchita bwino?

### **GAWO LACHISANU MCHITATU: Santhulani utumiki wanu wakale**

Ndi utumiki uti kapena mphatso iti imene imakupatsani chimwemwe chachikulu pamene mumatumikira? Kodi ndi gawo liti limene mumachita bwino?

## **GAWO LACHISANU NDI CHINAYI: Zindikirani mphatso imene mumaganiza kuti mutha kukhala nayo**

Lembani mndandanda wa mphatso umene mumaganiza kuti mungakhale nawo. Mndandandawu wakhazikika pa:

-Chidziwitso cha mphatso mwachipeza pophonzira.

-Zimene Mulungu wakuvumbulutsirani popemphera.

-Zimene mtsogoleri wa mpingo waona mwa inu.

-Kusanthula pa kuchitachita kwanu mu utumiki umene mumkachitanso kale.

## **GAWO LA KHUMI: Onani zosowa za uzimu pamene mukukhala.**

Kodi ndi zosowa ziti zimene sizikukwaniritsidwa mdera lanu, kapena mu mpingo wanu? Kodi pali chosowa cha aphunzitsi, alaliki, atsogoleri ndi ena. Lembani zosowa zimenezi.

## **GAWO LA KHUMI NDI CHIMODZI: Kwaniritsani chosowa cha uzimu**

Fananitsani mndandanda wa zosowa za uzimu ndi mndandanda wa mphatso zimene mukhulupirira kuti Mulungu akupatsani. Kudziwa chosowa sikutanthauza kuti muli ndi mphatso imene mutha kukwaniritsa chosowacho. Koma mutha kuona kuti pamene pali chosowa cha uzimu zimalingana ndi mphatso imene mukhulupirira kuti Mulungu anakupatsani.

Dziperekeni pokwaniritsa chosowachi. Mwachtsanzo, pali chosowa cha aphunzitsi mu mpingo wanu ndipo mukhulupirira kuti muli ndi mphatso yophunzitsa. Dziperekeni pokwaniritsa mphatso imeneyo.

## **GAWO LA KHUMI NDI CHIWIRI: Santhulani utumiki wanu.**

Mutatumikira kwa nthawi ndi mphatso yanu, santhulani utumiki wanu. Kodi ndinu wamphamvu pogwiritsa ntchito mphatsoyo? Kodi imakubweretserani chimwemwe? Kodi imakhala ndi zotsatira? Nanga abua anu kapena atsogoleri amaiona mphatsoyo? Ngati ndi choncho, Mulungu wakutsogolerani kuti mudziwe dera limene mukhoza kutumikira.

## **KUGWIRITSA NTCHITO ZOSATIRA ZA KUSANTHULA**

Kusanthula kumene mwamaliza kuzakhala kopanda ntchito pokhapokha mwakugwiritsira ntchito mmoyo komanso mu utumiki wanu. “Kugwiritsa ntchito kutanthauza kuti kuchita nazo moyenera, kapena kuchita nacho chinthu.

Nthawi iliyonse imene mufuna kukwaniritsa chinthu...kuchita ntchito iliyonse ya Mulungu...mukuyenera kukhala ndi dongosolo. Mulungu ndi Mulungu wa dongosolo. Anapanga dongosolo la chilengedwe pa dziko. Kuchokera pa chiyambi cha dziko, Mulungu anapanga dondosolo lopulumutsa munthu wochimwa. Itakwana nthawi yake, anakwaniritsa dongosolo lake potumiza Yesu ku dziko kukafera anthu onse ochimwa.

Pamene Yesu amapita kukagwira ntchito mmiyoyo ya anthu, amawaitana kuti akonzekere. Anamuza wakhungu kuti akasambe mu dziwe lamadzi. Analamulira ophunzira ake kuti abweretse mikate ndi nsomba. Anamuza wolumala kuti anyamule mphasa yake.

Mukuyenera kugwirizana ndi ntchito ya Mulungu mmoyo wanu. Poonetsetsa kuti mukuchita izi, mukuyenera kukonzekera kuchita zimenezi. Pamene mugwiritsa ntchito zotsatira za kuzisanthula kwanu, mumakonzekera kugwiritsa ntchito zimene mwaphunzira zokhudza inu pobweretsa ulemerero wa Mulungu.

Gwiritsani ntchito zotsatirazi pa kuzisanthula kwanu. Kumbukirani kupempherera gawo lililonse. Mfusen Mulungu kuti avumbulutse dongosolo lake pa moyo wanu, kenako lembani dongosolo lanu mmipatayo.

### **1. DZIWANI MMENE MOYO WANU WA UZIMU ULILI:**

Onaninso kusanthula kwanu, ndipo lembani ndime mwachidule yokhudza mmene moyo wanu wa uzimu ulili. Kuphatikizanso njira za mmene moyo wanu wa uzimu ukukhuzidwira ndi maubale anu, nyengo zakunja, chuma chanu, maphunziro, mphamvu komanso kufooka kwanu.

Pangani dongosolo: Kodi mungachite chiyani kuti mugwirizane ndi Mulungu pokozanso moyo wanu wa uzimu, kukula ku uzimu ndi kukhala wokhwima?

Ndiza chita izi:

---

---

### **2. ZINDIKIRANI KUFOOKA KWANU KWA UZIMU:**

Onaninso kusanthula kwanu ndi mndandanda wa zofooka zanu za kuuzimu. Pambali pa chofooka chilichonse lembani madongosolo othana ndi zofooka:

CHOFOOKA

DONGOSOLO LANGA LOTHANA NDI KUFOOKA

---

---

---

---



**3. ZINDIKIRANI MPHAMVU ZANU ZA KU UZIMU:**

Onaninso kusanthula kwanu ndi mndandanda wa mphamvu zanu za kuuzimu. Pambali pa mphamvu zanu lembani madongosolo ogwiritsa ntchito mphamvu zanu ku ulemerero wa Mulungu:

MPHAMVU DONGOSOLO LANGA LOGWIRITSA NTCHITO MPHAMVU KU ULEMERERO WA MULUNGU

---

---

**4. ZINDIKIRANI MPHATSO ZANU YA UZIMU:**

Onaninso zotsatira za kusanthula mphamvu zanu za uzimu. Lembani mphatso za uzimu zimene mukhulupirira kuti muli nazo. Pa mphatso iliyonse, lembani dongosolo la mmene muigwiritsire ntchito ku ulemerero wa Mulungu.

MPHATSO YA UZIMU

MMENE MUGWIRITSIRE NTCHITO

---

---

**5. DZIWANI MALO ANU A UTUMIKI:**

Santhulaninso moyo wanu onse. Mwapemphero onani komanso malizani chiganizo ichi:

Ndikhulupirira kuti malo anga a utumiki mu thupi la Khristu ndi:

---

---

**6. KONZANI DONGOSOLO LOKWANIRITSA UTUMIKI WANU:**

Kodi muyamba bwanji kukwaniritsa utumiki wanu umene mukhulupirira kuti Mulungu anakupatsani? Werengani chaputala cha 11 kuti chikuthandizeni kukonza dongosololi.

---

---

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera muntima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “kusanthula nyengo za munthu.”

---

---

3. Kodi kuzisanthula kwa munthu kumakhudza zinthu ngati ziti?

---

---

4. Lembani zolinga zisanu ndi chimodzi za kuzisanthula kwa munthu.

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani nkhani ya Samson mu Oweruza 13-16. Anali munthu amene akanapindula ku kuzisanthula kwake. Sanazindikire mmene uzimu wake unalili pamene anamuka kukathira nkondo ndi Afilisti. Samson akanazisanthula yenkha...

-Ndi mavuto ati a uzimu amene akanapezeka pa kuzisanthula kwake?

-Kodi akanabweretsa kusintha kumene kukanakhudza tsogolo la moyo wake?

-Kodi ndi kusintha kuti kumene akanakupanga?

2. Werengani Masalmo 51 pamene Davide akuzisanthula moyo wake wa uzimu atachimwa ndi Betisheba. Kuchokera pa zimene mwawerenga, yankhani mafunso awa:

-Kodi moyo wa uzimu wa Davide unali bwanji pamene amalemba chaputalachi?

-Kodi Davide anachitapo chiyani za tchimo lake?

-Kodi Davide anamfunsa chiyani Mulungu?

3. Werengani nkhani ya Belisazara mu Danieli 5. Apa pali munthu wina amene akanapindula pa kudzisanthula kwake.

-Kodi moyo wake wa uzimu unali wotani? (Onani 22-23)

-Kodi Mulungu anachita chiyani za zimenezi? (Onani 25-28)

-Belisazara akanakhala kuti amadziwa za mmene moyo wake wa uzimu unalili, ndi kusintha kuti kumene kukanakhalapo mmoyo wake kumene kukanalepheretsa chiweruzo cha Mulungu.

4. Werengani nkhani ya Nebukadinezara mu Danieli 4. Anali munthu amene anasanthula nyengo zake molakwika ndipo anazunzika chifukwa cha zimenezi.

-Fananitsani za mmene nyengo zake zinalili mu vesi 29-30 kufika 34-35. Kodi akusiyana bwanji?

-Kodi chinachitika ndi chiyani kuti adziwe za zenizeni za moyo wake wa uzimu? Onani 31-33

-Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Nebukadinezara anazindikira moyo wake bwinobwino ndi kudziwa kuti zonse zimachokera kwa Mulungu? (Onani 34-37)

5. Mu Luka 12:16-21 ndi nkhani ya mwini chuma amene sanasamale za uzimu mmoyo wake. Moyo wake unakhazikika pa zinthu za kuthupi za dzikoli osati pa zosatha za mtengo wapatali.
6. Werengani Luka 18:9-14. Fananisani kuzisanthula kwa Mfalisi ndi wochimwa uja. Kodi kusanthula kolondola kunali kuti?
7. Buku la Oweruza Mbaibulo limakamba za mafumu ambiri amene analamulira anthu a Mulungu. Ena anali abwino ena anali oyipa. Werengani buku la Oweruza ndi kusanthula mfumu iliyonse. Kodi zomwe anachita bwino ndi ziti, nanga zimene sanachite bwino zinali ziti? Kodi akanapindula bwanji pa kudzisanthula kwawo? Kodi ndi kusintha kuti kumene akanachita kumene kukanakhudza tsogolo lawo?
8. Werengani buku la Numeri 12. Miliyamu ndi Aroni sanasanthule bwino za uzimu wawo pamaso pa Mulungu. Kodi zinachitika ndi chiyani ngati zotsatira?
9. Kora ndi amene amamutsata analakwitsanso mu Numeri 16. Kodi zinzchitika ndi chiyani ngati ndi zotsatira pa kusanthula bwino kwawo?
10. Werengani I Mafumu 19. Kodi Eliya anasanthula bwanji nyengo zake panthawi imeneyi? Kodi Mulungu anakonza bwanji kusanthulako?

## CHAPUTALA CHA 6

### KUSANTHULA GULU LA ANTHU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “gulu la anthu.”
- Kulongosola zimene zimakhudza kusanthula gulu la anthu.
- Kudziwa zolinga za kusanthula gulu la anthu.
- Kusanthula gulu la anthu.
- Kugwiritsa ntchito kusanthula kwanu pa kufalisa uthenga wabwino.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo palibe colengedwa cosaonekera pamaso pace, koma zonse zikhala za pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pace pa iye amene ticita naye (Ahebri 4:13)**

#### MAWU OYAMBA

Mu chaputala chomaliza, mwazisanthula nokha pokonzekera utumiki. Chaputala ichi chikuyamba ndi mndandanda wa maphunziro amene amalongosola za mmene mungasanthulire nyengo zosiyana imene mumatumikira.

Mu chaputala ichi, muphunzira za mmene mungasanthulire gulu la anthu. Muphunzira za mmene mungasanthulire madera, mitundu, zigawo za dziko zimene zimapangidwa ndi anthu a magulu osiyana.

#### GULU LA ANTHU

Anthu a mdzikoli anagawikana ndi zotchinga zambiri zimene zimakhudza kufala kwa Uthenga Wabwino. Pali chotchinga cha malo monga mapiri, Nyanja, ndi zigwa. Komanso pali kugawanika kwa malire a maboma amene amasiyanitsa maiko.

Komanso anthu amasiyana chifukwa cha zikhalidwe. Mwachidule, chikhalidwe ndi makhalidwe a anthu osiyanasiyana amene ali mdziko. Chikhalidwe ndi monga chiyankhulo, zikhulupiro, miyambo, makonda, mitundu ya anthu ndi zina.

Kusiyana kwa zikhalidwe kwabweretsa magulu a anthu mdziko. Gulu la anthu ndi gulu lililonse la anthu amene ali mu moyo wa ukwati kapena ubale mdera kapena mdziko. Mwachitsanzo, gulu la anthu ndi anthu a padera a mtundu umodzi, kapena mbumba imodzi.

Pamene Yesu anawauza ophunzira ake kuti akalalike uthenga wabwino kwa amitundu yonse, anagwiritsa ntchito mawu oti “mitundu yonse” amene mu chigiriki ndi “ethnos.” Mtunda umakhala ndi anthu ambiri.

Sizokwanira kungofikira mtundu wa anthu ndi uthenga wabwino. Mukuyenera kuonetsetsa kuti gulu lililonse la anthu mdera lamva za uthenga wabwino. Pamene izi zachitika, dziko lonse lidzalalikidwa. Yesu analamulira kuti uthenga wabwino ufikire kwa anthu onse. Ngati mukufuna kukwaniritsa lamulo ili, mukuyenera kudziwa magulu a anthu amene muwafikire, kupanga dongosolo ndi kuyamba kuchitapo kanthu.

### **KUSANTHULA GULU LA ANTHU**

Pamene mukusanthula gulu la anthu, mumaphunzira gulu lapaderadera la anthu amene ali gawo limodzi ndi mtundu, kapena mbumba. Mumawaphunzira mmene amakhallira, zikhalidwe zawo, utsogoleri wawo ndi uzimu wawo. Komanso mumasanthula mphamvu zimene zimachokera kunja kwa magulu awo zimene zimakhudza pa kulandira kwawo kwa uthenga wabwino.

### **CHOLINGA CHOSANTHULA GULU LA ANTHU**

Cholinga cha maphunziro anu ndiko kufikira gulu la anthu ndi uthenga wabwino. Ndi kafukufuku wa cholinga cha kulalikira, osati kungofufuza chabe. Samalisani kuti nthawi yanu sikutha mkusanthula basin di kulephera kukwaniritsa cholinga chimene mukuyenera kuchita muphunzirolo.

Phunziro lanu lokhudza zikhalidwe za anthu lidzakuthandizani kuona mmene mungawafikire anthu. Mukhoza kulalikira uthenga wabwino potsindika zimene mwaphunzira zokhudza chikhalidwe chawo.

Mwachitsanzo, Paulo pamene amatumikira kwa Ayuda, amatsindika za chikhalidwe chawo ndi Yesu amene anali mbumba yawo ngati Mesiya wa Israyeli. Pamene amatumikira kwa amitundu, amatsindika madera osiyana a uthenga wabwino.

Zitsanzo zina ndi monga buku la Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane. Onsewa amakhazikika pa madera osiyana a uthenga wabwino amene amagwirizana ndi zikhalidwe zawo zimenenso analemba.

Pamene mugwiritsa ntchito zikhalidwe za anthu ngati khwerero lofalisa uthenga wabwino, uthengawo umalandilidwa. Kumvetsa zikhalidwe kukhoza kukupatsani mafungulo a ku uzimu amene adzatsekula makomo a anthu ena. Mumasanthula gulu la anthu poyankha mafunso awa:

### **NDI ANTHU ATI AMENE AYENERA KUFIKILIDWA?**

Ndi ndani amene makamaka tifuna kuti tiwafikire ndi uthenga wabwino. Kodi nanga gulu la anthu limapezeka kuti?

### **KODI ALI NGATI NDANI?**

Kodi ndi ziti zimene mufuna kudziwa zokhudza miyambo, mavuto, makhalidwe, ndi uzimu wawo pofuna kuwafikira?

### **NDI NDANI AMENE AWAFIKIRE?**

Kodi anthuwa atha kufikilidwa mosavuta ndi wamamuna kapena wamkazi, kudzera mmodzi wa anthu awo kapena wakunja? Kodi ndi zomuyenereza ziti zimene munthuyo ayenera kukhala nazo kuti athe kuwafikira? Mulungu ali ndi nthumwi zapaderadera lofikira magulu a anthu ake apaderadera. Paulo anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuti afikira amitundu. Petro anagwiritsidwa ntchito kufikira Ayuda.

### **KODI ANGAFIKILIDWE BWANJI?**

Ndi njira ziti zimene tingagwiritse ntchito kuwafikira anthuwa? Ndi ziti zimene zili zothandiza? Mayankho a mafunso awa adzakuthandizani kudziwa ntchito yanu yofikira anthu ndi kukonza dongosolo lowafikira anthu ndi uthenga wabwino.

## **MMENE TINGADZIWIWE ZINTHU**

Umu ndi mmene mungadziwire zinthu posanthula:

### **PEMPHERO:**

Mfuseni Mulungu avumbulutse zimene mukufuna kudziwa zokhudza gulu la anthu ndipo akuthandizeni kufikira anthuwo ndi uthenga wabwino. Mulungu ali ndi chidziwitso cha umulungu cha pa anthu ake (Ahebri 4:13).

### **PHUNZIRANI ZINTHU ZOLEMBEDWA:**

Phunzirani mabuku kapena zinthu zolembedwa zokhudza gulu la anthuwo. Mndandanda wa zomwe mungadziweko zinthu zili kumapeto kwa bukuli.

### **KUONETSETSA:**

Inuyo ngati munthu, onetsetsani gulu la anthulo mwa inu nokha.

## **MAFUNSO:**

Funsani mafunso kwa anthu amene ndi atsogoleri kapena amene ali mu gulu limene mukuliphunzira. Ngati kuli okhuylupirira amene akutumikira kale anthu kumeneko, afunsemi mafunso kuti mudziwe zimene aphunzira zokhudza anthuwo. Ena mwa mafunso akupezeka kumapeto kwa bukuli.

Gwiritsani ntchito magawowa posanthula gulu la a nthu. Simungathe kuyankha mafunso onse okhudza gulu la anthu, koma yankhani okhawo amene akhodza kukudziwitsani zinthu.

### **NDI ANTHU ANJI AMENE MUKUFUNA KUWAFIKIRA?**

1. Ndi anthu a mtundu wanji amene mukufuna kuwafikira?
2. Ndi chiyani chimawapanga kukhala “gulu la anthu”? akhoza kukhala ndi zinthu zina zofanana. Onani izi zimene zikupezeka ku gulu limene mukuliphunzira:
  - Chiyankhulo chofanana
  - Utsogoleri wofanana
  - Mtundu wofanana
  - Zikhulupiriro zofanana
  - Maphunziro ofanana
  - Madera okhala ofanana
  - Zokonda zofanana
  - Mavuto ofanana
  - Muyeso wa za chuma wa mmagawo; osauka, apakatipakati, ndi olemera.
  - Misinkhu yofanana.
  - Za umoyo zapaderadera

Kodi ndi zinthu zina ziti zimene zikhoza kufotokoza za gulu la anthuwo?

3. Kodi ndi anthu angati amene ali mgululo? Yerekezani za chiwerengero chawo ngati chiwerengero chenicheni simuchidziwa. Izi zizakuthandizani kudziwa kuchuluka kwa anthu amene mufuna kuti akafalise uthenga wabwino.

### **KUSANTHULA MADERA**

1. Ndi madera ati amene kumakhala anthu ochuluka?
2. Ndi madera ati amene anthuwa amapezekako?  
(Poyankha mafunsowa dziwani anthuwo bwinobwino, osati ngati anthu onse ku Indiya. Anthu ake ati? Mwachitsanzo ku Malawi, kuli anthu ena apaderadera mmudzi? Njira zimene mugwiritsira ntchito kufikira anthuwa kumasiyana.
3. Jambulani mulozo wa dziko ndi kuika zizindikiro za malo a magulu a anthu amene mufuna kuwafikira.



4. Tengani kapena lembani mapu a deralo limene anthu akukhalamo. Yambani kupemphera pa mapuwo kuti Mulungu afikire anthu amene mwaika zizindikiro.
5. Ndi zinthu ziti za mmadera zimene zimatcinga kufala kwa uthenga wabwino? Mwachitsanzo, kodi malo amene anthu akukhalawo ndi osafikilika?
6. Ndi zinthu ziti za mmadera zimene zingathandizire kufalitsa uthenga wabwino? Mwachitsanzo, kodi kuli misewu imene anthu amapita kochita malonda kapena kumene mungazaleko mipingo?
7. Kodi malowa ali ndi nthawi kapena nyengo imene mukhoza kuyenderako mkufikira anthu? Mwachitsanzo, kodi kumaloko ndi kotheka kuyendera nthawi ya mvula kapena nthawi ya dzuwa? Pokhapokha Mulungu akutsogolereni, malowo atha kukhala ovuta kufikako.
8. Fufuzani mbiri ya zinthu zokhudza izi zimene ndi zotchinga kapena zothandizira kuti mufikire anthu mmadera awo:
  - Mtunda wake wokafika mu mizinda:
  - Mtunda kwa ku mzinda waukulu wa boma:
  - Mtunda wa ku malo ogulitsira mafuta a galimoto:
  - Mtunda woyandikira ku malo okonza magalimoto:

### **KODI ALI NGATI NDANI?**

#### **KUSANTHULA MAUBALE AWO:**

1. Kodi makhalidwe a anthuwa mmagulu awo ndi otani? Mwachitsanzo, ndi mamuna kapena mkazi mmodzi ndi ana awo kapena akazi ndi ambiri? Kodi anthuwo amakhala mosiyana ngati mbanja monga atate, amayi ndi ana? Kapena amakhala ndi anthu ena owonjezera monga azakhali, malume, agogo ndi ena?
2. Kodi wotsogolera mnyumaba amakhala ndani? Kodi ndi atate, amayi, kapena apongozi ndi ena? Mukhoza kugwiritsa ntchito maubale a mbanja ngati khwerero lotengera uthenga wabwino kwa ena. Mwachitsanzo, chikhalidwe china atate amakhala mtsogolera wa mnyumba, ndiye kuti atatewa amakhala woyamba kuwafikira ndi uthenga wabwino. Banja lake lizibwera pambuyo iwo atatha kulandira kale.
3. Nanga atsogolera a mmudzi ndi ndani? Kodi mfumu ya anthu ndi ndani, ya abale, kapena ya mtundu. Nanga atsogolera amakhala kuti; mmudzi kapena mtawuni. Mukawafikira iwowa ndi uthenga wabwino, ena adzalandira mosavuta.
4. Kodi amapanga ziganizo mmudzi ndi ndani nanga ziganizo zimapangidwa bwanji? Mukuyenera kudziwa amene amapanga ziganizo ndi mmene ziganizo zimapangidwira ngati mukufuna kukhala ndi chilolezo cholowa mderalo kukafalitsa uthenga wabwino.
5. Kodi ndi ziti zimene amakangalika nazo mmudzi? Kodi amakhala ndi chidwi cha zinthu ziti? Mukhoza kutsindika zimenezi pamene mukufalitsa uthenga wabwino. Onetsetsani kuti zikugwirizana ndi uthenga wabwino.

6. Kodi anthu “akunja” amawalandira bwanji? Anthu amene sakhala kuderako. Kudziwa izi kumathandiza kukonzekara kulandilidwa kapena ayi pamene mukufuna kukafalisa uthenga wabwino.
7. Kodi muyeso wa anthu ndi otani? Pali anthu osauka, apakati ndi pakati kapena olemera. Ngati anthu ndi apansi amene ali ndi zosowa zambiri, ndiye kuti mukonzeke kutumikiranso zosowa zawo pamene mukufalisa uthenga wabwino.
8. Kodi anthuwo amapanga chiyani pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku? Ganizirani za mmene mungagwiritsire ntchito zimene amapanga kuti mukhale nawo chifupi. Mwachitsanzo mukhoza kuchita maphunziro a Baibulo kumene anthuwo amagwira ntchito kapena kugawana njira zochitira ulimi ndi alimi ndi zina.
9. Kodi ndi ndani ameneali ndi ulamuliro pa zachuma kapena katundu wa mmudzimo kapena mbanja. Amenewa azafunika pamene mufuna kudzamanga mpingo kapena kufuna thandizo la chuma kuderako ndi cholinga chofalitsa uthenga wabwino.

### **KUSANTHULA CHIKHALIDWE:**

Phunzirani machitidwe a zikhalidwe zimene zimakhudza polalikira uthenga wabwino. Izi ndi zina mwa izo:

1. Zikhulupiriro ndi zimene amazilemekeza:
  - a. Kodi ndi makhalidwe ati, zikhulupiriro za anthu zimene zingawathandize kumvetsetsa uthenga wabwino? Mwachitsanzo, ngati anthu amalemekeza banja, uthenga wabwino uyenera kusindika pa banja.
  - b. Kodi ndi zikhulupiriro, kapena makhalidwe ati amene atha kuwalepheretsa kumva uthenga wabwino?

#### 2. Makhalidwe awo:

Kodi pali makhalidwe ena amene samaloledwa Mbaibulo? Ngati ndi choncho, kodi ndi ati? Makhalidwe si olakwika pokhala kuti amasiyana ndi mmene mumachitira zinthu zanu. Makhalidwewa ndi olakwika ngati amasemphana ndi Mau a Mulungu. Makhalidwe ochimwa amayenera kuthana nawo pamene mufikira anthu ndi uthenga wabwino. Makhalidwe ena si ofunikira kusintha. Anthu sayenera kuvomereza makhalidwe anu ndi cholinga chakuti alandire uthenga wabwino.

#### 3. Zosowa:

- a. Kodi ndi mavuto ati amene amakumana ndi anthu ambiri, malinganliro awo, zimene zimawakhudza, ndi kudzipereka kwawo? Ndi ziti apa zimene ndi zosowa zawo zofunikira?
  - Kusowa kwa chakudya.
  - Kusowa kwa malo a zaumoyo.
  - Maphunziro operewera.

- Mayendedwe ovuta.
- kulumikizana kovuta.
- Mavuto a zautsogoleri.
- Mavuto a zachuma.

4. Maphunziro:

Ndi muyeso uti wa maphunziro? Ndi muyeso uti wa anthu ophunzira? Ndi anthu angati amene amadziwa kulemba ndi kuwerenga? Ndi zofunika kudziwa izi chifukwa simuzakonza uthenga wanu wabwino potengera zolemba za anthu zimene sadziwa kulemba ndi kuwerenga.

5. Kulumikizana:

- a. Ndi chiyankhulo chiti chimene ndi choyenera kulalikira uthenga wabwino? Kodi mukufuna mufikire gulu la anthu lalikulu koyamba, sankhani koyamba chiyankhulo chimene anthu amalankhula.
- b. Kodi ndi njira iti imene anthu amalumikizilana? Kodi ndi mmagulu awo kapena maubale awo? Kapena mbanja lawo. Gulu lililonse lili ndi njira yawo imene amalumikizirana imene imakhala yofunikira.
- c. Kodi anthuwa angafikilidwe kudzera:
  - Mawailesi?
  - Nyuzi pepala?
  - Makanema?
  - Ma lamyia?
- d. Kodi ndi njira iti imene amalumikizana kwambiri?

**MPHAMVU ZA KUNJA:**

1. Kodi ndi kusintha kuti kumene kukuchitika mmagulu a zautsogoleri kapena kunjia kwa dera?
2. Kodi kusinthaku kungathandize kufalitsa uthenga wabwino?
3. Kodi pali kuletsa kwina kwa malamulo a boma pa kulalikira uthenga wabwino? Ngati ndi choncho ndi ziti?
4. Ndi nira ziti zimene zingathandandize kufikira anthuwa popanda kusemphana ndi malamulowa?
5. Ndi magulu kapena madongosolo ati amane amatsutsana ndi kufalitsa uthenga wabwino kwa maguluwa? Ndi chifukwa chiyani?

Musalole kuti malamulo kapena zoletsa kukulepheretsani kutumikira kwa anthu amene Mulungu wakupatsani. Ngati simukwanitsa kuwafikira mu njira zina, gwiritsani ntchito njira zina.

### **KUSANTHULA UTSOGOLERI:**

1. Longosolani mwachidula za utsogoleri wawo wa anthuwa.
2. Ndi magulu ati a utsogoleri amene amaletsa kufala kwa uthenga wabwino?
3. Ndi magulu ati a utsogoleri amene amapititsa patsogolo uthenga wabwino?
4. Kodi ndi malamulo ati a boma amene amaletsa utumiki kwa anthuwa?
5. Kodi ndi malamulo ati a anthu amene amathandizira utumiki kwa anthuwa?
6. Kodi ndi atsogoleri ati amene ndi otchuka kwa anthuwa? Mukhoza kuyesa kucheza nawo ndi cholnga choti mupedze mwaayi wa kuchitako utumiki.

### **KUSANTHULA UZIMU:**

1. Kodi ndi magulu ati a chipembedzo amene akupezeka kwa anthuwa?
2. Nanga ndi anthu angati amene amatsatira zipembedzo?
3. Ndi ziti zimene sizimawasangalasa ndi zochitika mu chipembedzo chawocho?  
Mwachitsanzo masenga amene sachilitsa matenda ena ndi zina. Mukhoza kuwafikira ndi uthenga wabwino anthu awa amene ndi osakhutisidwa.
4. Kodi makhalidwe a chipembedzo akupita patsogolo kapena akubwerera mmbuyo kapena akupita patsogolo?
5. Kodi zipembedzo zawo zili ndi malemba olembedwa? Mwachitsanzo asilamu ali ndi Korani. Ngati ndi choncho kodi mungafikire bwanji ndi uthenga wabwino. Izi zingatheke kwa ena koma kwa enanso sizingatheke.
6. Kodi malingaliro a anthuwa pa kusintha kwa chipembedzo ndo otani? Yankho ku funsoli lizakukonzekerani ku mkangano wa zipembedzo umene muzakumane nawo.
7. Yankhani mafunsowa okhudza chidziwitso cha Chikhulupiriro cha chikhristu.  
Mayankhowa akuthandizani kudziwa poyambira kufalitsa uthenga wanu wabwino:

Kodi malingaliro a anthuwa ndo otani okhudza...

### **Mulungu:**

- amakhulupirira kuti Mulungu alipo.
- amakana kupezeka kwa Mulungu.
- amadziwa za Mulungu mmodzi wopezeka Mbaibulo.
- sadiwa za Mulungu za Mulungu mmodzi.
- amadziwa za Mulungu mmodzi amene ndi osiyana kwa Iye mwini.
- amadziwa za Mulungu mmodzi amene Sali pachiyanjano kwa Iye.

### **Yesu Khristu:**

- amakhulupirira kuti Yesu alipo.
- amakana kuti Yesu alipo.
- amadziwa kuti Yesu anafera machimo awo.
- samadziwa kuti Yesu anafera machimo awo.

- amadziwa za Yesu koma amachita zosemphana.
- amadziwa za Yesu koma ali naye pa udani.

Mzimu Woyera:

- amakhulupirira kuti Mzimu Woyera alipo.
- amakana za kupezeka kwa Mzimu Woyera.
- sanamvepo za Mzimu Woyera.
- samamvetsa za utumiki wa Mzimu Woyera.
- amamvetsa za utumiki wa Mzimu Woyera koma mosiyana kwa Iye.
- amamvetsa za utumiki wa Mzimu Woyera koma Sali pa chiyanjano ndi Iye.

Uthenga wabwino:

- samadziwa za uthenga wabwino.
- ali ndi chidziwitso cha uthenga wabwino.
- amadziwa choonadi cha uthenga wabwino.
- amamvetsa kuti ndi zofunika kuchitapo kanthu mwa okha pa uthenga wabwino.
- amazindikira chosowa chawo cha uthenga wabwino.
- anavomereza uthenga wabwino.

Baibulo:

- sanamvepo zokhudzana ndi Baibulo.
- amadziwa kuti Baibulo lilipo.
- amakhulupirira kuti ndi Mau a Mulungu.
- Sali pa chiyanjano ndi Mau a Mulungu.
- amachita mosiyana ndi Baibulo.

Kodi tanthauzo la malemba lili motani molingana ndi chiyankhulo chimene ndi choyenera kufikira anthu ndi uthenga wabwino? Ndi gawo liti la malemba limene lasala kutanthauziridwa mu chiyankhulo chawo?

Chipangano Chatsopano:

Chipangano Chakale:

Akhristu:

Kodi amawadziwa bwanji akhristu?

-Sanamvepo za akhristu.

- Anamvapo, koma sanakumanepo ndi mmodzi.
- Anakumanapo ndi akhristu ena.
- Ali ndi okhulupirira ena amene ndi owona pakati pawo

8. Ngati muli akhristu mu gulu la anthuli, yankhani mafunso awa:
  - Ndi anthu angati mugululi amene amazitchula kuti ndi akhristu?
  - Ndi anthu angati amene anakhalapo mu chiyanjano cha okhulupirira pa mpingo?
  - Ndi angati amene ali ochitachita kufalitsa uthenga wabwino?
  - Ndi angati amene anakhalapo akhristu koma anasiya kumtsata Yesu?
  - Ndi zifukwa ziti zimene zinawapangotsa kuti abwerere mbuyo?
  - Kodi ndi akhristu ati amene ali olimbikira mgululi?
  - Kodi alipo akhristu amene amagwira ntchito zina koma amafalitsa uthenga wabwino?
9. Mwachidule, kodi mukhulupirira kuti ino ndi nthawi yofesa uthenga wabwino pakati pa anthuwa mu nthawi yokolola? Choncho ogwira ntchito ambir akufunika pamene dera lapsa pa zokolola za ku uzimu.
10. Ndi mpingo uti kapena umishoni wa mpingo umene wayesedwa ndi kulephera? Mukuganiza kuti zimene zinalepheretsa ndi chiyani? Mukhoza kuphunzira ku zolakwa za ena kenako osabwerezanso zolakwa zomwezo.
11. Ndi mpingo kapena umishoni uti wa mpingo umene ukuchita bwino mmadera amene anthu ambiri ali komweko. Tengani mayina komanso kumene amakhala.
12. Ndi ati amene akadali amphamvu? Nanga ndi chifukwa chiyani ali amphamvu? Mukhonza kuphunzira za chipambano chawo. Mungakondenso mukuyanjana nawo limodzi pofalitsa uthenga wabwino kwa anthuwa. Kodi mungayanjane nawo bwanji pofuna kufalitsa uthenga wabwino kwa anthuwa?
13. Ngati pa mkhristu amene akuchitira umboni, kodi akuchitira mu chiyankhulo chanji? Mukhoza kutsogozedwa kufikira anthuwa amene amayankhula ziyankhulo zosiyana ndipo sakhonzanso kufikilidwa ndi akhristu amene alipo.
14. Kodi ndi mautumiki ati a chikhristu amene akupezeka pakati pa anthuwa? Mwachitsanzo kodi pali kale dongosolo la chakudya kwa anthu anjala limene cholinga chake ndi kufalisa uthenga wabwino, koma osabwereza zochita. Cholinga chanu ndi kufikira osafikilidwa ndi kuonjezera ntchito yofikira anthuwa osabwereza kapena kupanga mpikisano ndi mautumiki ena.

15. Kodi malingaliro a anthuwa ku umishoni wa mpingo ndi otani?

- Audani
- Osiyana
- Aubale

16. Ngati muli mipingo yoona ya uthenga wabwino kwa anthuwa, yankhani mafunsowa:

- Ndi mipingo ingati yoona imene inakhazikitsidwa pakati pa anthuwa?
- Kodi ikukula mwachangu motani?
- Ndi zovuta ziti zimene akukumana nazo nanga ndi chifukwa chiyani?
- Ndi ziti zimene akuchita bwino, nanga ndi chifukwa chiyani?
- Kodi pali chosowa chodzala mipingo yambiri?

17. Ngati palibe akhristu amene amachitira umboni pakati pa anthu amene mukuwaphunzirawa, kodi kapena panali magulu ena amene a chikhristu amene anawafikirapo anthuwa? Mukhonza kuphunzira pa zimene anachita kwa magulu omwewo amene mukuwaphunzira.

18. Kodi mungadziwe za maukulu ndi maulamuliro a mphamvu za Satana amene akupezeka ku magulu a anthuwa? Baibulo limaphunzitsa kuti pali mphamvu zina zimene zimagwira ntchito mmagulu a anthuwa osiyanasiyana ndi kumadera osiyana. Onani Danieli 10. Makamaka vesi 13. Komanso Aefeso 6:10-17.

Pemphero lidzaululu maukulu komanso maulamuliro a mphamvu za satana amene amagwira ntchito. Nthawi zina ndi bwino kuonetsetsa ndi kuwaphunzira anthu a mderawa, magulu awo. Zimenezi zimathandiza kudziwa mphamvu za satana zopezeka kumaderako.

Mwachitsanzo, malo ena kwa azungu aliko anthu amene amagonana amuna okhaokha. Ndi zosavuta kudziwa pakungoona mzimu umene ukulamulira wa kugonana kwa amuna okhaokha kwa anthu a gululi opezeka kumizindaku. Mzinda wina unagundika chifukwa chofuna golide. Mzimu wa dyera ndi umene umatenga malo kumaderako. Pamene mwazindikira mizimu kumaderako, mukuyenera kuimanga mu pemphero ndi kumasula mphamvu ya Mzimu Woyera kuti igwire ntchito mwa anthuwa. Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “*Ndondomeko za Mzimu*” buku la Nkhondo ya Uzimu limene limaonjezera maphunzirowa.

### **NDI NDANI AMENE AWAFIKIRA?**

Ndi ndani amene awafikire anthuwa? Ndi ndani amene akhoza kulankhula chiyankhulo chawo? Ndi ndani amene akhoza kulandilidwa mu chikhalidwe ndi maubale awo? Gwiritsani ntchito mfundo zimene mwapeza zokhudza chikhalidwe ndi maubale awo zimene zikuthandizani. Komanso pezani zina kwa akhristu amene anafikako kale ndi kuchita bwino kapena kulephera. Amene anagwiritsa ntchito pa kupambana kapena kulephera kwawo.

Aliyense amene afuna kuwafikira ndi uthenga wabwino ayenera...

-Akhale wokhulupirira amene ali ndi makhalidwe, malingaliro a chikristu.

-Akhale ndi moyo wapemphero ndi wowerenga Baibulo.

-Akhale ndi mphatso za mzimu woyera zimene zimagwira ntchito munjira zoyenera kuthandiza anthu.

-Azipezeka: Kuthekera mkopanda ntchito kopanda kupezeka. Kodi munthuyu ndi wofuna ndi wokonzeka kupita?

-Akhale wokhala bwino mthupi la khristu. Wofuna kuyanjana ndi ziwalo zina ndi cholinga chofuna kufalisa uthenga wabwino.

-Akhale woitanidwa ndi Mulungu kutumikira anthu. Mulungu amaitana anthu kuti akatumikire magulu, monga mmene anamuitanira Paulo kutumikira anthu amitundu ndi Petro anthu achiyuda.

-Akhale wokonzeka bwino kuthupi, ku uzimu, maphunziro kuti afikire magulu a anthu. Kumbukirani kuti Gidione anachepetsa chiwerengero cha asilikali kukhala ochepe amane anakonzekeretsedwa.

### **KODI AFIKILIDWA MOTANI?**

Kodi anthuwa angafikilidwe bwanji? Nanga ndi njira ziti zimene zigwiritsidwe ntchito? Poyankha funsoli, gwiritsani ntchito zimene mwaphunzira zokhudza makhalidwe awo ndi mabale awo. Mutenge njira zokhazo zimene zifikira zosowa zawo. Gwiritsani ntchito njira zabwino za kulumikizana. Onetsetsani njirazo ndi zochokera Mbaibulo. Musagwiritse ntchito njira zimene ndi zotsutsana ndi mfundo za Mbaibulo. Izi ndi zina mwa njira zimene zinagwiritsidwapo ntchito ngati gawo limodzi lochitira utumiki mmadera ambiri padziko lapansi. Kodi ndi njira ziti zimene zingathandize pofikira anthu a maguluwa?

Mawailesi

Makanema

Zolembe za chikristu

Maphunziro a Baibulo

Misonkhano ya maimbidwe

Maphunziro oyendera

Masewero

Ndondomeko zogawa zakudya, zaulimi ndi za umoyo

Mautumiki a akundende

Misonkhano ya pamtetete

Kuyenda khomo ndi khomo

Sukulu za maphunziro a Baibulo

Utumiki wa kwa olumala, okalamba, odwala, amasiye ndi omwe ena.



Mutantha kudziwa njira mwa pemphero ndi kusanthula bwino, dzifunsemi funso ili: ndi zotsutsa ziti zochokera kwa anthuwa kapene kwina zimene zingalimbane ndi njirazi? Kodi mungalimbane bwanji ndi zotsutsanazi?

### **PANGANI DONGOSOLO**

Kusanthula kumene mwaphunziraku, kukhala kosathandiza pokhapokha muthaphunzira anthu amene mukukawatumikira. Anthu sangafikireidwe pongophunzira chabe. Mukuyenera kupanga dongosolo lowafikira ndi uthenga wabwino. Mu chaputala chomalizachi munapanga dongosolo lanu la utumiki wofikira anthu, madera, mitundu ndi zigawo za dziko. Chaputala cha 11, *“Ndongomekoza Dongosolo,”* likuthandizani.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzola mawu oti, “gulu la anthu.”

---

---

3. Kodi kusanthula gulu la anthu kumafuna chiyani?

---

---

4. Kodi zolinga za kusanthula gulu la anthu ndi chiyani?

---

---

5. Ngati gawo limodzi lophunzira phunziroli, kodi munamalizitsa kusanthula kwa gulu la anthu?

---

6. Kodi mwapangapo dongosolo limene mwaphunzira lokafikira gulu la anthu ndi uthenga wabwino?

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Werengani buku la Hoseya chaputala cha 7 chmene ndi kusanthula kwa Mulungu kwa uzimu wa magulu a anthu a Efraimu ndi Samariya amene analinso gawo limodzi la mtundu wa Israyeli. Anthuwa samadziwa nyengo yawo yeniyeni ya uzimu (Vesi 9). Tsitsi la imvi ku uzimu ndi chizindikiro cha kulowa pansu kwa moyo wa uzimu kumene kumabweretsa imfa yak u uzimu.

Mu dziko lathuli kukhala ndi tsitsi la imvi ndi chinthu china, komanso ndi chinthu china kudziwa kuti uli ndi tsitsi la imvi. Ndi zosiyana pa chilengedwe kwa munthu kusadziwa kuti ali ndi imvi. Vuto la Mulungu ndi anthu ake siloti ali ndi tsitsi la imvi, koma kuti ali nawo koma sadziwa. Kukhala ndi tsitsi la imvi koma osadziwa ndi ndi chitsanzo cha moyo osadzisanthula. Vesi ya 2 imakamba kuti “sanazilingalire mumtima mwawo.” Mmitima mwawo, sanazindikire zizindikiro za kulowa pansu kwa moyo wawo wa uzimu ndi kubwera kwa imfa yak u uzimu (tsitsi la imvi).

Izi ndi zina mwa zinthu zimene zinapangitsa kulowa pansu kwa mphamvu za ku uzimu. Santhulani mtima wanu pamene mukuona za izi:

### **1. MAONEKEDWE A CHINYENGO:**

Mulungu anagwiritsa ntchito mbaula ngati poonetsera za izi mu vesi 6-7. Moto wa mu mbaula ukuoneka kuti wathima, koma mu zoonza zake, ndi utsi. Kodi mumawadziwa anthu amene ali ndi maonekedwe abwino? Amakhala ngati a khristu, kulankhula ngati a khristu, koma moto wa mkati mwawo ndi utsi. Izi ndi monga mkwiyo, mangawa, kusakhululuka, dyera, kutsutsa. Mulungu akutsekula khomo la mbaula pofuna kuonetsera vuto. Amalola nyengo mmoyo wathu kuti zitidziwitse kuti tilibe chigonjetso chimene timaganiza kuti tilinacho.

### **2. KUMVERA KOCHIPA:**

Mulungu amagwiritsa ntchito mkate wa theka pofuna kuonetsera mu vesi 8. Anachita zinthu zina zimene Mulungu anawalamulira, koma anasiya zina osachita. Kumvera pang’ono ndi kusamvera komwe. Mkazi amene amakhulupirika pang’ono kwa mwamuna wake, ndiye kuti samvera konse.

### **3. KUMVERA KOSAKHAZIKIKA:**

Izi zikuonetseredwa pa zopusa zimene zikuchitika mu vesi la 11. Anthuwa amatsatira liwu lililonse limene limawalonjeza thandizo mwachitsanzo Aigupto, ndi Asuri. Kuyang’ana uku ndi uko sikumathetsa mavuto athu. Mayankho Sali mwa Aigupto kapena Asuri. Mayankho ali mwa Yesu Khristu.

#### 4. UTUMIKI WOSAKHAZIKA:

Izi zikuonetsedwa mu uta woonongeka mu vesi la 16. Mulungu akuwafanizira athuwa ngati uta umene wasiya kugwira ntchito yake. Ngati tili osadalilika mu utumiki wa chikhristu ndiye kuti tidzalephera kukwaniritsa zolinga zathu. Sitimaumilizidwa kuti tikwaniritse zolinga zathu. Sitimafikira cholinga chimene Mulungu ali nacho pa ife.

## CHAPUTALA CHA 7

### KUSANTHULA DERA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “dera” molingana ndi phunziroli.
- Kulongosola mmene kusanthula dera kumakhalira.
- Kudziwa zolinga za kusanthula dera.
- Kusanthula dera.
- Kugwiritsa ntchito kusanthula pofalitsa uthenga wabwino mdera.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Tauka, nuyendeyendc m'dzikoli m'litari mwace ndi m'mimba mwace; cifukwa kuti ndidzakupatsa iwe limenelo (Genesis 13:17)**

### MAWU OYAMBA

Muchaputala chathachi mumasanthula gulu la anthu. Muchaputala ichi musanthula dera ndi cholinga chofuna kufalitsa uthenga wabwino.

### DERA

Malingana ndi phunziroli, dera ndi malo apadera a dziko amene amadziwika ndi chigawo, chilankhulo, chikhalidwe ndi utsogoleri.

**Chigawo cha dera**, mwachitsanzo chimakhala chigwa cha mapiri chimene chimasiyanitsa ndi maiko ena. Malire a derail amakhala a zinthu za chilengedwe.

**Chilankhulo cha dera**, ndi malo a dziko amene anthu amalankhula chilankhulo chofanana.

**Chikhalidwe cha dera**, ndi dera la dziko limene anthu ake amakhala ofanana. Mwachitsanzo amakhala a mtundu umodzi ndi chipembedzo chofanana.

**Utsogoleri wa dera**, ndi mzinda, dziko, malire, chigawo mkati mwa dziko. Malire ake amakhala a boma limene likulamulira.

## **KUSANTHULA DERA**

Pamene mukusanthula dera, mumasanthula zinthu zonse zopezeka mkati mwa dziko. Mumadziwanso malire, utsogoleri, chiyankhulo, ndi zikhalidwe zimene zimapanga deralo kukhala losiyana. Mumasanthulanzo nyengo za moyo wa uzimu. Mumasanthulanso mphamvu za kunjira zimene zimakhudza deralo pa kulalikira kwa uthenga wabwino.

## **CHOLINGA CHA KUSANTHULA DERA**

Cholinga cha phunziro lanuli ndiko kufikira dera la dziko ndi uthenga wabwino. Ndi kafukufuku wa cholinga cha umishoni, osati kungochita kafukufuku. Samalisani kuti simukutaya nthawi yanu ndi kuphunzira kokha koma kulephera kufikira cholinga cha maphunziro anu! Zinthu zimene zimamanga dera pamodzi ndi kuzisiyanitsa zimapereka ndondomeko zofikira dera ndi uthenga wabwino.

Mumasanthula dera poyankha mafunsowa:

### **NDI MAGULU ATI A ATHU AMENE ALI MDERALO?**

Kodi ndi ndani, alipo angati, ndipo ali mabli iti?

### **KODI ANTHUWA ALI NDI ZINTHU ZITI ZOFANANA?**

Ndi ziti zimene zimawabweretsa anthuwa pamodzi ngati a dera lofanana?

### **KODI DERA LAWO NDI LOTANI?**

Kodi ndi ziti zimene mukufuna kudziwa za derail ndi cholinga chofuna kufikira anthu ndi uthenga wabwino?

### **KODI NDI NDANI AMENE ANGAFIKIRE ANTHUWA?**

Kodi ndi ziti zimene ndi zowayenereza ogwira ntchito ya kufalisa uthenga wabwino mderalo?

### **KODI DERALO LINGAFIKILIDWE BWANJI?**

Ndi njira ziti zimene mungawiritse ntchito mderalo? Ndi ziti zimene zingathe kugwira ntchito? Mayankho a mafunsowa azakuthandizani kudziwa ntchito yanu pofika mderali ndi kukuthandizani kukonza dongosolo la kufalisa uthenga wabwino.

## **MMENE MUNGADZWIRE ZINTHU**

Mungadziwe zinthu pochita kafukufuku wanu pochita izi:

**PEMPHERO:**

Mfunseni Mulungu akuululireni zimene mukufuna kudziwa zokhudza deralo kuti muthe kulifikira ndi uthenga wabwino.

**KUWERENGA ZINTHU ZOLEMBEDWA:**

Werengani mabuku kapene zinthu zolembedwa zokhudza deralo. Mndandanda wa zinthu zomwe mungazidziwe zikupezeka kumapeto kwa bukuli.

**KUONETSETSA:**

Yenderani deralo mwa inu nokha ndi kuona zinthu malo ndi anthu.

**MAFUNSO:**

Amfunseni mafunso anthu a deralo amene ndi atsogoleri ndi okhala mdelaro. Ngati muli kale anthu okhulupirira amene amatumikira kuderalo, afunseninsu mafunso mafunso kuti muthe kudziwa zimene aphunzira. Zitsanzo za mafunsowa zaperekedwanso mu bukuli.

**Gwiritsani ntchito mndandandawu pofuna kusanthula dera. Simungakwanitse kuyankha mafunso onse okhudza deralo, koma yankhani amene akuthandizani kudziwa zinthu za deralo.**

**KUDZIWA DERA**

Choyamba, tsimikizani za dera limene mukufuna kusanthula mderalo. Dera limakhala lapadera kapena losiyana pa zina mwa zifukwa izi:

-Anthu onse a deralo amalankhula chiyankhulo chofanana.

-Magulu a anthu a mderalo ndi a zikhalidwe zofanana. Mwachitsanzo, magulu onse a deralo ndi a mtundu umodzi, kapena a chipembedzo chofanana.

-Deralo ndi logawikana ndi madera ena lina a zinthu za chilengedwe monga mapiri, mitsinje ndi zina.

-Deralo ndi losiyana kumbali ya utsogoleri: likhoza kukhala

- Mudzi
- Mzinda
- Boma
- Chigawo

### **NDI ANTHU A MTUNDU WANJI AMENE ALI MDERALO?**

1. Ndi anthu a mtundu wanji amene ali mderalo? Pezani dzina lake ndi kuyerekeza chiwerengero cha magulu a anthuwo.
2. Jambulani mapu a deralo ndi kudziwa malo amene gulu la anthu amapezekako. Yambani kupempherera deralo ndi magulu ake osiyana.
3. Kodi anthu onse mderalo alimo angati?

### **KODI ANTHUWO ALI NDI ZINTHU ZITI ZOFANANA?**

Mwachidule, kodi anthuwo ndi ofanana bwanji mu

- a. Maubale awo
- b. Zikhalidwe zawo
- c. Ziyankhulo zawo
- d. Zipembedzo zawo
- e. Utsogoleri wawo

Kodi maguluwo amasiyana bwanji mu zimene zili pamwambazi?

### **KODI DERALI NDI LOTANI?**

### **KUSANTHULA MALO AKE:**

1. Kodi ndi zinthu ziti za mderalo zimene zimatchinga kufalisa uthenga wabwino?
2. Kodi ndi zinthu ziti za deralo zimene zingathe kugwiritsidwa ntchito kufalisa uthenga wabwino? Mwachitsanzo kodi kuli misewu yopitira ku malonda kapena kumipingo?
3. Kodi kusintha kwa nyengo kumasinjtha nthawi ya pa chaka imene ndiyabwino kuyendera malowo mkuchita utumiki?
4. Ziwaninzo zinthu zokhudza malowo zimene zikuthandizani kufikira maderawo ndi utumiki monga:
  - a. Mizindi yaikulu: onetsani pa mapu anu, mmalo amenewa chiwerengero cha anthu chimakhala cha anthu ambiri, choncho mukuyenera kukhala ndi ndondomeko yabwino yowafikira.



- b. Malo okwerera ndenge: awonetseninso pa mapu anu.
- c. Malo okwerera za mmadzi kapena za mwamba: awonetseninso pa mapu anu?
- d. Kodi deralo lili ndi malo oyimbirapo foni kapena intaneti?
- e. Kodi deralo lili ndi malo operekerapo mauthenga?
- f. Kodi kuli misewu yoyenda magalimoto? Onetsani pa mapu.
- g. Kodi pali mitsinje kapena Nyanja? Onetsani pa mapu anu.

### **KUSANTHULA MAUBALE A ANTHU:**

- 1. Kodi anthuwo amawamasukira bwanji anthu kunja (anthu amene sachokera kumadera awo). Kudziwa izi zikuthandizani kukonzekera kulandiridwa ndi miyeso yonse ya anthu pamene muwafikira ndi uthenga wabwino.
- 2. Mwachidule, ndi nthani amene amalamulira chuma ndi zinthu za mderalo? Muzafunikira thandizo kuchokera kwa anthu amenewa kuti akuthandizeni ndi zinthu kapena chuma chofalisira uthenga wabwino.

### **KUSANTHULA CHIKHALIDWE CHA ANTHU:**

Phunzirani chikhalidwe cha anthu a mderalo chimene chimakhudza kulalikira uthenga wabwino. Izi ndi zina mwa zinthu zimene muyenera kuziwona

- 1. Zikhulupiriro ndi msanamira:
  - a. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingawathandizire anthuwo kumvetsa uthenga wabwino?
  - b. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingalepheretse kumvetsa uthenga wabwino?
- 2. Makhalidwe a zochita zawo:
 

Kodi pali makhalidwe amene amachitika mderalo amene ndi oletsedwa Mbaibulo? Ngati ndi choncho, ndi makhalidwe ati? Mukuyenera kuthana nawo.
- 3. Zosowa?
  - a. Tengani deralo lonse ngati banja ndi kudziwa zosowa zawo: Monga
    - Kusowa zakudya
    - kusowa kwa maphunziro
    - kusowa kwa za umoyo
    - kusowa kwa misewu yabwino
    - kusowa kwa za chuma
    - kusowa kwa njira zotumizira mauthenga

Kulalikira kwanu kwa uthenga wabwino ndi njira za utumiki wanu kudzakhudza zosowa izi.

- b. Ndi zosowa ziti zimene mayankho ake amatha kuozezeka mderali? Ndi zosowa ziti zimene derail zilibe?

Maphunziro:

Kodi maphunziro a anthu mderali ndi ofika pa muyeso wanji? Nanga ndi angati amene amatha kuwerenga ndi kulemba? Nanga ndi angati amene amalemba chiyankhulo chawo. Ndi zofunika ndithu kudziwa chifukwa simungakonze uthenga wolemba ngati anthu a mderalo sadziwa kulemba.

Mukuyenera kufufunzanso:

- a. Sukulu zimene zimapereka maphunziro mderalo kwa ana.
- b. Sukulu zimene zimapereka maphunziro kwa akulu.
- c. Sukulu za koleji
- d. Sukulu zomwe zimapereka maphunziro a Baibulo

Mauthenga:

- a. Ndi chiyankhulo chiti chimene ndi choyenera kuperekera uthenga wabwino mderalo? Ngati mukufuna mufikire anthu ochuluka koyamba, sankhani chiyankhulo choyamba chimene anthu amalankhula mderalo.
- b. Kodi nanga Malemba amanthauziridwa bwanji mu chiyankhulo chimene ndi choyenera kutfalisira uthenga? Chipangano Chatsopano komanso chipangano Chakale.
- c. Kodi ndi zotheka kuwafikira anthuwo ndi uthenga wa mawailesi, kanema, nyuzi pepala, zinthuzi ndi mauthenga a pa tenifolo?
- d. Ndi njira iti yotumizira mauthenga imene imagwiritsidwa ntchito kwambiri mderalo?

### **ZINTHU ZOCHOKERA KUNJA:**

1. Ndi zosintha ziti zimene zikuchitika mderalo chifukwa cha ndondomeko za utsogoleri kapena zinthu zina zochitika kunja?
2. Kodi kusintha kumeneku kungawiritsidwe ntchito pofalisa uthenga wabwino?
3. Ndi magulu ati kapena mabungwe akunja kwa deralo amene amatsutsana ndi uthenga wabwino? Nanga ndi chifukwa chiyani?

Musalore zolepheretsa kapena zotsutsa kukulepheretsani kutumikira uthenga wabwino mderalo limene Mulungu wakutumani. Ngati sizithekha kuwafikira mu njira ina, yeseraninso njira zinazo.

**KUSANTHULA ULAMULIRO:**

1. Longosolani mwachidule ndondomeko za ulamuliro mderalo.
2. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angalepheretse kufalitsa uthenga?
3. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angathandizire kufalsa uthenga wabwino?
4. Ndi malamulo ati a boma amene angalepheretse kuchita utumiki mderalo?
5. Ndi malamulo ati a boma amene angathandizire kuchita utumiki mderalo?
6. Nanga ndi atsogoleri ati akuluakulu amene ali mderalo? Mukhoza kucheza nawo ndi kupampha chilolezo pochita utumiki wanu mderalo.

**KUSANTHULA UZIMU:**

1. Ndi magulu ati a chipembedzo amene ali mderalo?
2. Ndi anthu ochuluka bwanji amene amatsata za chipembedzo?
3. Ndi malingaliro anji amene anthu alinawo pa kusintha kwa chipembedzo kwa mtundu uliwonse? Yankho pa funsoli lizakukonzekerani pa chitsutso cha nkhani za chipembedzo chimene mudzakumana nacho.
4. Nanga ndi anthu angati amene ali okhulupirira mderalo?
5. Kodi mungawadziwe atsogoleri a chikhristu amene ali mderalo?
6. Kodi mumalitenga deralo kukhala loti silinalalikidwepo, kapena pang'ono kapena linalalikidwa mokwanira?
7. Mwachidule, mumakhulupirira kuti iyi ndi nthawi yofesa uthenga wabwino mderalo kapena nthawi yotuta?
8. Ndi mautumiki ati a chikhristu amene anayesedwa kuchitika mderalo ndi kulephereka? Mumakhulupirira kuti ndi chiyani chimene chinalepheretsa? Mukhoza kuphunzira ku zimene zinalepheretsa kuti musabwerezense zolakwikazo.
9. Ndi mipingo iti kapena mautumiki ati amene ali ochitachita mderalo?
10. Ndi ati amene akupambana naga ndi chifukwa chiyani? Mukhoza kuphunzira pa kupambana kwawo kwa maguluwa. Mukhonzansk kugwirizana nawo pofalisa uthenga wabwino.
11. Nanga mungagwirizane nawo bwanji kufikira anthuwo?
12. Mwa anthu amenewa, ndi angati amene akadalipobe mkutumikira?
13. Kodi muli magulu a anthu amene alibe mboni za a khristu pakati pawo?
14. Kodi muli akhristu amene amachitira umboni mderalo, nanga amachita mu chiyankhulo chanji? Mukhodza kutsogoleredwa kufikira anthu amene amalankhula chiyankhulo koma sanafikilodwe ndi uthenga wabwino.
15. Kodi nanga malingaliro a anthu pa mautumiki a akhristu nderalo ndi otani? Ochezeka, osiyana, kapena a udani?
16. Ndi mipingo iti yomwe imalalikira uthenga woonadi mderalo?
17. Kodi nanga imakula mwachangu motani?
18. Ndi zovuta ziti zimene anthu amakumana nazo nanga ndi chifukwa chiyani?

19. Ndi ati amene amachita bwino ndi ena amene sachita bwino?
20. Kodi pali chosowa chokhadzikisa mpingo kapena ayi?
21. Taganizrani mphamvu komanso maukulu a Satana amene ali ochitachita kapena kulamulira mderalo?

### **KODI NANGA NDI NDANI AMENE ANGAFIKIRE DERALO?**

Ndi ndani amene angawafikire anthuwa? Ndi ogwira ntchito angati amene akufunika kuti afikire mderali? Chiyerekezo cha chiwerengero chanu chizanena za ichi.

Nanga ndi zoyenerereza ziti zimene ogwira ntchito yotumikira uthenga ayenera kukhala nazo mderali. Aliyense amene apita kukafalisa uthanga ayenera:

- kukhala wokhulupirira amene ndi wa makhalidwe ndi moyo wabwino.
- wapemphero ndi wowerenga mau a Mulungu.
- wamphatso za uzimu zogwirizana ndi njira zimene agwiritse ntchito kufikira anthu a deralo.
- akhale wopezeka: kuthekera mkopanda ntchito kopanda kupezeka. Kodi munthu ndi wofuna ndi wokonzeka kupita?
- wokhala bwino ndi thupi la akhristu enanso amene ali ndi cholinga chofanana.
- woitanidwa ndi Mulungu kukatumikira mderalo.
- akhale wokonzeka bwino kuthupi, ku uzimu, ndi maphunziro pokafikira anthu.

### **KODI NANGA DERALI LINGAFIKILIDWE BWANJI?**

Kodi nanga derail lingafikilidwe bwanji? Nanga ndi njira ziti zimene zingagwiritsidwe nchito? Poyankha funsoli, onani zimene munaphunzira za kusanthula malo, chiyankhulo, zikhalidwe, ulamuliro ndi uzimu mderalo. Ndi ziti zimene ndi zofanana pa magulu a anthu mderalo zimene zimalora njirazo? Nanga ndi kusiyana kuti kumene kumafuna njiranzo zosiyana? Onetsetsani kuti njira zanuzo ndi za mmalemba. Musagwiritse ntchito njira zimene zimatsutsana ndi Mbaibulo.

Ndi ndondomeko ziti za utumiki zimene zimachita bwino mderalo? Ndi njira ziti zatsopano zimene mungaziyetsere? Mutatha kudziwa njira mwapemphero ndi kusanthula, dzifunsi funso lakuti: ndi zotsutsana ziti zimene pa njira zimenezi ndi magulu a anthu mderali kapena kunja kwa derail. Nanga mungathane nawo bwanji zitsutsozi?

### **PANGANI DONGOSOLO**

c

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “dera” molingana ndi phunziroli.

---

---

3. Kodi kusanthula dera kumakhudza chiyani?

---

---

4. Kodi cholinga cchosanthula dera ndi chiyani?

---

---

5. Ngati gawo limodzi la phunziro lanu, kodi munamaliza kusanthula dera lanu?

---

---

6. Kodi munapanga dongosolo logwiritsa ntchito zimene mwaphunzira pofalitsa uthenga wabwino mdera lanu?

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Werengani Genesis chaputala cha 13 chimene chimanena za kusanthula madera awiri osiyana. Limodzi linali la “Dera la Yorodano,” ndipo lina ndi “dziko la Kanani.” Lembani zotsatira za zimene mwasanthula:

**Dera la Yorodano**

**Dziko la Kanani**

## CHAPUTALA CHA 8

### KUSANTHULA MTUNDU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “mtundu.”
- Kulongosola kusanthula mtundu mmene kumakhalira.
- Kudziwa zolinga zosanthulira mtundu.
- Kusanthula mtundu.
- Kugwiritsa ntchito kusanthula pofalisa uthenga wabwino.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu (Luka 24:47)**

#### MAWU OYAMBA

Mwaphunzira za mmene mungasanthulire gulu la anthu ndi dera la anthu a mtundu. Muphunziro ili musanthula mtundu wa anthu onse ndi cholinga chofuna kuwafikira ndi uthenga wabwino.

#### MTUNDU

Mtundu ndi anthu amene amakhala pamodzi ndi ndondomeko zofanana za utsogoleri. Ndi malo amene akhazikitsidwa pa malire a dziko.

#### KUSANTHULA MTUNDU

Pamene mukusanthula mtundu mumachita mwatsatanetsatane podziwa utsogoleri, malire, chiyankhulo, zikhalidwe, uzimu komanso mphamvu ya zinthu za kunjira imene imakhudza kulakira kwa uthenga mdziko lonse.

#### CHOLINGA CHOSANTHULA MTUNDU

Cholinga cha phunziro lanu ndi kukula kuchokera kudera limene inu mukutumikira ndi cholinga chofuna kufikira mtundu wonse wa anthu ndi uthenga wabwino. Ndi kafukufuku wa cholinga chofuna cholalikira, osati kungofufuza chabe. Samalisani kuti nthawi yanu sikutha ndi kungophunzira koma osakwaniritsa cholinga chimene mukuchitira maphunzirowa! Zinthu

zimene zimamanga mtundu pamodzi ndi kusiyantsa ku mitundu ina zikhoza kukupatsani njira zothandizira kufikira mtundu wonse ndi uthenga wabwino.

Mumasanthula mtundu poyankha mafunso awa:

**NDI MAGULU ATI A ANTHU AMENE ALI PAMTUNDUPO?**

Kodi ndi ndani, alipo angati, nanga amakhala kuti? Ndi angati amene anafikilidwa ndi uthenga wabwino ndi amene sanafikilidwe?

**NDI ZINTHU ZITI ZIMENE MAGULUWA ALINAZO ZOFANANA?**

Ndi zinthu ziti zimene zimawabweretsa maguluwa pamodzi ngati mtundu? Kodi amafanana bwanji pa maubale, chikhalidwe, chiyankhulo, chipembedzo ndi utsogoleri?

**KODI MTUNDUWO ULI NGATI CHIYANI?**

Ndi ziti zimene mukuyenera kudziwa kudziwa zokhudza mtunduwo ndi cholinga chofuna kufikira anthuwo ndi uthenga wabwino?

**NANGA NDI NDANI AMENE AFIKIRE MTUNDUWO?**

Ndi ziti zimene ndi zowayenereza iwo amene akagwire ntchito yowayendera pofalisa uthenga wabwino?

**KODI NANGA MTUNDU UNGAFIKILIDWE BWANJI?**

Kodi nanga ndi njira ziti zimene mungagwiritse ntchito pofikira mtunduwo? Ndi ziti zimene zikhoza kuchcita bwino? Mayankho a mafunsowa adzkuthandizani kudziwa udindo wanu wofikira mtunduwo ndi kukhala ndi dongosolo lokhala lofikira anthuwo ndi uthenga wabwino.

**MUNGADZIWE BWANJI ZINTHU?**

Mungadziwe zinthu pochita kafukufuku wanu pochita izi:

**PEMPHERO:**

Mfunzeni Mulungu akuululireni zimene mukufuna kudziwa zokhudza deralo kuti muthe kulifikira ndi uthenga wabwino.

**KUWERENGA ZINTHU ZOLEMBEDWA:**

Werengani mabuku kapene zinthu zolembedwa zokhudza deralo. Mndandanda wa zinthu zomwe mungazidziwe zikupezeka kumapeto kwa bukuli.



## **KUONETSETSA:**

Yenderani deralo mwa inu nokha ndi kuona zinthu malo ndi anthu.

## **MAFUNSO:**

Amfunсени mafunso anthu a deralo amene ndi atsogoleri ndi okhala mdelaro. Ngati muli kale anthu okhulupirira amene amatumikira kuderalo, afunсениnso mafunso mafunso kuti muthe kudziwa zimene aphunzira. Zitsanzo za mafunsowa zaperekedwanso mu bukuli.

**Gwiritsani ntchito mndandandawu pofuna kusanthula dera. Simungakwanitse kuyankha mafunso onse okhudza deralo, koma yankhani amene akuthandizani kudziwa zinthu za deralo.**

## **KUDZIWA DERA**

Choyamba, tsimikizani za dera limene mukufuna kusanthula mderalo. Dera limakhala lapadera kapena losiyana pa zina mwa zifukwa izi:

-Anthu onse a deralo amalankhula chiyankhulo chofanana.

-Magulu a anthu a mderalo ndi a zikhalidwe zofanana. Mwachitsanzo, magulu onse a deralo ndi a mtundu umodzi, kapena a chipembedzo chofanana.

-Deralo ndi logawikana ndi madera ena lina a zinthu za chilengedwe monga mapiri, mitsinje ndi zina.

-Deralo ndi losiyana kumbali ya utsogoleri: likhoza kukhala

-Mudzi

-Mzinda

-Boma

-Chigawo

## **NDI ANTHU A MTUNDU WANJI AMENE ALI MDERALO?**

4. Ndi anthu a mtundu wanji amene ali mderalo? Pezani dzina lake ndi kuyerekeza chiwerengero cha magulu a anthuwo.
5. Jambulani mapu a deralo ndi kudziwa malo amene gulu la anthu amapezekako. Yambani kupempherera deralo ndi magulu ake osiyana.
6. Kodi anthu onse mderalo alimo angati?

## **KODI ANTHUWO ALI NDI ZINTHU ZITI ZOFANANA?**

Mwachidule, kodi anthuwo ndi ofanana bwanji mu

- f. Maubale awo
- g. Zikhalidwe zawo
- h. Ziyankhulo zawo
- i. Zipembedzo zawo
- j. Utsogoleri wawo

Kodi maguluwo amasiyana bwanji mu zimene zili pamwambazi?

## **KODI DERALI NDI LOTANI?**

### **KUSANTHULA MALO AKE:**

- 5. Kodi ndi zinthu ziti za mderalo zimene zimatchinga kufalisa uthenga wabwino?
- 6. Kodi ndi zinthu ziti za deralo zimene zingathe kugwiritsidwa ntchito kufalisa uthenga wabwino? Mwachitsanzo kodi kuli misewu yopitira ku malonda kapena kumipingo?
- 7. Kodi kusintha kwa nyengo kumasinjtha nthawi ya pa chaka imene ndiyabwino kuyendera malowo mkuchita utumiki?
- 8. Ziwaninzo zinthu zokhudza malowo zimene zikuthandizani kufikira maderawo ndi utumki monga:
  - h. Mizindi yaikulu: onetsani pa mapu anu, mmalo amenewa chiwerengero cha anthu chimakhala cha anthu ambiri, choncho mukuyenera kukhala ndi ndondomeko yabwino yowafikira.
  - i. Malo okwerera ndenge: awonetseninso pa mapu anu.
  - j. Malo okwerera za mmadzi kapena za mwamba: awonetseninso pa mapu anu?
  - k. Kodi deralo lili ndi malo oyimbirapo foni kapena intaneti?
  - l. Kodi deralo lili ndi malo operekerapo mauthenga?
  - m. Kodi kuli misewu yoyenda magalimoto? Onetsani pa mapu.
  - n. Kodi pali mitsinje kapena Nyanja? Onetsani pa mapu anu.

### **KUSANTHULA MAUBALE A ANTHU:**

- 3. Kodi anthuwo amawamasukira bwanji anthu kunja (anthu amene sachokera kumadera awo). Kudziwa izi zikuthandizani kukonzekera kulandiridwa ndi miyeso yonse ya anthu pamene muwafikira ndi uthenga wabwino.

4. Mwachidule, ndi nthani amene amalamulira chuma ndi zinthu za mderalo? Muzafunikira thandizo kuchokera kwa anthu amenewa kuti akuthandizeni ndi zinthu kapena chuma chofalisira uthenga wabwino.

### **KUSANTHULA CHIKHALIDWE CHA ANTHU:**

Phunzirani chikhalidwe cha anthu a mderalo chimene chimakhudza kulalikira uthenga wabwino. Izi ndi zina mwa zinthu zimene muyenera kuziwona

4. Zikhulupiriro ndi msanamira:
  - c. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingawathandizire anthuwo kumvetsa uthenga wabwino?
  - d. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingalepheretse kumvetsa uthenga wabwino?

5. Makhalidwe a zochita zawo:

Kodi pali makhalidwe amene amachitika mderalo amene ndi oletsedwa Mbaibulo? Ngati ndi choncho, ndi makhalidwe ati? Mukuyenera kuthana nawo.

6. Zosowa?

- c. Tengani deralo lonse ngati banja ndi kudziwa zosowa zawo: Monga
  - Kusowa zakudya
  - kusowa kwa maphunziro
  - kusowa kwa za umoyo
  - kusowa kwa misewu yabwino
  - kusowa kwa za chuma
  - kusowa kwa njira zotumizira mauthenga

Kulalikira kwanu kwa uthenga wabwino ndi njira za utumiki wanu kudzakhudza zosowa izi.

- d. Ndi zosowa ziti zimene mayankho ake amatha kuozezeka mderali? Ndi zosowa ziti zimene derail zilibe?

Maphunziro:

Kodi maphunziro a anthu mderali ndi ofika pa muyeso wanji? Nanga ndi angati amene amatha kuwerenga ndi kulemba? Nanga ndi angati amene amalemba chiyankhulo chawo. Ndi zofunika ndithu kudziwa chifukwa simungakonze uthenga wolemba ngati anthu a mderalo sadziwa kulemba.

Mukuyenera kufufunzanso:

- e. Sukulu zimene zimapereka maphunziro mderalo kwa ana.
- f. Sukulu zimene zimapereka maphunziro kwa akulu.
- g. Sukulu za koleji
- h. Sukulu zomwe zimapereka maphunziro a Baibulo

Mauthenga:

- e. Ndi chiyankhulo chiti chimene ndi choyenera kuperekera uthenga wabwino mderalo? Ngati mukufuna mufikire anthu ochuluka koyamba, sankhani chiyankhulo choyamba chimene anthu amalanikhula mderalo.
- f. Kodi nanga Malemba amatanthauziridwa bwanji mu chiyankhulo chimene ndi choyenera kutfalisira uthenga? Chipangano Chatsopano komanso chipangano Chakale.
- g. Kodi ndi zotheka kuwafikira anthuwo ndi uthenga wa mawailesi, kanema, nyuzi pepala, zinthuzi ndi mauthenga a pa tenifolo?
- h. Ndi njira iti yotumizira mauthenga imene imagwiritsidwa ntchito kwambiri mderalo?

#### **ZINTHU ZOCHOKERA KUNJA:**

- 4. Ndi zosintha ziti zimene zikuchitika mderalo chifkwa cha ndondomeko za utsogoleri kapena zinthu zina zochitika kunja?
- 5. Kodi kusintha kumeneku kungagwiritsidwe ntchito pofalisa uthenga wabwino?
- 6. Ndi magulu ati kapena mabungwe akunja kwa deralo amene amatsutsana ndi uthenga wabwino? Nanga ndi chifukwa chiyani?

Musalore zolepheretsa kapena zotsutsa kukulepheretsani kutumikira uthenga wabwino mderalo limene Mulungu wakutumani. Ngati sizithekha kuwafikira mu njira ina, yeseraninso njira zinazo.

#### **KUSANTHULA ULAMULIRO:**

- 7. Longosolani mwachidule ndondomeko za ulamuliro mderalo.
- 8. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angalepheretse kufalitsa uthenga?
- 9. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angathandizire kufalsa uthenga wabwino?
- 10. Ndi malamulo ati a boma amene angalepheretse kuchita utumiki mderalo?
- 11. Ndi malamulo ati a boma amene angathandizire kuchita utumiki mderalo?
- 12. Nanga ndi atsogoleri ati akuluakulu amene ali mderalo? Mukhoza kucheza nawo ndi kupampha chilolezo pochita utumiki wanu mderalo.

#### **KUSANTHULA UZIMU:**

- 22. Ndi magulu ati a chipembedzo amene ali mderalo?

23. Ndi anthu ochuluka bwanji amene amatsata za chipembedzo?
24. Ndi malingaliro anji amene anthu alinawo pa kusintha kwa chipembedzo kwa mtundu uliwonse? Yankho pa funsoli lizakukonzekerani pa chitsutso cha nkhani za chipembedzo chimene mudzakumana nacho.
25. Nanga ndi anthu angati amene ali okhulupirira mderalo?
26. Kodi mungawadziwe atsogoleri a chikristu amene ali mderalo?
27. Kodi mumalitenga deralo kukhala loti silinalalikidwepo, kapena pang'ono kapena linalalikidwa mokwanira?
28. Mwachidule, mumakhulupirira kuti iyi ndi nthawi yofesa uthenga wabwino mderalo kapena nthawi yotuta?
29. Ndi mautumiki ati a chikristu amene anayesedwa kuchitika mderalo ndi kulephereka? Mumakhulupirira kuti ndi chiyani chimene chinalepheretsa? Mukhoza kuphunzira ku zimene zinalepheretsa kuti musabwerezenso zolakwikazo.
30. Ndi mipingo iti kapena mautumiki ati amene ali ochitachita mderalo?
31. Ndi ati amene akupambana naga ndi chifukwa chiyani? Mukhoza kuphunzira pa kupambana kwawo kwa maguluwa. Mukhonzansk kugwirizana nawo pofalisa uthenga wabwino.
32. Nanga mungagwirizane nawo bwanji kufikira anthuwo?
33. Mwa anthu amenewa, ndi angati amene akadalipobe mkutumikira?
34. Kodi muli magulu a anthu amene alibe mboni za a khristu pakati pawo?
35. Kodi muli akhristu amene amachitira umboni mderalo, nanga amachita mu chiyankhulo chanji? Mukhodza kutsogoleredwa kufikira anthu amene amalankhula chiyankhulo koma sanafikilodwe ndi uthenga wabwino.
36. Kodi nanga malingaliro a anthu pa mautumiki a akhristu nderalo ndi otani? Ochezeka, osiyana, kapena a udani?
37. Ndi mipingo iti yomwe imalalikira uthenga woonadi mderalo?
38. Kodi nanga imakula mwachangu motani?
39. Ndi zovuta ziti zimene anthu amakumana nazo nanga ndi chifukwa chiyani?
40. Ndi ati amene amachita bwino ndi ena amene sachita bwino?
41. Kodi pali chosowa chokhadzikisa mpingo kapena ayi?
42. Taganizrani mphamvu komanso maukulu a Satana amene ali ochitachita kapena kulamulira mderalo?

### **KODI NANGA NDI NDANI AMENE ANGAFIKIRE DERALO?**

Ndi ndani amene angawafikire anthuwa? Ndi ogwira ntchito angati amene akufunika kuti afikire mderali? Chiyerekezo cha chiwerengero chanu chizanena za ichi.

Nanga ndi zoyenereza ziti zimene ogwira ntchito yotumikira uthenga ayenera kukhala nazo mderali. Aliyense amene apita kukafalisa uthanga ayenera:

- kukhala wokhulupirira amene ndi wa makhalidwe ndi moyo wabwino.
- wapemphero ndi wowerenga mau a Mulungu.
- wamphatso za uzimu zogwirizana ndi njira zimene agwiritse ntchito kufikira anthu a deralo.
- akhale wopezeka: kuthekera mkopanda ntchito kopanda kupezeka. Kodi munthu ndi wofuna ndi wokonzeka kupita?
- wokhala bwino ndi thupi la akhristu enanso amene ali ndi cholinga chofanana.
- woitanidwa ndi Mulungu kukatumikira mderalo.
- akhale wokonzeka bwino kuthupi, ku uzimu, ndi maphunziro pokafikira anthu.

### **KODI NANGA DERALI LINGAFIKILIDWE BWANJI?**

Kodi nanga derail lingafikilidwe bwanji? Nanga ndi njira ziti zimene zingagwiritsidwe nchito? Poyankha funsoli, onani zimene munaphunzira za kusanthula malo, chiyankhulo, zikhalidwe, ulamuliro ndi uzimu mderalo. Ndi ziti zimene ndi zofanana pa magulu a anthu mderalo zimene zimalora njirazo? Nanga ndi kusiyana kuti kumene kumafuna njiranzo zosiyana? Onetsetsani kuti njira zanuzo ndi za mmalemba. Musagwiritse ntchito njira zimene zimatsutsana ndi Mbaibulo.

Ndi ndondomeko ziti za utumiki zimene zimachita bwino mderalo? Ndi njira ziti zatsopano zimene mungaziyetsere? Mutatha kudziwa njira mwapemphero ndi kusanthula, dzifunsemi funso lakuti: ndi zotsutsana ziti zimene pa njira zimenezi ndi magulu a anthu mderali kapena kunja kwa derali. Nanga mungathane nawo bwanji zitsutsozi?

### **PANGANI DONGOSOLO**

Kusanthula kumene mwakupangaku, mkopanga phindu pokhapokha mutagwiritsa ntchito zimene mwaphunzira zokhudza dera. Derali silingafikilidwe ndi kuphunzira kokha ayi. Mukuyenera kupanga dongosolo lofikira deralo ndi uthenga wabwino. Chaputala cha 11, “Njira za Dongosolo,” lizakuthandizani kupanga dongosolo lofikira dera limene mwalisanthula.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauza la mawu oti “mtundu.”

---

3. Kodi kusanthula mtundu kumakhudza chiyani?

---

4. Kodi zolinga za kusanthula mtundu ndi chiyani?

---

---

5. Ngati gawo limodzi lophunzira phunziroli, kodi munamaliza kusanthuloa mtundu?

---

6. Kodi mwapanga dongosolo loti mugwiritse ntchito zimene mwaphunzira zokhudza kufalisa uthenga wabwino kwa amitundu?

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Phunzira kusanthula kwa mbiri komanso uzimu wa mtundu wa ana a Israyei mu Machitdwe chaputala cha 7.



## CHAPUTALA CHA 9

### KUSANTHULA CHIGAWO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “chigawo.”
- Kulongosola za kusanthula chigawo.
- Kuzindikira zolinga za kusanthula chigawo.
- Kusanthula chigawo.
- Kugwiritsa ntchito kusanthula kwanu pofalisa uthenga wabwino.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse (Marko 16:15)**

#### MAWU OYAMBA

Mwaphunzira za mmene mungasanthulire gulu la anthu, dera komanso mtundu. Muphunziro ili muphunzira za mmene mungasanthulire chigawo chonse cha dziko ndi cholinga chofuna kuchifikira ndi uthenga wabwino.

#### CHIGAWO

Chifukwa cha phunziroli, chigawo ndi gawo la dziko limene lapangidwa ndi mitundu yambiri yopezeka moyandikana mmalire, ndipo amayankhula ziyankhulo zofanana, makhalidwe awo ofanana, zipembedzo komanso ulamuliro.

Boma la Nsanje lili mu chigawo cha kumwera. Ndipo kumweraku kulinso maboma ena monga Chikwawa, Thyolo ndi ena ambiri. Mmabomawa mumakhala anthu a mitundu yosiyana ndipo ena ali ndi malire, zikhulupiriro, chiyankhulo, komanso makhalidwe ofanana osaiwalanso utsogoleri wawo.

#### KUSANTHULA CHIGAWO

Pamene mukusanthu achigawo mumachita mwatsatanetsatane pofuna kudziwa ulamuliro, malo, chiyankhulo, chikhalidwe ndi zinrthu zina za uzimu komanso za kunja kwa mzinda zimene zimakhudza kufalisa uthenga wabwino mu zigawo zonse.

#### CHOLINGA CHOSANTHULA CHIGAWO

Cholinga cha phunziro lanu ndi kuchulukana kuchokera ku mtundu umene inu mukutumikirako ndi kufikira chigawo chonse ndi uthenga wabwino.

Kusanthula chigawo ndi kafukufuku wa cholinga chochita ulaliki, osangoti kafukufuku chabe. Samalisani kuti nthawi yanu sikuthera pongochita maphunzirowa mkuiwala kukwaniritsa cholinga chenicheni chopangira maphunziro anu.

Zinthu zimene zimabweretsa chigawo pamodzi ndi kukhala chosiyana ndi zigawo zina zimatithandiza kukhala ndi dongosolo lofikira chigawo chonse ndi uthenga wabwino. Dziko linapangidwa ndi zigawo zambiri monga Malawi. Ngati tifikira zigawo zonse ndiye kuti tizatha kufikira dziko lonse.

Mumasanthula chigawo pofuna kuyankha mafunso awa:

### **KODI NDI MTUNDU KAPENA MAGULU A ANTHU ATI AMENE ALI MUCHIGAWOCHO?**

Ndi mitundu iti imene ikupezeka mu chigawocho? Muli mitundu ingati? Nanga athu alimo angati, nanga chimawapanga kukhala chigawo ndi chiyani?

### **NDI ZITI ZIMENE ZIMAPANGA MTUNDU NDI MAGULU A ANTHU KHUKHALA AMODZI?**

Kodi ali ngati ndani mmaubale awo, muchikhalidwe chawo, muzipembedzo zawo komanso mu utsogoleri wawo?

### **KODI CHIGAWOCHI CHILI NGATI CHIYANI?**

Kodi ndi ziti zimene tikufunika kudziwa mu chigawocho ndi cholinga chofuna kuwafikira anthu amene akhala mmenemo ndi uthenga wabwino?

### **NANGA NDI NDANI AMENE AYENERA KUFIKIRA CHIGAWOCHO?**

Ndi zinthu ziti zimene ndi zomuyenereza munthu wokalalikira uthenga mchigawocho kuti akhale nazo? Nanga ndi ophunzira angati amene akufunikira?

### **NANGA CHIGAWOCHI CHINGAFIKILIDWE BWANJI?**

Ndi njira ziti zofanana zimene zingagwiritsidwe ntchito mu chigawo chonsecho? Ndi ziti zimene zikhoza kuchita bwino?

Mayankho a funsoli azakuthandizani kudziwa ntchito yanu yofikira chigawocho komanso kukonza dongosolo la kuwafikira anthu ndi uthenga wabwino.

### **MUNGADZIWE BWANJI ZINTHU?**

Mungadziwe zinthu pochita kafukufuku wanu pochita izi:

#### **PEMPHERO:**

Mfunzeni Mulungu akuululireni zimene mukufuna kudziwa zokhudza chigawocho kuti muthe kulifikira ndi uthenga wabwino.

#### **KUWERENGA ZINTHU ZOLEMBEDWA:**

Werengani mabuku kapene zinthu zolembedwa zokhudza chigawocho. Mndandanda wa zinthu zomwe mungazidziwe zikupezeka kumapeto kwa bukuli.

#### **KUONETSETSA:**

Yenderani chigawocho mwa inu nokha ndi kuona zinthu malo ndi anthu.

#### **MAFUNSO:**

Amfunzeni mafunso anthu a deralo amene ndi atsogoleri ndi okhala mdelaro. Ngati muli kale anthu okhulupirira amene amatumikira kuchigawocho, afunseinso mafunso mafunso kuti muthe kudziwa zimene aphunzira. Zitsanzo za mafunsowa zaperekedwanso mu bukuli.

**Gwiritsani ntchito mndandandawu pofuna kusanthula dera. Simungakwanitse kuyankha mafunso onse okhudza chigawocho, koma yankhani amene akuthandizani kudziwa zinthu za chigawocho.**

### **KUDZIWA CHIGAWO**

Choyamba, tsimikizani za dera limene mukufuna kusanthula chigawocho. Gawo limakhala lapadera kapena losiyana pa zina mwa zifukwa izi:

-Anthu onse a chigawocho amalankhula chiyankhulo chofanana.

-Magulu a anthu a mchigawo ndi a zikhalidwe zofanana. Mwachitsanzo, magulu onse a chigawocho ndi a mtundu umodzi, kapena a chipembedzo chofanana.

-Chigawocho ndi chogawikana ndi magawo ena lina a zinthu za chilengedwe monga mapiri, mitsinje ndi zina.

-Chigawocho ndi chosiyana kumbali ya utsogoleri: likhoza kukhala

-Mudzi

-Mzinda

-Boma

-Chigawo

### **NDI ANTHU A MTUNDU WANJI AMENE ALI MCHIGAWOCHO?**

7. Ndi anthu a mtundu wanji amene ali mchigawo? Pezani dzina lake ndi kuyerekeza chiwerengero cha magulu a anthuwo.
8. Jambulani mapu a chigawo ndi kudziwa malo amene gulu la anthu amapezekako. Yambani kupempherera chigawo ndi magulu ake osiyana.
9. Kodi anthu onse mchigawo alimo angati?

### **KODI ANTHUWO ALI NDI ZINTHU ZITI ZOFANANA?**

Mwachidule, kodi anthuwo ndi ofanana bwanji mu

- k. Maubale awo
- l. Zikhalidwe zawo
- m. Ziyankhulo zawo
- n. Zipembedzo zawo
- o. Utsogoleri wawo

Kodi maguluwo amasiyana bwanji mu zimene zili pamwambazi?

### **KODI CHIGAWOCHO NDI CHOTANI?**

### **KUSANTHULA MALO AKE:**

9. Kodi ndi zinthu ziti za mchigawo zimene zimatchinga kufalisa uthenga wabwino?
10. Kodi ndi zinthu ziti za mchigawo zimene zingathe kugwiritsidwa ntchito kufalisa uthenga wabwino? Mwachitsanzo kodi kuli misewu yopitira ku malonda kapena kumipingo?

11. Kodi kusintha kwa nyengo kumasijntha nthawi ya pa chaka imene ndiyabwino kuyendera malowo mkuchita utumiki?
12. Ziwaninzo zinthu zokhudza malowo zimene zikuthandizani kufikira maderawo ndi utumki monga:
  - o. Mizindi yaikulu: onetsani pa mapu anu, mmalo amenewa chiwerengero cha anthu chimakhala cha anthu ambiri, choncho mukuyenera kukhala ndi ndondomeko yabwino yowafikira.
  - p. Malo okwerera ndenge: awonetseninso pa mapu anu.
  - q. Malo okwerera za mmadzi kapena za mwamba: awonetseninso pa mapu anu?
  - r. Kodi deralo lili ndi malo oyimbirapo foni kapena intaneti?
  - s. Kodi deralo lili ndi malo operekerapo mauthenga?
  - t. Kodi kuli misewu yoyenda magalimoto? Onetsani pa mapu.
  - u. Kodi pali mitsinje kapena Nyanja? Onetsani pa mapu anu.

#### **KUSANTHULA MAUBALE A ANTHU:**

5. Kodi anthuwo amawamasukira bwanji anthu kunja (anthu amene sachokera kumadera awo). Kudziwa izi zikuthandizani kukonzekera kulandiridwa ndi miyeso yonse ya anthu pamene muwafikira ndi uthenga wabwino.
6. Mwachidule, ndi nthani amene amalamulira chuma ndi zinthu za mderalo? Muzafunikira thandizo kuchokera kwa anthu amenewa kuti akuthandizeni ndi zinthu kapena chuma chofalisira uthenga wabwino.

#### **KUSANTHULA CHIKHALIDWE CHA ANTHU:**

Phunzirani chikhalidwe cha anthu a mderalo chimene chimakhudza kulalikira uthenga wabwino. Izi ndi zina mwa zinthu zimene muyenera kuziwona

7. Zikhulupiriro ndi msanamira:
  - e. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingawathandizire anthuwo kumvetsa uthenga wabwino?
  - f. Ndi zikhulupiriro kapena misanamira iti kapena miyambo imene ingalepheretse kumvetsa uthenga wabwino?

8. Makhalidwe a zochita zawo:

Kodi pali makhalidwe amene amachitika mderalo amene ndi oletsedwa Mbaibulo? Ngati ndi choncho, ndi makhalidwe ati? Mukuyenera kuthana nawo.

9. Zosowa?

- e. Tengani deralo lonse ngati banja ndi kudziwa zosowa zawo: Monga

- Kusowa zakudya
- kusowa kwa maphunziro
- kusowa kwa za umoyo
- kusowa kwa misewu yabwino
- kusowa kwa za chuma
- kusowa kwa njira zotumizira mauthenga

Kulalikira kwanu kwa uthenga wabwino ndi njira za utumiki wanu kudzakhudza zosowa izi.

- f. Ndi zosowa ziti zimene mayankho ake amatha kupezeka mchigawocho? Ndi zosowa ziti zimene mchigawo zilibe?

Maphunziro:

Kodi maphunziro a anthu mderali ndi ofika pa muyeso wanji? Nanga ndi angati amene amatha kuwerenga ndi kulemba? Nanga ndi angati amene amalemba chiyankhulo chawo. Ndi zofunika ndithu kudziwa chifukwa simungakonze uthenga wolemba ngati anthu a mderalo sadziwa kulemba.

Mukuyenera kufufunzanso:

- i. Sukulu zimene zimapereka maphunziro mchigawo kwa ana.
- j. Sukulu zimene zimapereka maphunziro kwa akulu.
- k. Sukulu za koleji
- l. Sukulu zomwe zimapereka maphunziro a Baibulo

Mauthenga:

- i. Ndi chiyankhulo chiti chimene ndi choyenera kuperekerera uthenga wabwino mchigawo? Ngati mukufuna mufikire anthu ochuluka koyamba, sankhani chiyankhulo choyamba chimene anthu amaalankhula mchigawo.
- j. Kodi nanga Malemba amatanthauziridwa bwanji mu chiyankhulo chimene ndi choyenera kutfalisira uthenga? Chipangano Chatsopano komanso chipangano Chakale.
- k. Kodi ndi zotheka kuwafikira anthuwo ndi uthenga wa mawailesi, kanema, nyuzi pepala, zinthuzi ndi mauthenga a pa tenifolo?
- l. Ndi njira iti yotumizira mauthenga imene imagwiritsidwa ntchito kwambiri mchigawo?

### **ZINTHU ZOCHOKERA KUNJA:**

7. Ndi zosintha ziti zimene zikuchitika mchigawo chifkwa cha ndondomeko za utsogoleri kapena zinthu zina zochitika kunja?

8. Kodi kusintha kumeneku kungagwiritsidwe ntchito pofalisa uthenga wabwino?
9. Ndi magulu ati kapena mabungwe akunja kwa deralo amene amatsutsana ndi uthenga wabwino? Nanga ndi chifukwa chiyani?

Musalore zolepheretsa kapena zotsutsa kukulepheretsani kutumikira uthenga wabwino mchigawo umene Mulungu wakutumani. Ngati sizithekha kuwafikira mu njira ina, yeseraninso njira zinazo.

#### **KUSANTHULA ULAMULIRO:**

13. Longosolani mwachidule ndondomeko za ulamuliro mchigawo.
14. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angalepheretse kufalitsa uthenga?
15. Ndi magulu ati a ulamuliro amene angathandizire kufalisa uthenga wabwino?
16. Ndi malamulo ati a boma amene angalepheretse kuchita utumiki mchigawo?
17. Ndi malamulo ati a boma amene angathandizire kuchita utumiki mchigawo?
18. Nanga ndi atsogoleri ati akuluakulu amene ali mchigawo? Mukhoza kucheza nawo ndi kupampha chilolezo pochita utumiki wanu mchigawo.

#### **KUSANTHULA UZIMU:**

43. Ndi magulu ati a chipembedzo amene ali mchigawo?
44. Ndi anthu ochuluka bwanji amene amatsata za chipembedzo?
45. Ndi malingaliro anji amene anthu alinawo pa kusintha kwa chipembedzo kwa mtundu uliwonse? Yankho pa funsoli lizakukonzekerani pa chitsutso cha nkhani za chipembedzo chimene mudzakumana nacho.
46. Nanga ndi anthu angati amene ali okhulupirira mchigawo?
47. Kodi mungawadziwe atsogoleri a chikristu amene ali mchigawo?
48. Kodi mumalitenga gawolo kukhala loti silinalalikidwepo, kapena pang'ono kapena linalalikidwa mokwanira?
49. Mwachidule, mumakhulupirira kuti iyi ndi nthawi yofesa uthenga wabwino mderalo kapena nthawi yotuta?
50. Ndi mautumiki ati a chikristu amene anayesedwa kuchitika mchigawo ndi kulephereka? Mumakhulupirira kuti ndi chiyani chimene chinalepheretsa? Mukhoza kuphunzira ku zimene zinalepheretsa kuti musabwerezenso zolakwikazo.
51. Ndi mipingo iti kapena mautumiki ati amene ali ochitachita mchigawocho?
52. Ndi ati amene akupambana naga ndi chifukwa chiyani? Mukhoza kuphunzira pa kupambana kwawo kwa maguluwa. Mukhonzansk kugwirizana nawo pofalisa uthenga wabwino.
53. Nanga mungagwirizane nawo bwanji kufikira anthuwo?
54. Mwa anthu amenewa, ndi angati amene akadalipobe mkutumikira?
55. Kodi muli magulu a anthu amene alibe mboni za a khristu pakati pawo?

56. Kodi muli akhristu amene amachitira umboni mchigawocho, nanga amachita mu chiyankhulo chanji? Mukhodza kutsogoleredwa kufikira anthu amene amalankhula chiyankhulo koma sanafikilodwe ndi uthenga wabwino.
57. Kodi nanga malingaliro a anthu pa mautumiki a akhrsitu nderalo ndi otani? Ochezeka, osiyana, kapena a udani?
58. Ndi mipingo iti yomwe imalalikira uthenga woonadi chigawo?
59. Kodi nanga imakula mwachangu motani?
60. Ndi zovuta ziti zimene anthu amakumana nazo nanga ndi chifukwa chiyani?
61. Ndi ati amene amachita bwino ndi ena amene sachita bwino?
62. Kodi pali chosowa chokhadzikisa mpingo kapena ayi?
63. Taganizrani mphamvu komanso maukulu a Satana amene ali ochitachita kapena kulamulira mderalo?

### **KODI NANGA NDI NDANI AMENE ANGAFIKIRE CHIGAWOCHI?**

Ndi ndani amene angawafikire anthuwa? Ndi ogwira ntchito angati amene akufunika kuti afikire chigawocho? Chiyerekezo cha chiwerengero chanu chizana za ichi.

Nanga ndi zoyenera ziti zimene ogwira ntchito yotumikira uthenga ayenera kukhala nazo mderali. Aliyense amene apita kukafalisa uthanga ayenera:

- kukhala wokhulupirira amene ndi wa makhalidwe ndi moyo wabwino.
- wapemphero ndi wowerenga mau a Mulungu.
- wamphatso za uzimu zogwirizana ndi njira zimene agwiritse ntchito kufikira anthu a deralo.
- akhale wopezeka: kuthekera mkopanda ntchito kopanda kupezeka. Kodi munthu ndi wofuna ndi wokonzeka kupita?
- wokhala bwino ndi thupi la akhristu enaso amene ali ndi cholinga chofanana.
- woitanidwa ndi Mulungu kukatumikira mderalo.
- akhale wokonzeka bwino kuthupi, ku uzimu, ndi maphunziro pokafikira anthu.

### **KODI NANGA CHIGAWOCH CHINGAFIKILIDWE BWANJI?**

Kodi nanga chigawochi chiingafikilidwe bwanji? Nanga ndi njira ziti zimene zingagwiritsidwe nchito? Poyankha funsoli, onani zimene munaphunzira za kusanthula malo, chiyankhulo, zikhalidwe, ulamuliro ndi uzimu mderalo. Ndi ziti zimene ndi zofanana pa magulu a anthu mderalo zimene zimalora njirazo? Nanga ndi kusiyana kuti kumene kumafuna njiranzo zosiyana? Onetsetsani kuti njira zanuzo ndi za mmalemba. Musagwiritse ntchito njira zimene zimatsutsana ndi Mbaibulo.



Ndi ndondomeko ziti za utumiki zimene zimachita bwino mderalo? Ndi njira ziti zatsopano zimene mungaziyetsere? Mutatha kudziwa njira mwapemphero ndi kusanthula, dzifunsemi funso lakuti: ndi zotsutsana ziti zimene pa njira zimenezi ndi magulu a anthu mderali kapena kunja kwa derali. Nanga mungathane nawo bwanji zitsutsozi?

### **PANGANI DONGOSOLO**

Kusanthula kumene mwakupangaku, mkopanga phindu pokhapokha mutagwiritsa ntchito zimene mwaphunzira zokhudza dera. Derali silingafikilidwe ndi kuphunzira kokha ayi. Mukuyenera kupanga dongosolo lofikira deralo ndi uthenga wabwino. Chaputala cha 11, “Njira za Dongosolo,” lizakuthandizani kupanga dongosolo lofikira dera limene mwalisanthula.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “chigawo.”

---

---

3. Kodi kusanthula chigawo kumakhudza chiyani?

---

---

4. Kodi ndi zolinga ziti zosanthulira chigawo?

---

---

5. Ngati gawo limodzi la phunziro lanu, kodi munamaliza kusanthula chigawo?

---

---

6. Kodi mwapanga dongosolo limene mugwiritsa ntchito molingana ndi mmene mwaphunzirira ndi cholingachofalitsa uthenga wabwino muchigawo?

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## CHAPUTALA CHA 10

### KUSANTHULA BUNGWE LA CHIKHRISTU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulongosola kusanthula kwa mabungwe a chikhristu mmene kumakhalira.
- Kudziwa zolinga za kusanthula mabungwe a chikhristu.
- Kusanthula bungwe la chikhristu.
- Kugwiritsa ntchito zotsatira za kusanthula kwanu pothandiza bungwe kukwaniritsa cholinga cha Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Iye wokhala nalo khutu amve cimene Mzimu anena kwa Mipingo (Chibvumbulutso 2:29)**

### MAWU OYAMBA

Okhulupirira onse amene ndi obadwa mwatsopano ali gawo limodzi la mpingo woona umene umatchedwa thupi la Khristu.

**Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse rinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi (I Akorinto 12:13)**

(Yuda 3 amalongosola za kukhala wobadwa mwatsopano mwa Mzimu.)

Thupi la Khristuli kapena mpingo wapangidwa mu njira zambiri mdziko lapansi. Pali mipingo yambiri ya mmadera, mautumiki, ziyanjano za anthu opemphera ndi mabungwe a chikhristu. Mabugwe onsewa akhazikika pa cholinga chofuna kukwaniritsa cholinga cha mpingo wa mmadera. Mu phunziro limeneli, za mmene mungasanthulire mabungwe a chikhristuwa.

### CHOLINGA CHA KUSANTHULA BUNGWE

Pakuti ndi dongosolo la Mulungu kuti mpingo ukhale malo ofalisirapo uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi:

**ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse**

**tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu (Aefeso 3:9-11)**

Baibulo limatiuza kuti ogwira ntchito mmunda alipo ochepa:

**Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka (Mateyu 9:37)**

Ngati ogwira ntchito alipo ochepa, ndiye kuti ayenera kupangana mwakuthekera ndi cholinga chofuna kuti mpingo ukwaniritse ntchito yake yotumikira kudziko lapansi.

Mumasanthula bungwe la chikristu ndi zolinga izi:

1. Kudziwa cholinga cha bungwe, upaderadera wake pokwaniritse ntchito ya mpingo yofalisa uthenga wabwino.
2. Kudziwa kuchita bwino kwa bungwe kumene kulipo. Kodin limakwaniritse bwino bwanji zolinga zake. Likupambana bwabji? Nanga likulephera bwanji?
3. Kukonza dongosolo la bungwe kuti likwaniritse bwino cholinga cha Mulungu.

Ngati muli mmodzi wa anthu a bungwe limene mukusanthula, mudzaziwanso gawo lanu lothandiza bungwelo kuti likwaniritse cholinga chake.

### **KUSANTHULAKO KUMAKHUDZA CHIYANI**

Kusanthula kwa bungwe kumakhudza kuphunzira zolinga zake, dongosolo lake, mphamvu zake, zofooka zake, malo amene lili, chuma chake ndi ndondomeko zake.

### **MMENE MUNGADZIWIRE ZINTHU**

Mungathe kudziwa zinthu pamene mukusanthula pochita izi:

#### **PEMPHERO:**

Mfunseni Mulungu akuululireni za zimene mukufuna kudziwa za bungwelo.

#### **WERENGANI ZINTHU ZOLEMBEDWA:**

Werengani zinthu zonse zolembedwa zokhudza bungwelo. Mwachitsanzo, kodi ali ndi chiphunzitso chawo, mawu okhudza cholinga chawo, dongosolo la zochita, zomuyenereza munthu kukhala mmodzi wawo, malamulo kapena mbiri?

**KUWONETSETSA:**

Mwai inu nokha onetsetsani bungwelo. Onani mamembala ake ndi atsogoleri pamene akugwira ntchito yautumiki imene Mulungu wawaitanira.

**MAFUNSO:**

Funsani mafunso atsogoleri komanso ogwira ntchito okhudza bungwelo.

**KUSANTHULA BUNGWE**

Izi ndi zina mwa zinthu zimene muziphunzira pamene mukusanthula bungwe:

**CHOLINGA:**

1. Kodi bungwelo lili ndi zolembedwa zimene zimakamba za cholinga cha bungwelo? Izi ndi zolembedwa zimene zimakamba za cholinga cha bungwelo. Si zimene bungwelo limakhulupirira ayi. Koma ndi mawu amene amafotokoza za zifukwa zimene akupezekera. Kodi cholinga chawo chenicheni ndi chiyani?
2. Kodi anthu a mubungwelo amamvetsa zolinga za bungwelo? Pofuna kudziwa funsani mafunso ambiri okhudza bungwelo. Kodi cholinga cha mpingo kapena bungwe ndi chiyani?
3. Kodi anthu a mubungwelo amamvetsa gawo lawo pokwaniritsa cholinga cha bungwelo?
4. Kodi bungwelo likukwaniritsa cholinga chake? Kodi likukwaniritsa zimene limakhulupiriranso kuti Ambuye akadachita?
5. Kodi cholinga cha bungwelo chikugwirizana bwanji ndi cholinga cha Mulungu? Werengani cholinga cha Mulungu mu Aefeso 1:9-11 ndi 3:9-11.

**ZOCHITA/MALINGALIRO:**

1. Kodi bungwelo lili ndi zoti lizichita zolembedwa?
2. Kodi zochitazi zikugwirizana ndi zolinga za bungwelo? Kodi chochitazo chilichonse chimathandizira kukwaniritsa cholinga cha bungwelo?
3. Kodi zochitazo zimaonetsera zimene zikuchitika, ndi ndani, komanso liti?
4. Kodi zochitazo ndi zolembedwa kuti ndi zotheke kuwauza antthu ngati zikukwaniritsidwa?
5. Kodi bungwelo limachita misonkhano. Kodi limakhala ndi nthawi yopemphera ndi kumfuna Mulungu pa chitsogozo?
6. Ndi ndani amapanga zochita za bungwelo?

**ZAMPHAMVU?**

Fufuzani za mphamvu za bungwelo. Ndi ziti zimene likuchita bwino? Ndi chabwino chiti chimene bungwelo chili nacho?

**ZOFOOKA?**

Santhulani zoffoka za bungwelo. Kodi likulephera pati? Nanga ndi pati pamene pakufunika kukonza?

### **MALO?**

1. Ndi malo anji amene bungwelo likutumikirako? Kodi limatumikira kwa anthu apadera, gulu, dera, mtundu kapena chigawo cha dziko?
2. Kodi bungwelo linafufuza za malowo? Kodi linasanthula za anthuwo, malowo, mtundu umene akutumikirako?
3. Ndi zinthu ziti zimene ndi zokhudza malowo zomwe zikuyenera kusintha zaka zochepa za mtsogolo?
4. Ndi zinthu ziti zimene zikuyenera kukhala chimodzimidzi?

### **CHUMA/KATUNDU:**

Ogwira, ndalama ndi katundu wina ndi zinthu zofunikira ku bungwe lililonse.

1. Anthu: awa ndi anthu amene akugwira ntchito mu bungwelo. Funsani mafunso awa:
  - a. Kodi anthuwa amagwiritsa ntchito mphatso zawo za uzimu kukwaniritsa ntchito ya utumiki?
  - b. Kodi munthu aliyense amavetsa gawo lake mu dongosolo la Mulungu?
  - c. Ngati ali ndi udindo mu bungwelo kodi amavetsa ntchito zawo ndi udindo wawo?
  - d. Kodi pali kulumikizana kwabwino pakati pa atsogoleri ndi anthu ena?
  - e. Kodi pakufunika kuonjezera ogwira ntchito ena? Ngati ndi choncho udindo wanji?
  - f. Kodi pali uballe wabwino pakati pa anthuwo ndi atsogoleri? Ngati sichoncho, mavuto ake ndi ati? Kodi pafunikira upangiri wauzimu kapena malangizo okonza mavutowo?
  - g. Kodi atsogoleri amafanana ndi zitsanzo za Mbaibulo ngati atsogoleri otumikira?
  - h. Kodi anthu opezeka mu bungwelo analandira maphunziro okwanira a utumiki umene akuchitawo. Kodi nanga angakonzekeredwe bwino bwanji?
  - i. Kodi anthuwo amachita zinthu mwandondomeko. Kodi pali ndondomeko loti akwaniritse zolinga za Mulungu. Ngati ogwira ntchito ndi ochepa, akuyenera kupanga chotheke kuti akakolole zokolola.
  - j. Mabungwe ena ali ndi zowayenereza anthu kukhala mamembala, muyeso woti anthu afikire mu utumiki. Kodi zimenezo zimachokera Mbaibulo, ndipo anthu amazitsatira?

Ndalama:

Zimatengera ndalama kuti tichite ntchito ua Mulungu. Tili ndi udindo wosamalira ndalama komanso mphatso za uzimu. Funsani mafunso awa:

- a. Kodi pali kayendetsedwe ka ndalama kolembedwa? Ndondomeko imene imaonetsa mmene mukugwiritsira ntchito ndalama zimene mumalandira. Zimenezi ndi za Mbaibulo, onani Luka 14:28-30.

- b. Kodi bungwelo limatsatira ndongosololo?
- c. Kodi bungwelo limagwiritsa ntchito bwanji ndalama zimene Mulungu wapereka? Kodi pali magawo ena amene ndalama zimaonongeka kapena kusala zimene zingapewedwe? Kodi ndalama zingagwiritsidwe ntchito bwanji bwino kuti zikwaniritse cholinga cha ufumu wa Mulungu?
- d. Kodi pamakhala malipoti a ndalama a chaka kapena mwezi onetsa mmene ndalama. Izi zimapangidwa ndalama zisanayambe kugwiritsidwa ntchito. Lipoti la ndalama zimaonetsa mmene ndalama zagwirira ntchito.
- e. Ngati bungwelo lili mu mzinda, kodi lili ndi malo osungira ndalama ku banki.
- f. Kodin alipo munthu amene anaphunzitsidwa kuti aziyang'anira za ndalama, kukonza dongosolo la kagwiritsidwe ntchito ka ndalama ndi kulemba ma lipoti?
- g. Kodi bungwelo limatsatira malamulo a boma okhudza ndalama ngati kupereka msonkho, ndi kupereka lipoti la ndalama pa chaka?
- h. Kodi bungwelo limaphwanya mfundo za Mbaibulo mmagawo a chuma?
- i. Ndi ndalama zingati zimapita ku thumba lolalikira uthenga wabwino?
- j. Kodi ndalama za bungwelo zimachokera kuti? Kodi pali malo ena amene kukhoza kuchokera ndalama?
- k. Ndi ngongole ziti zimene zikuyenera kuti zithetsedwe?

Zipangizo zina:

Izi ndi monga nyumba ndi katundu wina wa bungwelo amene amagwiritsidwa ntchito pa utumiki. Zifunzeni mafunso awa:

- a. Ndi nyumba ziti zimene zimagwiritidwa ntchito ndi bungwelo. Kodi ndi zokwanira molingana ndi dongosolo la mapulogalamun awo? Kodi nanga zingakonzedwe bwanji?
- b. Ndi nyumba ziti zimene zikufunikira mtsogolo kuti utumiki wa bungwelo upite patsogolo?
- c. Kodi pali nyumba zimene zinafikira muyeso wa boma? Ndi ziti zimene zikuyenera kukonzedwa? Pali zozimitsa moto, kapena za ngozi? Khomo losonyeza polowera kapena potulukira?
- d. Lembani mndandanda wa nyumba zimene bungwelo lili nawo. Mndandandawu umatchedwa invetale.
- e. Ndi zipangizo ziti zimene zikufunika kuti zikwaniritse ntchito ya Mulungu?
- f. Kodi pali malo osungira galimoto?

Mapulogalamu:

Izi ndi zochitika za bungwelo pofuna kuwaniritsa cholinga chake.

1. Ndi mapulogalamu ati a bungwelo amene akukwaniritsa cholinga cha bungwelo? Ndi ati satero?

2. Ndi mapulogalamu ati amene akukwaniritsa utumiki wolalikira uthenga wabwino? Ndi ati satero?
3. Ndi mapulogalamu ati amene syenera kubwerenedwanso? Ndi chiyani chikuyenera kuchitika?
4. Ndi mapulogalamu ati ayenera kuchotsedwa?
5. Ndi mapulogalamu ati amene amathandiza bungwelo kuchita bwino ndi kuwaniritsa cholinga chake?
6. Kodi pali ma pulogalamu ena amene sagwirizana ndi malemba?
7. Kodi pali mapulogalamu amene amathandiza mamembala kukula ku uzimu?

### **MAYESO ODZIFUNSA NOKHA**

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pamtima?

---

---

2. Kodi zolinga za kusanthula bungwe la chikhristu ndi chiyani?

---

---

3. Kodi kusanthula kwa bungwe kumakhudza chiyani?

---

---

4. Ngati gawo limodzi la phunziro lanu, kodi munamaliza kusanthula bungwe la chikhristu?

---

---

5. Kodi mwapanga dongosolo la zomwe mwaphunzira lothandizira kufalisa uthenga wabwino kwa anthu amitundu yonse ku dziko lapansi?

---



## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Werengani Chibvumbulutso 1:10-3:22. Machaputalawa amakamba za kusanthula kwa Mulungu kwa mipingo isanu ndi iwiri imene inali mu M'Asiya.

## CHAPUTALA CHA 11

### NDONDOMEKO ZA DONGOSOLO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kudziwa zinthu ziwiri zimene okhulupirira amakhudzira nyengo zawo za ku uzimu.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “cholinga.”
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “dongosolo.”
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “zolinga.”
- Kulemba magawo asanu a dongosolo lopambana.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika (Mateyu 5:14)**

#### MAWU OYAMBA

Maphunziro opezeka mu phunziro ili akutsogolerani mu kusanthula kwa zinthu zomwe zatizungulira. Mwaphunzira za mmene mungasanthulire anthu, magulu a anthu, madera, mitundu, zigawo ndi mabungwe. Maphunzirowa amakhazikika kuti kusanthula zinthu kokha sikokwanira. Mukuyenera kugwiritsa ntchito kusanthula kwanu ndi cholinga chofalitsa uthenga wabwino.

#### KUKHUDZA NYENGO

Monga okhulupirira, mukuyenera kukhudza nyengo ya uchimo ya dziko limene inu mukukhalamo pakukhala kuunika komkanso mchere wa dziko lapansi. Yesu anati anali kuunika kwa dziko lapansi.

**Ndadza Ine kuunika ku dziko lapansi, kuti yense wokhulupirira Ine asakhale mumdima (Yohane 12:46)**

Kodi mphamvu imene kuunika kunali kwa Yesu pa dziko lapansi. Kuunika kwake kunawalitsa njira yochoka mmoyo wamdima wa uchimo ndi kupita ku kuwala kwa ulemerero wa chipulumutso:

**Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa ciwalitsiro ca cidziwitso ca ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu (II Akorinto 4:6).**

Yesu ananena kuti okhulupirira akuyenera kukhala kuunika kwa dziko lapansi:

**Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika. Kapena sayatsa nyali, ndi kuibvundikira m'mbiya, koma aiika iyo pa coikapo cace; ndipo iunikira onse: ali m'nyumbamo. Comweco muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona nchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa Kumwamba (Mateyu 5:14-16)**

Mu dziko lathuli, kuwala kumapangitsa anthu kuona mumdima. Kumawatsogolera pamseu pamene akuyenda. Kumawapangitsa kukwaniritsa ntchito zawo. Anthu amatha kuwerenga, kuphunzira chifukwa cha kuwala.

Mu dziko la uzimu, okhulupirira akuyenera kuwaniritsa cholinga cha kuwala kwa dziko kunmene tili nako. Tikuyenera kuwala mu dziko la uchimo ndi kupangitsa anthu amene ndi otayika mu uchimo kuti awone njira ya chipulumutso kwa Yesu. Kuwala kwanu kwa uzimu kupangitse okhulupirira amene muli nawo kukwaniritsa utumiki wawo. Anthu adziwe Mulungu chifukwa cha kuwala kuli mwa inu.

Yesu ananena kuti wokhulupirira ali ngati:

**Inu ndinu mcere wa dziko lapansi; koma mcerewo ngati uka: sukuluka, adzaukoleretsa ndi ciani? Pamenepo sungakwanirenso kanthu konse, koma kuti ukaponyedwe kunjira, nupondedwe ndi anthu (Mateyu 5:13)**

Mu dziko lathuli, mchere umakometsa chakudya ndi kuchiteteza kuti chisaonongeke. Komanso umachotsa zonyasa makamaka pabala. Mu dziko la uzimu, mukuyenera kukwaniritsa cholinga cha mchere wa dziko lapansi. Mukuyenera kukometsa, kuteteza, ndi kuyeretisa nyengo ya uchimo imene ili chifupi ndi inu. Ngati simusintha malo anu, muli ngati mchere umene wasiya kukometsa ndiwo. Palibe chimene muchita.

Pogwiritsa ntchito zitsanzo za kuwala ndi mchere, Yesu ananenetsa momveka kuti wokhulupirira akuyenera kusintha malo amene amakhala mdziko lapansi. Timakhudza malo athu pobweretsera anthu ku kuwala kwa uthenga wabwino.

Baibulo ndi buku limene lili ndi nkhani za anthu a Mulungu amene anasintha malo awo ngati mchere ndi kuwala.

## **DONGOSOLO**

Dongosolo ndi njira yopangira zinthu. Ndi ndondomeko yokwaniritsa ntchito zathu.

Dongosolo la kulalikirira motsogozedwa ndi Mzimu Woyera ndi chida champhamvu. Chimasintha masomphenya kukhala zoonza zake, chokhumba choonetsera. Chimapereka mwayi kuti Mulungu atsogolere mu kuchita ulaliki kopambana. Pamene mupanga dongosolo, mumakonzekera kuchita ntchito ya Mulungu. Kupanga dongosolo kumathandiza kudziwa zosowa ndi mmene mungakwaniritsire pochita chifuniro cha Mulungu.

## **NDONDOMEKO ZA DONGOSOLO**

Mulungu ali ndi ndondomeko yofikira magulu a anthu mdzikoli. Ali ndi njira ya dera, mtundu, ndi chigawo. Ndi udindo wathu kudziwa ndi kukwaniritsa njirayo. Izi ndi zina mwa njira za dongosolo zimene zikuthandizani kukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Njira ili yonse yalongosoledwa mwamveve mu buku la Harvestime International Institute lotchedwa Dongosolo la Zolinga.

### **Gawo Loyamba: Konzeka**

Gawo loyamba lokwaniritsa cholinga chilichonse ndiko kukonzeka mwa pemphero ndi kufuna chfuniro cha Mulungu.

Mfunseni Mulungu awulure njira zake zofikira magulu a anthu, dera, mtundu ndi chigawo ndi uthenga wabwino:

### **Malongosoledwe a mtima nga munthu; Koma mayankhidwe a lilime acokera kwa Yehova (Miyambo 16:1)**

Mumakonzekanso posanthula malo amene muli. Cholinga chanu ndi dongosolo lidzapanga kusanthulaku. Mukuyenera kudziwa anthu, dera, mtundu, chigawo chimene mukutumikira. Gwiritsani ntchito luso limene mwalipeza mu phunziroli posanthula malo amene muli.

### **Gawo lachiwiri: Dziwani cholinga chanu:**

Dziwani cholinga chanu mu dongosolo la Mulungu la anthu ake. Cholinga ndi chinthu chimene mukufuna kukwaniritsa. Ndi zotsatira, cholinga cha ntchito yanu. Onaninso zotsatira za kusanthula kwa malo. Mfunseni Mulungu awulure cholinga mkati mwa dongosolo lofikira anthu ake ndi uthenga wabwino.

Dongosolo la Mulungu ndi loti anthu onse akhale amodzi mwa Yesu polandira uthenga wabwino:

### **Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, 10kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko (Aefeso 1:9-10)**

Ndi dongosolo la Mulungu kugwiritsa ntchito mpingo kuwaniritsa cholinga chake:

**kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, 11monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu (Aefeso 3:10-11)**

mpingo ndi wopangidwa ndi okhulupirira woota. Ngati mpingo ukwaniritsa cholinga chake, ndiye kuti wokhulupirira aliyense ayenera kudziwa ndi kukwaniritsa cholinga chake. Mulungu ali ndi cholinga cha wokhulupirira aliyense, njira yake ndi yofalitsa uthenga wabwino. Pamene mwadziwa cholinga chanu, mumadziwanso gawo lanu la mu dongosolo la Mulungu.

### **Gawo lachitatu: Dongosolo.**

Pamene mwadziwa gawo lanu mu cholinga cha Mulungu, mukuyenera kupanga dongosolo lakwaniritsa. Mumachita izi pokhala ndo zolinga. Zolinga ndi ndondomeko zolembedwa zimene...

- zimagwirizana ndi cholinga cha Mulungu chimene mukufuna kukwaniritsa
- mumakhala ndi chimene mufuna kuchita.
- mumadziwa amene angachite.
- mumasankha tsiku loti zinthu zichitike. Zinthu zina zikhodza kukwaniritsidwa popanda ndalama

Ndi chinthu chabwino kulemba dongosolo lanu. Cholinga chilichonse chiyenera kulembedwa mu njira yoti chikhoza kukwaniritsidwa kapena ayi.

### **Gawo lachinayi: Pitolizani.**

Baibulo limatiuza kuti chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chafuka (Yakobo 2). Kutanthauza kuti pemphero, chikhulupiriro ndi kupanga dongosolo mkopanda ntchito popanda kugwira ntchito. Kupanga dongosolo ndi ntchito yokwaniritsa cholinga, osati kungopanga dongosolo. Mukuyenera kukwaniritsa zolinga zanu. Zolinga zimayenera kunenedwa kwa anthu ena amene mugwira nawo ntchito limodzi. Anthu ayenera aphunzitsidwe ndi luso, kulimbikitsidwa ndi kukonzekera kukwaniritsa zolinga.

Ndife zipangizo za Mulungu zokwaniritsa zolinga zake:

**ndipo musapereke ziwalo zanu kuucimo, zikhale zida za cosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo ataturuka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za cilungamo (Aroma 6:13)**

Monga chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa, momwemonso dongosolo lopanda ntchito.

## **Gawo lachsanu: ungwiro**

Pamene Yesu anatuma ophunzira ake kukatumikira, anabwera ndi kupereka lipoti la zotsatira. Yesu anasanthula utumiki wawo. Kusanthula mkofunikira poona kupambana kwa utumiki. Pamene muunikira mumasanthula chithu mosamala ndi kudziwa kupambana kwake.

Pamene muonanso zolinga, mumadziwa kupambana kokwaniritsa zolinga za Mulungu. Mumaphunzira zotsatira za utumiki wanu ngati mwakwaniritsa ndondomeko zanu. Mumaonanso za mmene mwapambanira kapena kulephera. Choncho mumapanga ungwiro pa madongosolo anu. Mumapemphera mwachidwi pa zotsatira zanu za kuonanso kuti mupite chitsogolo.

Cholinga chanu nthawi zonse chidzakhala chofanana, koma madongosolo okwaniritsa zolinga zimasintha. Malo anu amasintha choncho muyenera kusinthanso ma dongosolo anu. Muthetsetso zolinga zimene sizikwaniritsa chofuna cha Mulungu ndi kupanga zolinga zina.

Cholinga chanu sichidzasintha koma mubwereza magawo anayi pa ndondomeko yanu ndi cholinga chofuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Konzekani, pangani dongosolo, kupitiliza, ndi ungwiro.

Nthawi zonse sungani cholinga chanu. Cholinga chili ngati masomphenya a uzimu. Popanda cholinga, muzalephera:

**Popanda cibvumbulutso anthu amasauka (Miyambo 29:18)**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “cholinga.”

---

---

3. Perekani tanthauzo la mawu oti “dongosolo.”

---

---

4. Perekani tanthauzo la mawu oti zolinga “zazikulu.”

---

---

5. Tchulani zitsanzo ziwiri zimene Yesu anaonetsera mmene okhulupirira angakopera anthu kumalo kumene akukhala.

---

---

6. Lembani magawo asanu a ndondomeko za dongosolo omwe mwapunzira.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Phunzirani moyo wa anthu ena amene anali atsogoleri mu Baibulo. Kodi anasinthabwanji nyengo za anthu ena?  
Mwachitsanzo, Yosefe, Mose, Estere, Danieli, Nehemiya ndi ena.

Phunziraninso moyo wa Yesu umene anakhudza nawo anthu ambiri

2. Phunzirani zambiri za Yesu ndi okhulupirira ngati kuunika kwa dziko lapansi:  
Mateyu 4:16; 5:14-16; 6:22-23  
Luka 1:79; 2:32; 8:16; 11:33; 12:35; 15:8  
Afilipi 2:5  
Yohane 1:4-9; 3:19-21; 5:35; 8:12; 9:5; 11:9-10; 12:35-46  
Aroma 13:12  
Aefeso 5:8  
I Atesalonika 5:5  
I Petro 2:9  
II Petro 1:19  
I Yohane 1:5-7; 2:8-10  
Chibvumbulutso 21:23

Dzifunseni nokha: kodi ine ndimasintha bwanji anthu a kumalo kumene ndikukhala ngati kuunika?

3. Phunzirani za okhulupirira ngati mchere wa dziko lapansi:  
Mateyu 5:13  
Marko 9:50  
Luka 14:34  
Akolose 4:6

Dzifunseni nokha: kodi ine ndimasintha bwanji anthu a kumalo kumene ndikukhala ndi ngati mchere?

4. Pitilizani ndi maphunziro anu a kukhala ndi dongosolo ndi phunziro la a Harvestime International Institute la “Dongosolo la Zolinga” limene ndi phunziro lotsiriza mu buku la “Dongosolo”



## MAYANKHO A MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA

### CHAPUTALA CHA 1:

1. Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha (Genesis 6:5).
2. Zinthu zomwe zatizungulira ndi zooneka, anthu, zikhalidwe ndi za uzimu. Komanso ndi dera limene anthu akhalako, agwira ntchito ndi kutumikira.
3. Malo oyamba a munthu anali mmunga wa Edeni. Anali malo abwino ndi angwiro.
4. Dziko limene tikukhalali ndi limene munthu anachimwa ndipo Satana akugwirabe ntchito.
5. Tchimo linapangitsa kusintha mmunda mwa Edeni.
6. Adani atatu a dziko ndi dziko, thupi ndi mdyierekezi zimene zikugwirabe ntchito.
7. Mulungu anatuma Yesu kufera zochimwa za anthu onse. Aliyense amene akhulupirira Yesu mkulapa machimo amapulumsidwa ku imfa ya uzimu.
8. Utumiki umachitika mu dziko limene ndi lochimwa. Koma pali kusiyana kwambiri kwa dzikoli. Monganso mmene anthu alili okhudzidwa ndi uchimo mosiyana molingana ndi malo amene akupezeka.

### CHAPUTALA CHA 2:

1. Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu (I Yohane 5:4)
2. Kusanthula malo ndi kuchita mwatsatane monga malo, maubale, zikhalidwe ndi zinthu za uzimu.

3. Mitundu ya kusanthula malo imene muphunzire mu phunziroli ndi monga anthu, magulu a anthu, mitundu, madera, zigawo mabungwe a chikhristu.
4. Onani zifukwa zisanu za kufunika kwa kusanthula malo mu chaputala cha 2.
5. Mavuto asanu ndi limodzi a kusanthula malo:
  - Osasanthula zinthu zooneka mmaso
  - Osaopsedwa ndi kukula kwa ntchito
  - Osakopeka ndi malipoto oyipa
  - Osakhala wamantha ndi wosakhulupirira
  - Osatenga zinthu opanda pake
  - Osakhazikika pa ngati, koma pa bwanji

### **CHAPUTALA CHA 3:**

Palibe mafunso.

### **CHAPUTALA CHA 4:**

Palibe magunso.

### **CHAPUTALA CHA 5:**

1. Dziyeseni nokha, ngati muli m'cikhulupiriro, dzitsimikizeni nokha. Kapena simuzindikira kodi za inu nokha kuti Yesu Kristu ali mwa inu? mukapanda kukhala osatsimikizidwa (II Akorinto 13:5).
2. Kusanthula munthu ndi kuphunzira nyengo za munthuyo.
3. Kusanthula munthu kumakhudza malo ake, maubale ake, zinthu zake, maphunziro, zachuma, ndi za uzimu.
4. Izi ndi cholinga cha kusanthula munthu:
  - Kudziwa moyo wauzimu
  - Kudziwa zofooka za uzimu
  - Kudziwa mphamvu za uzimu
  - Kudziwa mphatso za uzimu
  - Kudziwa malo anu mu utumiki

Kukonza dongosolo lokwaniritsa utumiki wanu

## **CHAPUTALA CHA 6:**

1. Ndipo palibe colengedwa cosaonekera pamaso pace, koma zonse zikhala za pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pace pa iye amene ticita naye (Ahebri 4:14)
2. Gulu la anthu ndi anthu amene ali pa ubale wa mu ukwati wa anthu amtundu umodzi, mbumba imodzi mdera limodzi.
3. Mumaphunzira za maubale awo, chikhalidwe ndi uzimu wawo. Komanso mumaphunzira mphamvu zakunja zimene zimakhudza kufala kwa uthenga wabwino.
4. Kusanthula gulu la anthu kumakhudza kudziwa za mmene anthu afikilidwe ndi uthenga wabwino, kodi ali ngati ndani, afikire ndani ndi njira za mmene mungawafikirire.
5. Ngati simunasanthule gulu la anthu, mukuyenera kusanthula.
6. Ngati simunapange dongosolo la lofikira anthu malingana ndi mmene mwaphunzirira, pangani chonde dongosolo.

## **CHAPUTALA CHA 7:**

1. Tauka, nuyendeyendc m'dzikoli m'litari mwace ndi m'mimba mwace; cifukwa kuti ndidzakupatsa iwe limenelo (Genesis 13:17).
2. Pachifukwa cha phunziroli, dera ndi malo a mdziko okhala ndi malire, chiyankhulo, zikhalidwe ndi ulamuliro.
3. Mumasanthula malo opezeka mdziko. Mumadziwa za malowo, zikhalidwe, zikhalidwe, ndi zinthu zina zosiyana ndi deralo. Komanso mumasanthula uzimu ndi zinthu zina za kunja kwa deralo zimene zimakhudza uthenga wabwino.
4. Kusanthula dera umadziwa gulu la anthu mdera, zimene ali nazo zofanana, mmene alili, amene angawafikira, ndi njira zowafikira ndi uthenga wabwino. Ndipo mumadziwa udingo wanu mu dongosolo la Mulungu.

5. Ngati simunasanthule dera muphunziroli, mukuyenera kusanthula.
6. Ngati simunapange dongosolo la lofikira dera malingana ndi mmene mwaphunzirira, pangani chonde dongosolo.

#### **CHAPUTALA CHA 8:**

1. Ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu (Luka 24:47)
2. Mtundu ndi anthu okhala pamodzi ndi utsogoleri umodzi. Ndi malo okhala ndi malire a dziko.
3. Pamene mukusanthula mtundu mumawona utsogoleri, malo, chiyankhulo, zikhalidwe, ndi zauzimu ndi za kunja zimene zimakhudza kufala kwa uthenga wabwino.
4. Kusanthula mtundu kumachitika ndi cholinga chodziwa gulu la anthu, limene lafikilidwa ndi uthenga wabwino. Komanso ndi zimene anthuwo ali nazo zofanana, ali ngati ndani, ndi ndani amene afikire ndi uthenga, nanga achita bwanji, ndi kudziwa udindo wanu mu dongosolo la Mulungu.
5. Ngati simunasanthule mtundu muphunziroli, mukuyenera kusanthula.
6. Ngati simunapange dongosolo la lofikira mtundu malingana ndi mmene mwaphunzirira, pangani chonde dongosolo.

#### **CHAPUTALA CHA 9:**

1. Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse (Marko 16:15)
2. Pachifukwa cha phunziroli chigawi ndi gawo la dziko lokhala ndi mitundu lopezeka kumalo kumene kuli anthu a ziyankhulo, zikhalidwe ndi zipembedzo zofanana.

3. Pamene mukusanthula chigawo, mumaona za utsogoleri, malo, chiyankhulo, zikhalidwe ndi zauzimu komanso za kunja zimene zimakhudza uthenga wabwino.
4. Kusanthula chigawo kumachitika pofuna kudziwa mtundu, zimene ali nazo zofanana, mmene alili, amene angafikire, mmene angafikilidwe. Cholinga ndiko kudziwa udindo wanu wofikira chigawocho pokonza dongosolo lofalisa uthenga wabwino.
5. Ngati simunasanthule chigawo muphunziroli, mukuyenera kusanthula.
6. Ngati simunapange dongosolo la lofikira chigawo malingana ndi mmene mwaphunzirira, pangani chonde dongosolo.

#### **CHAPUTALA CHA 10:**

1. Iye wokhala nalo khutu amve cimene Mzimu anena kwa Mipingo. (Chivumbulutso 2:29)
2. Cholinga chosanthula bungwe la chikhristu ndi:  
Kudziwa cholinga cha bungwelo, ndi ntchito yawo ya kutumikira  
Kudziwa kupambana kwa bungwelo pokwaniritsa zochita zawo.  
Kukonza dongosolo la bungwelo kuti lizichita bwino koposa.
3. Kusanthula bungwe lomwe lilipo ndi kuona zolinga, madongosolo, mphamvu, zofooka, malo, katundu ndi zochita.
4. Ngati simunasanthule bungwe la chikhristu muphunziroli, mukuyenera kusanthula.
5. Ngati simunapange dongosolo la lofikira bungwe la chikhristu malingana ndi mmene mwaphunzirira, pangani chonde dongosolo.

#### **CHAPUTALA CHA 11:**

1. Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika (Mateyu 5:14).
2. Cholinga ndi chimene mukufuna kuwaniritsa. Ndi zotsatira zotsiriza, cholinga chimene mwagwirira ntchito.

3. Dongosolo la zochita ndi njira yokwaniritsa zolinga.
4. Zolinga ndi zimene zimanena za mmene mukwaniritse zofuna zanu.
5. Kuunika ndi mchere.
6. Konzeka  
Dziwa cholinga chako  
Panga dongosolo  
Pitiliza  
Ungwiro